




MAFUNSO A ANA pA

CHIKHULUPIIRO

Abdullah bin Hamd Al-rakaf

MAFUNSO A ANA pA CHIKHULUPIIRO

Abdullah bin Hamd Al-rakaf



٢٠٢٢
(ح) جمعية الدعوة والإرشاد وتوعية الجاليات بالربوة ، ١٤٤٣ هـ

فهرسة مكتبة الملك فهد الوطنية أثناء النشر

الركف ، عبدالله حمد عبدالعزيز

أسئلة الطفل الإيمان بالغة السواحلية. / عبدالله حمد عبدالعزيز الركف؛ مركز أصول..- الرياض ،

١٤٤٣هـ

١٥٦ ص، ١٦ سم x ٢٣ سم

ردمك : ٩٧٨-٦٠٣-٨٣٥٢-٣٠-٤

١- التربية الإسلامية أ. مركز أصول (مترجم) ب. العنوان

١٤٤٣/٤٣٦٩

ديوي ٣٧٧،١

رقم الايداع: ١٤٤٣/٤٣٦٩

ردمك : ٩٧٨-٦٠٣-٨٣٥٢-٣٠-٤



This book has been conceived, prepared and designed by the Osoul Centre. All photos used in the book belong to the Osoul Centre. The Centre hereby permits all Sunni Muslims to reprint and publish the book in any method and format on condition that 1) acknowledgement of the Osoul Centre is clearly stated on all editions; and 2) no alteration or amendment of the text is introduced without reference to the Osoul Centre. In the case of reprinting this book, the Centre strongly recommends maintaining high quality.

+966 11 445 4900

+966 11 497 0126

P.O.BOX 29465 Riyadh 11457

www.osoulcenter.com

ISBN 978-603-8352-30-4

L.D. No.: 1443 / 4369

Première Édition. 2022

بِسْمِ اللَّهِ الرَّحْمَنِ الرَّحِيمِ

Bismilillahirrahmanirrahim



MAU OYAMBA 4

Ndithu kutamandidwa konse ndi kwa Allah bwana wazolengwedwa zonse, ndipo madalitso ndi mtendere zipite kwa wolemekezeka wa aneneri onse wa pamwamba ndi wopambana wa atumiki onse, mneneri wathu Muhammad, ndi omutsatira onse.

Pambuyo pa kutero:-

Nditthu zaka zoyambilira za umwana zili ndi ubwino wa ukulu pokonza m'mene mwana azionera chilengedwe, chifukwa chithunzi thunzi chomwe chimadzalidwa mu nzeru za mwana mu nyengo imeneyi, chimatengedwa ngati mwala wa maziko womwe umakonza umunthu wa mwanayo kumbali zake zonse (zosiyana siyana) ndipo umafunikira (mwawo) kuti uziyendera limodzi ndi zofunikira za mwanayo zokhudza umoyo, chikhalidwe ndi chipembedzo, zomwe zingamuthandize mwanayo kuti ayambe mwa mphamvu ulendo wake wolowa mu zipsinjo ndi mikwingwirima ya umoyo (mavuto) ndi kudutsamo molongosoka ali munthu waphindu komanso wothandiza kudzera mu zimene akumazimva ndi kuziona, amakon-zanso chitsanzo chake chake chadzikoli, kotsala kwa moyo wakeko pambuyo pa zimenezi kumangokhala kukonza kapena kupititsa pat-sogolo chithunzi thunzi chake choyambilira chiya potengera nyengo zimene akudutsana nazo.

Mu nyengo imeneyi mwana amadalira makolo ake ngati njira yodzizira zinthu, chifukwa kulongosoka kwa ana kumachokera mu kulongosoka kwa chikhalidwe cha makolo, iwo ndi amene ali ndi udindo wophunzitsa ana awo. Pa chifukwa chimenechi, adalankhula mtumiki (saw) kunena kuti **“aliyense mwa inu ndi muyang'aniri ndipo aliyense mwa inu ali ndi udindo pa chomwe akuyang'anira”**(muslim). Moti chilamulo chimenechi chikukakamiza kuyikira mtima ndi kulimbikira pa maphunziro ndi kuphunzitsa.

Poona kuti ife tili mu nyengo yomwe yadzadzana ndi zilako lako ndi zisokonezo: kunali kofunikira kwambiri kuti makolo alimbikire kuphunzitsa ana (kulimbikira kwake) kodzadzidwa ndi chilungamo, chidwi komanso kupereka mpata wokwanira (kwa ophunzirawo),

chifukwa kutheka njere imene makolo angayidzale mmitima ya ana itha kubala ntchito yopitilira kwa makolo akadzachoka moyo uno (akadzamwalira), nakhala mwana uja ntchito yopitilira ya makolo pambuyo pa ifa ya makolowo (sadaqah jaariyah), ngati m'mene adanenera mtumiki (saw) - pamene amatchula zinthu zomwe zimakhala zikumuthandizabe munthu ngakhale atamwalira - kunena kuti **"kapena mwana wabwino yemwe amawapemphera zabwino makolo ake"**. (Muslim)

Ana ndi chithu chimodzi mwazithu zomwe Allah anawalangiza makolo (kuti achisamalire), ngati m'mene Allah akunenera mu buku lolemekezeka la Quru'an kuti: **"Mulungu akukulangizani zokhudza ana anu"** (sura 4 :11)

kutanthauza kuti ndithu ana anu (inu makolo) painu ndi chosungitsidwa, ndipo Allah wakulangizani za iwo kuti muwasamalire chipembedzo chawo ndi dziko lawo, ndipo mudziwaphunzitsa ndi kuwalangiza ndi kuwaletsa zoipa ndi kuwalamulira kuti azimumvera Allah ndi kusamala malamulo ake nthawi zonse, ngati m'mene akunenera Allah mu quruan yolemekezeka kunena kuti **"E, inu amene mwakhulupilira! dzitchinjirizeni nokha ndi mawanja anu ku moto..."** (sura 28:6).

Allah anawalangiza makolo za ana awo, zili ndi iwo kugwiritsa ntchito langizolo ndi kukapeza Jannah kapena kuliononga ndi kupeza chilango, zimenezi zikusonyeza kuti Allah ndi wachisoni kwambiri kuposa makolo awiri; moti anawalangiza makolo awiri zoyang'anira ana awo mwa ubwino kumachita kuti makolo amakhala achisoni nkale kwa ana awo ⁽¹⁾.

Choncho, kuphunzitsa mwana m'banja kukakhala kuti kwachitika mwa ubwino, mwana ameneyo amadzakhala wa chitsanzo cha pamwamba. Ndipo kusowekera kulikonse kwa maphunziro ndi maleledwe a chikhulupiro cholongosoka mwa mwana m'banjamo, kudzatulutsa mwana wosowa khalidwe labwino ⁽²⁾.

Sikuti maphunziro ndiye kungokonza zolakwika zokha ayi, koma kuphunzitsa ndi kupereka maziko a chipembezo ndi malamulo a chisilam ndi kugwiritsa ntchito njira zosiyana siyana monga kukhazikitsa zithuzi thuzi (za zomwe ukumuphunzitsa) ndi kuzipangitsa zimenezo kuti zikhazikike mmitima mwawo – monga kuphunzitsa kudzera mukuonera kwa ena, ulaliki, nkhani, zochitika, ndi zina zotero ⁽³⁾; ncholinga choti titulutse munthu wolongosoka komanso waphindu pa umoyo komanso pa mudzi (pa malo).

Bukuli lagawidwa m'magawo awiri : **gawo loyamba** (zokhudza maphunziro a chikhulupiliro), m'menemo muli maziko ambiri omwe an-gathandize makolo kuphunzitsa ana awo – mu chifuniro cha Allah -, pomwe gawo la chiwiri likuzungulira pa (zitsanzo zochitika pakayankhid-we ka mafunso a ana okhudza chikhululupiliro) m'menemo tiyankhamo mafunso amene ali otchuka kwambiri pakati pa ana amisinkhu yosiya-na siyana, makamaka omwe akukhudzana ndi msichi zachikhulupiliro zisanu ndi imodzi (6) ndipo tafotokozamo momveka bwino m'mene tin-gayankhire mafunso ngati amenewa.

Ndithu Allah ndi mwini kuthekera, komanso muwongoli ku njira ya chiongoko.

Abdullah bin Hamd Alrakaf

DAFTAR ISI

10

ZOKHUDZA
MAPHUNZIRO
A za
CHIKHULUPILIRO



MAPHUNZIRO A ZA
CHIKHULUPILIRO
A ANA

26

52

NSANAMIRA
ZA MAPHUNZIRO
Aza
CHIKHULUPILIRO





CHIYAMBI CHA

**KAYANKHIDWE
KAMAFUNSO**

78

98

ZITSANZO
ZA MMENE
TINGAYANKHIRE
**MAFUNSO A
ANA OKHUDZA
CHIKHULUPIIRO**



ZOKHUDZA MAPHUNZIRO A za CHIKHULUPILIRO





Ndithu

Ndithu maphunziro ndi chimozi mwazinthu zofunikira kwambiri pokhonza munthu, ndipo ndi chipangizo chokonzero mwana ndi kumpatsira maziko ambali zonse za umoyo wake, kudzero mmaphunziro tingathe kukonza umunthu wa mwana pa kakhalidwe kake ndi anthu a mudzi wake, pa maphunziro ake, pa nzeru zake, pa umoyo wake ndi zina zotero, ndiye tisanakambe za maphunziro achikhulupiliro ndi kufotokoza za kufunika kwake, ndi bwino titadziwa tanthaunzo la maphunziro, kuti amatanthauza chiyani komanso kuti anthu a za maphunziro amafuna chiyani paliwuli?!

TANTHAUZO LA MAPHUNZIRO



Maphunziro ndi ntchito yokhala ndi cholinga komanso yonkera nkera mt-sogolo (yopitirira) imene imayendet-sedwa ndi malamulo, ndi cholinga chofuna kukonza zikhalidwe za bwino kudzera mukulangiza, kuongolera, kuphunzitsa, kukonza ndi kuyetsetsa kupanga zomwe waphunzirazo. Maphunziro amagwira ntchito ya kusamalira ndikuyang'anira chibadwa cha mwana, ndi kupititsa pa tsogolo ma-

luso ndi zikonzekero za mwanayo, ndi kupangitsa kuti chibadwa chakechi ndi maluso ake aja zikhale zabwino ndi zolongosoka komanso zokwanira ndizoyenera, zomwe zimathandiza kukonza munthu wabwino yemwe angayang'anire dziko la pansi, ndipo maphunziro ndi chida chimene chimapanga utsogoleri mbali zonse za moyo⁽⁴⁾.

KUFUNIKA KWA MAPHUNZIRO A zaCHIKHULUPIIRO



Ndithu chikhulupiliro ndiye cholinga chachikulu chakupezeka chilengedwe ndi munthu, ndipo pa chikhulupiliro ndi pamene pasiyanirana njira paulendo wathu wa dziko la pansi, Allah akulankhula mu Quru'an yolemekezeka kunena kuti **“choncho mwaiwo alipo amene adakhulupilira ndipo ena mwaiwo sadakhulupilire”**. (Surat Al Baqarah: 253).

Pachikhulupiliro ndi pamene pagona zichito chito za anthu komanso ndi chimene chimasiyanitsa kumalo okafikira mu umoyo womwe uli nkudza⁽⁵⁾, nthawi ya umwana ndi nthawi imene mwana amatha kusiyanitsa zinthu, chifukwa zimene zimadzalidwa mu nzeru za mwana pa msinkhu umenewu monga: zikhulupiliro, zokonda, zikhalidwe ndi malangizo, zimakhala zovuta kusintha nanji nanji kuchotsera, mwinanso chipsera chake chimatsaliranso pa munthuyo moyo wakewonse⁽⁶⁾, pachifukwa chimenechi maphunziro azachikhulupiliro amene amatengedwa iye ali mwana wa mng'ono ndiwo maziko omwe amamanga moyo wa munthu padziko pano.

Ndithu maphunziro kunena mosakuluwika ndikuyikira mtima, popanda kuyikira mtima palibe maphunziro, choyenera kuyikira mtima kwambiri pa maphunziro ndiye kudzala chikhulupiliro, ife tili munyengo yomwe chidwi cha anthu ofufuza za maphunziro chakhamukira kumaphunziro kumbali ya nzeru ndi thupi, ndipo anthu ambiri sakulabadira zamaphunziro ambali ya chikhulupiliro, kafukufuku wawo amalunjika ku zakupambana pa dziko lapansi poona zinthu zooneka ndi maso, popanda kuyikira mtima ndi kukonza zinthu zoti zikamuthandize komanso akasangalare ku umoyo umene uli mkudza, zimene zimapangitsa kuti kuona kwathu pa maphunziro kukhale kosiyana kwambiri ndi iwowo kumabali imeneyi⁽⁷⁾.

Zachidziwikireni kuti maphunziro achikhulupiliro pa chisilamu ndi imodzi mwananamira imene inamanga maphunziro munyengo ya mtumiki yoyera, monga mmene tikumvera nkhani kuchokera kwa mwana wa Umaru (r.a) iye adati ndinamumva mtumiki (saw) akunena kuti: **“wina aliyense mwa inu ndi muyang’ayan-iri, ndipo aliyense wainu ali ndi udindo pa chimene akuyang’aniracho, mtsogoleri ndi muyang’aniri ndipo ali ndi udindo pa zimene akuyang’anirazo, nayeso mzimayi ndi muyang’aniri wa nyumba ya mwamuna wake ndipo ali ndi udindo pa zimene akuyang’anirazo”**⁽⁸⁾.



Apa mtumiki akufotokoza zakuku-
la kwa udindo womwe aliyense mwa
ife wasenza, ndipo udindo ume-
newu - palibe kuchitira mwina – ndi
wokhudzana kuti wapanga chani kwa
anthu amene ali pansi pako? Palinso
mau ena amene mtumiki (saw) anane-
na kuti: **“Kapolo wina aliyense yem-
we mulungu wampatsa owayang’nira
ndiye sanawasamalire moyenera,
sakalinunkha fungo la ku Jannah”**
(Bukhar -7150),

Apa zikuonetsa kufunikira kop-
ereka malangizo mwachilungamo
ndi mokhulupilika koteru pafunika
langizo lizikhala losayang’ana mbali
ndi lokomera olangizidwayo kumbali
zonse, mwankhani zina zimene zina-
bwera pa mutuwa ndi mau amwana
wa umaru (r.a) onena kuti: “Umu-
phunzitse chikhalidwe mwana wako
chifukwa ndi udindo wako pa iyeyo
kuti unamuphunzitsa khalidwe lanji?
Komanso wamuphunzitsa chiyani?
Nayenso ali ndi udindo wokuchitirani
inuyo ubwino ndi kukumverani mala-
mulo anu”⁽⁹⁾.

Apa mwana wa Umaru akutsindi-
ka kuti udindo umenewu poyamba
umakhala pa makolo, chifukwa iwowo
ndigwero limene ana amapezera ma-
phunziro ndi chikhalidwe, ndipo mu
hadith ina ananena kuti maphunziro
ndi abwino kuposa kupereka chaulele,
chifukwa zanenedwa kuti **“munthuku-
phunzitsa mwana wako chikhalidwe
ndi kwabwino kuposa kupereka cha
ulere cholemera ma kilogalamu awiri
ndi theka(2.5kg) azakudya”⁽¹⁰⁾.**

Komanso pali hadith ina yomwe
imati: **“kuphunzitsa mwana chikhal-
idwe chabwino ndi kwa bwino kupo-
sa kupereka china chilichonse mwa
ulere”, inaso ikuti: “kholo silingath-
andize mwana wake ndi chinthu cha
pamwamba kwambiri choposa kumu-
phunzitsa chikhalidwe chabwino”⁽¹¹⁾.**

Maumboni onsewa ndi ena otero
akusonyeza kuti kuikira mtima pa ku-
phunzira ndi kuphunzitsa ndi chimod-
zi mwazinthu zikulu zikulu zofunikira
zomwe makolo angapereke Kwa ana
awo.




Ndiye kale ana timawalera munjira yotsekeka mbali ina, koma lero tiku-mawalera kumachita kuti makomo ndi mazenera anyumba zathu ali otsekukira kudziko lapansi kuchokera ku mapeto adziko mpaka kumapeto, zimenezi mwa-chikhalire zimakhala ndi ubwino ndi kuyipa, moti tikapanda kuchenjera ndikuz-imvetsa bwino zimene zikuyendazo, ndiye kuti zoipazo zitha kuononga zabwi-nozo, tingathe kumvetsa zizindikiro za kusintha kwa makono ngati tikhala ndi chidwi pa kusinthasintha kwachangu komwe kukuchitika panopa ndi kukuw-erenga bwino (kusinthako) pogwiritsa ntchito maphunziro, zimenezi zimapangit-sa iye uja kuti adzadzitse matanthaunzo achikhulupiliro m'mitima ya ana kudzera mu umoyo wapa banja womwe banja lonse limafuna, komanso kudzera muku-wasakira ana masewero ndi masukulu omwe amayikira chidwi pa zimenezi, kusazimvetsa zomwe zikuyenda zimapangitsa kuti uluze kuluza kwake kokanika nako kubwezeretsa⁽¹²⁾.

Koma kudzera mmaphunziro opitilira, ndi (kudzera mu) kupilira kosalekeza; ti-tha kupeza zotsatira zapamwamba zambiri - muchifuniro cha Allah-. Pamaphun-ziro sizimakwanira kulangiza ndi kusiyira pompo ayi, koma zimafunika kutsatira ndi kulangiza mosalekeza⁽¹³⁾.



MAPHUNZIRO A ZACHIKHULUPILIRO ngoFUNIKA zedi



Anthu am'bado uno amafuna kutchuka iwo eni ndi kutchukitsa chikhali-dwe chawo (culture) ndi kukhala ndi chili chonse, koma zomusokoneza zomwe zamuzungulira mbali zake zonse ndi zoopsa kwambiri komanso ndizoyenera kuzilingalira, ndipo ife timagwira ntchito yovuta kwambiri pa anthu, ntchito yake ndiya maphunziro⁽¹⁴⁾.

Zina mwa zimene zikusonyeza kufunika kwa maphunziro achikhulupiliro kwa ana ndi kusowekera kwa maphunziro amenewa kwa anthu: ndi kuti kuonetsetsa chidwi pophunzitsa anthu maphunziro achikhulupiliro ndi kuwayitanira kuchimenecho makamaka ana ndiwo mchitidwe wa atumiki _ madalitso ndi mtendere zikhale pa iwo— ndi anthu olungama omwe anabwera pam-buyo pa iwo, zina mwaizo ndi mawu

amene akulankhula Allah zokhudza Nowa (Nuhu) (madalitso ndi mtendere zikhale pa iye) m'mene amaitanira mwana wake ndi kumuchenjeza zoyenda ndi anthu osochera Allah akunena kuti Nowa adati kwa mwana wake: **"Mwana wanga! Kwerera pamodzi ndi ife usakhale pamodzi ndi osakhulupilira"** (surat Hud :42)

Komanso Allah akulankhula zokhudza Ibrahim pa nthawi imene amawalangiza ana ake, Allah akunena kuti: **"Ndipo Ibrahim adalangizanso ana ake za zimenezi chonchonso Yakubu (adalangiza ana ake kuti) E. inu ana anga! Ndithu mulungu wakusankhirani chipembedzo (cha chisilamu) choncho musafe pokha pokha muli asilamu (ogonjera iye)"** (Surat baqarah: 132),

Komanso langizo loyamba la Luqman pamwana wake anamuchenjeza za shirik ndipo Allah akunena kuti **“Ndipo (akumbutse) pamene Luqman adauza mwana wake akumulangiza Ee! iwe mwana wanga! Usaphatikize Mulungu ndi mafano. Ndithu, kumuphatikiza (Mulungu) ndi zinthu zina ndi kuipitsa kwakukulu”** (Surat Luqman: 13).

Nayeso mtumiki Muhammad (saw) analangiza mwana wa Abbas (r.a) kunena kuti **“oh! mwana iwe, ndikufuna ndikuphunzitse mau awa: Samala malamulo amulungu ndipo iye adzakusamala, umusunge Mulungu ndipo iye udzamupeza patsogolo pako, ukafuna kupempha uzipempha Mulungu, ukafuna thandizo uzimupempha Mulungu”** (Tirmizi -2516). Mulangizo limeneli muli kuonetsa chidwi pamaphunziro azachikhulupiliro.

Mwazinanso zimene zikusonyeza kufunikira kwa maphunziro ndi: podziwa kuti kuphunzitsa chikhulupiliro ndiye phata la maphunziro onse, ndiye mwana akaphunzira maphunziro achikhulupiliro nadzalidwa mu mtima mwakemo mogwirizana ndi ndondomeko ya atumiki, ndiye kuti mapemphero ena onse ndi nthambi zina za chipembedzo zimatsatira pambuyo pake, ndipo kuikira chidwi ndi chifukwa chimodzi chopezera chiongoko – muchifuniro cha Mulungu -, chifukwa malamulo ambiri amangidwa (amayenda) ndi chikhulupiliro mwa Allah ndi tsiku lomaliza, ndiye chikhulupiliro chikakhala ndi mphamvu, chimamuletsa munthu uja njira yoletsedwa.

Chinanso chimene chikuonetsa kufunikira kwa maphunziro: ndikusalabadira komwe tikukuona mwa makolo ena posaphunzitsa ana awo zokhudza chikhulupiliro pogwiritsa umboni wonena kuti akadali achichepere, ngakhale akamakula samathanso kuwaphunzitsa. Yemwe angazengereze zophunzitsa mwana wake zinthu zomwe zingamuthandize namutayilira ndiye kuti wapanga chinthu choipitsitsa. Ana ambiri kusokonezeka kwao kumachokera kwa makolo awo ndi kusalabadira kwawo (makolo) posawaphunzitsa zinthu zimene zili zokakamizika pa chipembedzo ndi zichito chito zamtumiki (Sunnah), ndipo amawaononga ali aang’ono moti anawo amakhala kuti sanapindule ndipo sangathandize makolo awo ku ukulu⁽¹⁵⁾.

Chinanso ndi kuchuluka kwa mapologaramu okhudza ana mu njira ya mauthenga (monga: zoonerera, zomverera ndi zowerengedwa), zomwe zimafalitsa kwambiri zithunzithunzi ndi matanthaunzo osokoneza mmitima ya ana, ndiye pakufunikira kwambiri kuti papezeke maphunziro azachikhulupiliro omwe angalimbane ndi mauthenga amenewa, ndiye maphunziro adza chikhulupiliro amagwiritsa ntchito zipangizo zimene zili zovomerezeka mchipembedzo, ndipo zimateteza mwana mokwanira ku mavuto onse apa maphunziro asanachitike, komanso amathandiza kuwachiza mavutowo akachitika, izi ndizofunikira kwambiri kuti makolo awachitire ana awo komanso zimabweretsa chisangalalo padziko lapansi pano, komanso ndi kukapeza chipulumutso pa umoyo umene uli nkudza - muchifuniro cha Mulungu-, ndipo icho ndi chifukwa chomwe chidzasiyanitse anthu tsiku la chiweruzo⁽¹⁶⁾.

Chomaliza maphunziro a zachikhulupiliro amabweretsa kukhazikika ndi mten-

ZOLINGAZA MAPHUNZIRO Aza CHIKHULUPILIRO



Ndithu cholinga chachikulu chamaphunziro ndiko kukwanilitsa ukapolo weni weni pa Mulungu, choncho cholinga chimenechi chimafuna kukwanilitsa zolinga zina zing'ono zing'ono zochuluka, zina mwaizo:

Choyamba: kukhazikitsa chikhulupiliro cholondola pa ana a dera la chisilam; pofuna kukhonza munthu wolungama yemwe azipembedza Mulungu wa pamwamba movomereza ndi mozindikira.

Chachiwiri: kuti munthu akhale m’dera la chisilam ndi chikhalidwe chabwino motsatira makhalidwe amtumiki (saw) yemwe Mulungu anamuyikira umboni ponena kuti **“Ndipo ndithu uli nawo (iwe Muhammad) makhalidwe abwino kwambiri”** (Surat Qalam: 4), komanso pogwiritsa ntchito mawu amtumiki onena kuti: **“Ndithu ndinatimizidwa padzikoli kudzakwanilitsa makhalidwe abwino”**⁽¹⁸⁾.

Chachitatu: kukhazikitsa umodzi pakati pa asilamu; chifukwa munthu uja amadzimva kuti iye ndi mmodzi mwa anthu adelaro ndiye kuti amalumikizana ndi azinzake pogwiritsa ntchito mau a Mulungu onena kuti: **“Ndithu, okhulupilira onse ndi pachibale choncho yanjani sani pakati pa abale anu ndipo muopeni Mulungu kuti akuchitireni chifundo”** (Surat Al-hujurat: 10), ndi mawu ochokera kwa mtumiki onena kuti: **“wokhulupilira pa wokhulupilira nzake ali ngati nyumba yomwe chipupa china chimalimba kamba ka chipupa chinzake”** (Bukhar -6026), komanso anati: **“mupeza anthu okhulupilira pakumverana chisoni kwao, ndi pa chifundo chawo, ndikukondana kwao ndi kufewerana kwa mitima yawo, alingati thupi limodzi, ngati chiwalo chimodzi chitadwala thupi lake lonse limathandizira kucheza ndi kunjenjemera”** (Bukhar -6011). Kudzera muzimenezi ubale wa chikhulupiliro umamangika pakati pa asilamu.

Chachinayi: kukhonzha munthu wolongosoka m’maganizo ndi mumtima momwe, zimenezi zimathandiza kukhonzha munthu waphindu mudera la asilamu. Yemwe angakwanitse kugwiritsa ntchito maudindo ake pakutukula ndi kupititsa patsogolo zabwino za dzikoli, ndikugwirantchito yolemetsa ndi yofunikira ya utsogoleri yomwe Allah anamuyikira munthu (Adam) padzikoli⁽¹⁹⁾.

Kuchokera pa zimenezi; pakuonekera kufunikira koyamba kwa maphunziro achikhulupiliro – cheni cheni -, omwe amagwira ntchito popereka mphamvu za uzimu, ndikulimbitsa chitetezo cha thupi ndikuyika uzimu muzolankhula ndi zichitochito zawo ndiye kuchokera pazimenezi zimakhala zophweka kwa munthu kugwira ntchito zofunikira pofuna kukwaniritsa zolinga za maphunziro akuzindikira wamba (theory) ndi a zichitochito (practical)⁽²⁰⁾.

Maziko A MAPHUNZIRO



Pali ngodya zomwe zimayezamilidwa pomanga maphunziro, zomwe tingathe kuzisonkhanitsa mungodya ziwiri zikulu zikulu, yoyamba: ngodya yakuzindikira wamba (theory), ndipo yachiwiri ndi ngodya ya ntchito (practical).


Ngodya ya kuzindikira imeneyi itha kugawidwanso pawiri:

- 1- Maphunziro
- 2- Chikhulupiliro

Gawoloyamba: Maphunziro: gawo ili limatengedwa ngati kiya wamkulu kwambri yomvetsetsera zinthu komanso ndikumangira ndi kutetezera chikhalidwe, ndipo Allah akunena kuti **“Nena (kwa iwo iwe mtumiki) “kodi amene akudziwa ndi amene sakudziwa ngofanana”?** (Surat Azumar: 9).

Ndithu mtumiki (saw) anayetsetsa kuphunzitsa ophunzira ake maphunziro aphindu, komanso anawaphunzitsa kuti azimupempha Allah kuti awateteze kuchokera kumaphunziro opanda phindu, moti anati muduwa (pempho) yomwe amawaphunzitsa maswaha bawo: **“O! Allah ine ndikuzitchinjiriza ndi kupempha chitetezo mwainu kuchokera kumaphunziro opanda phindu ndi mtima wosaopa Allah.** (Muslim – 2722).

Gawolachiwiri: Chikhulupiliro: ichi ndi chomwe chimakhazikika m’mitima ya ana monga kukhulupilira nsanamira zisanu ndi imodzi za chikhulupiliro, limenelo ndi tanthaunzo losonkhanitsa zomwe zili mu umoyo uno ndi umoyo womwe uli nkudza. Ndipo mtumiki (saw) anaonetsa chidwi pofuna kudza chikhulupiliro cholongosoka m’mitima ya ummah (anthu) wake.



Pomwe ngodya ya ntchito (practical) itha kugawikana patatu

1- Kupembedza. 2- Kukwanilitsa (ntchito). 3- Chikhalidwe.

Gawo loyamba: kupembedza⁽²¹⁾, maphunziro aphindu amafunika azimukhonza munthu pachikhulupilro chabwino komanso azimupatsa mbiri zapamwamba, zomwe zingamange umunthu wa ana ndicholinga choti akhale woyera mtima ndi wolumikizana kwambiri ndi Mulungu wake, nakhala wachikhalidwe ndi maganizo olungama, ndikukhala zolingalira zake zolongosoka, pachifukwa chimenechi mtumiki (saw) anamuza Muadhi bun Jabal kuti ndikulumbira mwa Allah kuti ine ndimakukonda, ndiye usamasiye pambuyo pa swala ili yonse kunena mau oti **“O, Allah ndithandizeni ine kuti ndizikumbukira ni pafupipafupi ndikukuyamikani ndikukupembedzanimoyenerera”**(Abu Daudu – 1522).

Apa mtumiki anamuphunzitsa iye kuti kupembedza ndi mphatso ya pamwamba yochokera kwa Mulungu, osati chifukwa cha kulimbikira kwa munthu kokha ayi, koma chifukwa cha kuthekera kwa Allah (taufiq), komanso anamuphunzitsa kuti mapemphero amafuna nthawi zonse chithandizo chochokera kwa Mulungu, ndiye zikhazikike mu mtima mwakemo kuti munthu wokhulupilira akukakamizidwa kuti akamamupembedza mbuye wake azimupempha thandizo ndikumuyezamira iye, chifukwa iye Mulungu ndi amene amapereka kuthekera komumvera malamulo ake.

Gawolachiwiri: Nchito (practical): palibe maphunziro ngati sakutsatilidwa, ndiye ntchito ndi chida chomwe chikawapambanitse anthu ena ku umoyo umene uli mkudza, Allah akunene kuti **“Choncho, amene angachite chabwino cholemera ngati kanjere kakang’ono, adzaona malipiro ake. Ndipo amene angachite choipa cholemera ngati kanjere kakang’ono, adzaona malipiro ake (Mulungu sachitira chinyengo aliyense).** (Surat az zalalah: 7-8).

Gawolachitatu: Makhalidwe: ndondomeko yachisilamu imakonzana munthu kakhala ndi khalidwe labwino, mpakana mtumiki mwini wake amaona kuti uthenga wake wonse ukuzungulira pa tanthaunzo limodzi lomwe ndi khalidwe labwino, ndikuphunzitsa khalidwelo, ndipo anati: **“Ndithudi ndinatimizidwa kudzakwanilitsa makhalidwe abwino”** (Ahmad – 8939), ndipo analimbikitsa za makhalidwe abwino m’mau ake onena kuti: **“Ndithu okonedwa kwambiri mwainu kwaine komanso wachifupi kwambiri mwa inu kwaine tsiku lachiweruzo; ndi okhawa amene ali ndi makhalidwe abwino”** (Tirmizi – 2018), choncho kukhala ndi makhalidwe abwino ndilo phindu la maphunziro a zachikhulupilro loonekera ndi zotsatira za maphunziro a za chikhulupilro

ZITSANZO ZOCHITIKA ZOPHUNZITSA (PRACTICAL)



Ndithu kupereka zitsanzo za ntchito (practical) ndi chimodzi mwazithu zomwe zimathandiza kulimbitsa maziko ndi zikhulupiriro, ndiye pano tibweretsa mwachidule zambiri mwa-zitsanzo zomwe zimagotokoza m'mene chiphunzitso cha mtumiki chinalili ndi ophunzira ake pomanga chikhulupiriro pa ana⁽²⁴⁾.

1. Nkhani inachokera kwa mwana wa Abbas (r.a) iye adati: **Anali mtumiki akuwapemphera chitetezo Hassan ndi Hussein ndipo amana kuti ndithu bambo anu (Ibrahim) anali kuwapemphera chitetezo Ismaila ndi Ishaaq kwa Mulungu ndi mau awa: Ndiku-pempha chitetezo kudzeram-mau a Allah omwe ali okwanira kuti asandifikire satana aliyense ndizoipa zina zilizonse komanso kuti lisandifikire diso lamatsoka (Bukhar – 3371).**



2. Adanenanso Abu Huraira (r.a) kuti iye adamumva mtumiki (saw) akunena kuti:

“Mwana wina aliyense amabadwa ali ndi chikhulupiliro choti Mulungu ndi modzi, koma makolo ake ndi amene amapangitsa kuti (mwanayo) akhale muyuda, mkirisitu kapena wopembedza moto (mafano)” (Bukhar – 1358).



3. Ndipo Umaru mwana wa Abi Salama akunena kuti: tsiku lina ndili mwana mnyumba ya mtumiki (saw), unali mkono wanga ukuyendayenda paliponse mumbale ya chakudya ndiye mtumiki anandiuza kuti: **“Ee! mwana iwe, umutchule kaye Allah, ndipo uzidya dzanja lako lakumanja ndipo uzidya mbali yako”.**(Bukhar – 5376, Muslim – 2022)

4. Mwana wa Abbas(r.a) ananenanso kuti: tsiku lina ndinali pambuyo pa mtumiki (saw) ndiye mtumiki anandiuza kuti: **“E, mwana iwe, ine ndikuphunzitsa mawu awa: Umusunge Mulungu ndipo iye adzakusunga, umusunge Allah ndipo udzamupeza patsogolo pako, ukafuna kupempha uzimupempha Allah, ukafuna kupempha chithandizo uzimupemphanso Allah, dziwa kuti anthu onse atati asonkhane kuti akuthandize china chake sangakwanitse kupatula pachimene Allah anakulemba”.**(Tirmiz – 2516).

5. Ndipo Hassan mwana wa Allie (r.a) anati: anandiphunzitsa mthenga wa Allah mau oti ndiziwalankhula mu dua ya qunoot ya witri) kuti ndiziti: **“O Allah ndiongoneni ine muniyike mgulu la anthu omwe mudawaongola, nditetezeni kuzoipa pondiyika**

mugulu la amene munawateteza, ndiyang'anireni muniyike mugulu la amene mumawayang'anira, ndidalitseni pa zimene mumandipatsa, ndipo nditchingireni zoipa zimene munazikonza kuti zindipeze, ndithu inu ndi amene mumayika zikonzero pa ife ndipo palibe amene angatero pa inu, ndithu sanganyozeke yemwe mwamuyang'anira inu (Allah), ndipo sangalemekezeke yemwe mwadana naye, mwayeretseka inu mbuye wathu Allah komanso ndinu wapamwambamwamba" (Abu Daudu – 1425).

6. Anasi mwana wa Malick adati: mtumiki wa Allah adandiuza kuti **"Ee! mwana wanga, ukamalowa mnyumba muli mkazi wako; uzipereka salaam, zikubweretsera madalitso iweyo ndi apa banja lako"** (Tirmizi – 2698).
7. Jumdubi wa fuko la bujari (r.a) adati: **Tidali ndi mtumiki (saw) tili anyamata achisodzera, tidaphunzira chikhulupiliro tisanaphunzire Quru'an, tita-phunzira Quru'an tidaonjezereka nayo chikhulupiliro"** (Ibun Majah-61).
8. Mayi ake a Suleymu Arraymiswaau mayi ake a Anasi bun Malik (r.a) analowa chisilamu mayi amenewa Anasi ali mwana wang'ono, asanasiye kuyamwa, koma mzimayi ameneyu ankamuphunzitsa Anasiyu kuti anene mau awa : **"palibe wina wopembedzedwa mwachoonadi koma Allah yekha"** komanso amamuuza kuti anene kuti: **"ndikuchitira umboni kuti Muhammad ndi mthenga wa Allah"**, ndipo Anasi amanena zimenezi⁽²²⁾.
9. Ndipo Ibrahim wafuko la taymu (r.a) anati: ophunzira amtumiki (maswaha-ba) **"ankaona kuti ndibwino kuti mwana akangoyamba kulankhula amuphunzitse liwu loti (Laa ilaahailallah), kutanthauza kuti (palibe winawom-upembedza mwachoonadi koma Allah yekha) kasanu ndi kawiri -, ncholinga choti zimenezo zikhale zoyambirira kuziyankhula mwanayo"**⁽²³⁾.



MAPHUNZIRO A ZA CHIKHULUPILIRO A ANA





Maphunziro

Maphunziro azachikhulupiliro pa ana ndi umodzi mwamitu yofunikira kwambiri pamaphunziro potengera zimene zikuphezeka mkati mwa maphunziro, chifukwa ndi umene umakhazikitsa makhalidwe abwino, ndi chikhulupiliro chabwino kuchokera mkati mweni mweni mwanzeru ndi mumtima, komanso zimathandizira kukuongolera kuzikhalidwe zapamwamba ndikuzipangitsa kuti zikhalidwe zimenezo zigwire ntchito pa zichitochito zake zonse.

Pa msinkhu umenewu ndi pamene mwana amakonza m'mene dzikoli lizionekera, kuchokera mu zimenezi iye amakonza zikhalidwe ndi zichitochito ndi upangiliwake, malinga ndi m'mene zakhazikikira pa iye ndi mmenenso munthuyu angasangalalire pa dziko lino, komanso ndi m'mene angakapambanire ku umoyo wosatha .Poona kuti uwu ndi udindo wamakolo, quruan inachemelera zimenezi ngati m'mene Allah akunenera kuti: **“ Mulungu akukulamulani za ana anu”** (Surat An Nisa: 11) komanso mtumiki anakamba mwa tchutchutchu kunena kuti: **“Mwana wina aliyense akamabadwa amabadwa ali ndi chikhulupiliro choti Mulungu ndi mmodzi koma makolo ake ndi amene amamupangitsa kukhala muyuda, mkirisitu kapenanso wopembedza moto”** (Bukhar – 1359).

Hadith imeneyi ikulozera zithu zingapo izi:

1. Chikhulupiliro ndi chibadwa cha munthu wina aliyense, yemwe angasiye chikhulupilirochi ndiye kuti wakhota kamba kosokonezedwa ndi munthu wina.
2. Yafotokozanso hadithyi udindo wa ukulu wamakolo pophunzitsa ana awo.
3. Ikusonyezanso za zotsatira za chilengedwe kapena nyengo pa maphunziro⁽²⁵⁾.

Ena mwa ma ubwino a Allah pa munthu ndi oti anatsegula mtima wa mwana aliyense kumayambiliro kuti apeze chikhulupiliro mopanda kufuna umboni⁽²⁶⁾, pa chifukwa chimenechi, makolo akukakamizidwa kuti ateteze udindo wawo ume newu mwaubwino kwambiri ndi kuyereza chibadwa cha ana chimenechi, ndikuti awalere anawo pachipembedzo choona chomwe chamangidwa ndi maumboni ochokera mu quruan ndi chiphunzitso cha mtumiki (swa)(sunnah), ndipo makolo asadalire nyengo yokha kuti iphunzitse ana awo yomwe imatenga matanthaunzo ake kuchokera mu zomwe zili mbali mwake, chisilam chongoyendera kutsatira sichingamulepheretse munthu kusochera - pa nthawi ino imene dziko lapansi latseguka ndikufewetsedwa komanso kufupikitsidwa kwa dzikoli - komanso sichingathetse kusungunuka kwa umunthu.

Ndithu mtima wa mwana ndiwabwino bwino ulingati mwala wa mtengo wapatali womwe siunalembedwepo kapena kujambulidwa kalikonse, umalora kulembapo china chili chonse akaphunzitsidwa ndi kuzoloweretsedwa ndipo amakulira muchimenecho ndipo amasangalala padziko lapansi komanso akasangalala ku umoyo wosatha, ndipo makolo ndi aphunzitsi ake amapeza nawo malipiro, ndipo akazoloweretsedwa zoipa nalekeleredwa ngati zinyama amakhala watsoka ndi woonongeka ndipo machimo ake amapeza nawo yemwe amamuyang'anira iye ndi kumutsogolera⁽²⁷⁾, chifukwa kungomulera kwa pamwamba ndikumene kumachitika ali wamg'ono akangosiyidwa kuti aziyenda pa chibadwa pake naphunzitsidwa zimenezo, zotsatira zake zimakhala zovuta (kumubweza)⁽²⁸⁾.

Mwana amene amakulira mu banja lomwe chikhulupiliro chake chili cholimba ndi logwiritsa ntchito maphunziro achipembedzo, ana amatsatira makolo awo pa china chili chonse, komanso amakonza matanthaunzo ake kudzera pamene akuonera kwa makolo ake, tikupeza kuti pali anthu omwe amapereka matanthaunzo a chipembedzo molakwika, zomwe zimabweretsa zotsatira zosiyana pa ana, pomwe ana akamakula napeza makolo awo kuti samagwiritsa ntchito maphunziro achipembedzo; ndithu ndithu zimakhala zovuta kuti iye akopeke kuchipembedzoku chifukwa iye kuumwana wake sadaone chizindikiro cha chipembedzo, chifukwa amakhala alibe kulondoleledwa kuli konse kwa chipembedzo⁽²⁹⁾.



KUKULA MWACHIPEMBEDZO KWA ANA



Ndithu chipembezo pa mwana chimayamba ndi ganizo limodzi - ganizo lake la kupezeka kwa Allah-, kenako amayamba kuonekera m'maganizo ena- mon- ga ganizo la kulenga kapena lokudza umoyo umene uli nkudza, kapena Angelo, kapena ziwanda (asatana)-, zizindikiro zakukula mwa chipembedzo mwa mwana zimaonekera mu zinthu zinayi izi:

- A** Practical (ntchito): mwana amawapatsa matanthauzo achipembezochithuz- ithuzi chokhuzika, akamakula amaonjezera kuwalitsa chimenechi, koman- so amachidziwitsitsa choona cheni cheni, ndipo amachiyika m'malo ake akakula.
- B** Kupereka chithunzithunzi: mwana amatsatira makhalidwe a akulu akulu m'mene akuchitira pamapemphero (ibadah) awo ndi mapepho awo (dua) popanda kufufuzamatanthauzo ake kapena kufunikira kwake pa uzimu, ndi- ye ndizofunikira kuti mphunzitsi apindule kuchokera mukukhota kwa ana pa msinkhu umenewu m'mene angadzoloweretsere anawo chikhalidwe komanso nsanamira za chikhulupiliro ndi zotsatira pa zimenezo.

- C** Kufuna kukhala wofunikira (utilitarian): mwana akamaona chisangalalo cha makolo ake ndi mphunzitsi wake ndi amene amuzungulira pamene iye akupanga ena mwa mapemphero, mwanayu amatha kupanga zimenezi ndicholinga choti apeze chikondi cha anthu amenewa, komanso ngati njira yopezera mapindu ena ake, kapena pofuna kutchinga chilango chimene chimafuna chimupeze.
- D** Kukhala membala: mwana amakondera chipembedzo chake kuchokera pansu pa mtima molimbikitsidwa ndi zofuna za chibadwa chake chimene chinadzalidwa mu mtima wake, pa chifukwa chimenechi iye amasangalat-sidwa kuti azitchedwa msilamu wochokera mwa asilamu, ndipo chizindikiro chapamwamba choti ndiwe msilamu ndiko kuchikonda chithu chifukwa cha Allah⁽³⁰⁾.

Kuchokera pa zimene zadutsazi tikupeza kufunikira kokhazikika pa maphunziro a zachikhulupiliro, komanso kufunikira kwa makolo ndi aphunzitsi kuti alimbikire kwambiri kuwayandikitsira ana chikhulupiliro - maka maka nyengo ino imene yachuluka mayesero, zosokoneza ndi zosewera sewera (zibwana) ndi njira zake za zimenezo-, zina mwa zofunikira kwambiri makolo kuti awapangire ana awo ndi izi:

Choyamba: kumupangitsa mwanayo kuti achimvetse chibadwa chake (choti Allah ndi mmodzi) mu mtima mwa mwanayo, zomwe zingachitike kudzera pomuphunzitsa kalima tauhid (laa ilaaha illallah).

Chachiwiri: kumuphunzitsa mwana chikhulupiliro pomupatsa msichi zonse, zomwe zimachitika podzala chikondi mwa mwanayo chomukonda Allah ndi mtumiki wake ndi kumamuphunzitsa buku lolemekezeka la Quru'an⁽³¹⁾.

Kupezeka kwachibadwa chachipembedzo mu mtima mwa mwanayo zimaghandiza makolo pa ntchito yawo yophunzitsa mwanayo, chibadwa chime-nechi chimasonyeza kuti mwa iye muli kambeu kachipembedzo, ndiye kambeu kameneka monga mbeu zina, sikamalola kusinthidwa koma kamangolola kukao-ngolera ndi kukapititsa patsogolo. Ndipo chibadwa chimenechi chitha kugwirit-sidwa ntchito mu njira zosiyanasiyana posakhala njira yomwe chinalengedwera, pomwe chisilamu chimayitanira kuti chibadwa chimenechi chiongoleledwe kun-jira yomwe chinalengedwera⁽³²⁾.

Mwazithu zofunikira kwambiri kuti mwana akule nazo; ndi nsanamira zachikhu-lupiliro zokwana zisanu ndi imodzi, ndipo chofunikira kwambiri mu nsanamira zimenezi ndi kukhulupilira mwa Allah; ndipo kumukonda Allah ndicho chotsatira chakuppezeka kwa nsichi za chikhulupiliro zinazo, ndipo Allah anakupanga ku-mukonda iye kukhala chithu chimene chimamanga kwambiri chikhulupiliro pa iye komanso ndichimene chimasonyeza kugonjera kwa munthu mwa iye (Al-

lah) zimene zikutanthauza kuti kumukonda kwambiri ndikofunika pomumvera komanso podana ndi adani ake (Allah) ndipo zikukakamizidwa kuti chimenechi chipose chokondedwa chilichonse cha dziko lapansi, Allah akunena kuti: **“Nena iwe mtumiki kuti: ngati makolo anu, ana anu , akazi anu, ndi anansi anu ndi chuma chimene mwachipata, ndi malonda anu amene mukuopa kuti angaonongeke, ndi nyumba zanu zimene mukuzikonda, (ngati zimenezi zili) zokondeka kwambiri kwa inu kuposa Mulungu ndi mtumiki wake ndikuchita Jihad pa njira Allah yo, choncho dikirani kufikira Mulungu adzabweretse lamulo lake (lokukhaultsani),Ndipo Mulungu satsogolera (sawaongola) anthu otuluka mchilamulo”** (Surat Taubah: 24)

Ndipo anayipanga mbiri yoyambirira ya akapolo omwe iye (Allah) amawakonda yoti iwo amamukondanso Allah; Allah akulankhula mu buku lake lolemekezeka kunena kuti **“Eh, inu amene mwakhulupilira! Amene mwa inu angasiye chipembedzo chake, ndiye kuti posachedwa Mulungu adzabweretsa anthuena omwe iye awakonda, nawonso amukonda; odzichepetsa kwa asilamu anzawo; amphamvu kwaosakhulupilira; omenyera nkondo chipembedzo cha Mulungu, saopa kudzudzula kwa odzudzula,umenewu ndi ubwino wa Mulungu; amau-pereka Kwa amenewawafuna, ndipo Mulungu ndiye mataya; ngodziwa kwam-biri”** (Surat Al Maidah: 54).

Anafotokozanso kuti tauhid yabwino ndi yokhayo imene imapatula Allah pom-patsa chikondi chosagawika Allah akunena kuti **“Pali ena mwa anthu amene akudzipangira milungu namaifananiza ndi Mulungu, amaikonda monga mom-we amamkondera Mulungu, Koma Asilamu amene akhulupilira amakonda Mulungu koposa”.**(Surat Al baqarah: 165).

Kupanga ibada (mapemphero) imene Mulungu anatilengera kumeneko ndiko kumukonda Allah kwa pamwamba, ndipo phata la tauhid ndiko kuyeretsa chikon-di chako kwa Mulungu yekha,limenelo ndiye phata lopembedza, imeneyo ndiye ibada yeni yeni, siyingakwanire tauhid mwa kapolo mpaka chitakwanila chikondi chake pa Allah komanso chipose zokondeka zathu zonse, moti zonse zimene ka-polo amazikonda zizitsatira chikondi chimenechi, chomwe chidzapereke chipam-bano kwa iye⁽³³⁾.

Ndiye chikondi chimenechi chomwe chamangidwandi chikhulupiliro ndiyo njira yaikulu yokonzera khalidwe la ana ndikuwakhazikitsa pachipembedzo cha chisil-amu ndikumvera Allah ndi mtumiki wake, yemwe mu mtima mwake mwadzalid-wa ndi chikondi cha Allah ndi mtumiki wake amakhala woongoka pa chikhalidwe ndi mapemphero ake, ngakhale atakhota pa nkhani zina ndi maganizo ena, ng-akhaleso aziwala; chikondi chimene chili mwaiye chidzam’bwezeretsa munjira yoonngoka - muchifuniro cha Mulungu ⁻⁽³⁴⁾chifukwa chakuti chikondi chimakhala ndi mphamvu za mkati osati zakunja zokha ayi.

Ndithu masomphenya omwe chikhulupiliro cha chisilam chimapereka kuzolengedwa, ndi opambana chifukwa amagwirizana ndi chibadwa cha munthu, komanso zimagwirizana ndi nzeru zolongosoka ndipo sizimakhulana ayi⁽³⁵⁾. Komanso ili ndi kupambana kumene sikumapezeka mu zikhulupiliro zina chifukwa muli kukwanila kwa kasanjidwe ka nzeru, chikhulupiliro, miyambo ndi malamulo, zili choncho chifukwa chakuti iyo ndi ndondomeko ya kaganizilidwe ndi chikhulupiliro, ndipo iyo imayika tanthauzo la maziko adziko ndi chiyambi cha dziko ndi mathero ake ndi zopezeka mkati mwakemo ndi za mtsogolo, imatanthauziranso momveka bwino chiyambi cha moyo wa munthu ndi mathero ake, kenako cholinga chomwe dziko linalengedwera, ndi cholinga chomwe munthu analengedwera kuti akwanilitse, izi zimathandiza kuyankha mafunso amunthu okhudza chilengedwe omwe ali ofunika kwaiye kufunsa chifukwa chachibadwa chanzeru zake, chifukwa munthu sangakwanitse kupeza mpumulo wa bwino akapanda kupeza mayankho okwanila ndi ogwira mtima amafunso amenewa, kupanda kutero amasowa mtengo wogwira nthawi zonse, chifukwa amakhala asanapeze tanthauzo la umoyo umenewu⁽³⁶⁾.



ZIPATSO ZA MAPHUNZIRO Aza CHIKHULUPILIRO



Pali mapindu angapo omwe mphunzitsi amapeza akamaphunzitsa maphunziro a zachikhulupiliro, ena mwa iwo ndi awa:


- 1** | **Choyamba:** Amatengedwa kuti ndi woyambilira ndiwamachawi popanga zinthu zabwino; iye amafufuza khomo lililonse lomwe lingamuyandikitse kuchisangalalo ndi chifundo cha Mulungu.
- 2** | **Chachiwiri:** Kulimbitsa mkati mwa munthuyu; chikhulupiliro chenichen-indichimene chimakonzaka khalidwe la munthu.
- 3** | **Chachitatu:** Kusalabadira zamoyo wadziko lapansi; mtima wake suyezamira za dziko lapansi koti mpakana gwero lazofuna zake ndizochita zake kukhala kufuna kupeza za dziko la pansi ayi.
- 4** | **Chachinayi:** Kupeza chilimbikitso chochokera kwa Allah; chifukwa chakuti Allah amayang'anira zichitochito za kapolo wake yemwe ali wokhulupilira zomwe zimakwanilitsa pa iye maubwino eni eni ndikumamubweretsera iye chisangalalo mu umoyo uno ndi womwe uli nkudza.
- 5** | **Chachisanu:** Kukhala ndi chikhumbokhumbo mwa Mulungu; chikhulupiliro chikamaonjezereka, kapolo amaonjezereka kusakaikira mwa Mulungu ndi khumbo khumbo lake mwaiye ndikutalikirana ndizolengedwa.
- 6** | **Chachisanundichimodzi:** Kusaonekera kwa zoipa zake ndikuchepa kwa zolakwika pakati pa anzake; chikhulupiliro chikamaonjezereka m'mitima zotsatira za maganizo wamba sizimapezeka mwa iye ndipo khumbokhumbo lake lokhala ndi makhalidwe abwino ndi apamwamba limakhala la mphamvu.
- 7** | **Chachisanundichiwiri:** Kukhala wothandiza anthu; munthu wokhulupilira wamphamvu amapanga zodzithandiza yekha ndikuthandizanso omwe amuzungulira.
- 8** | **Chachisanu ndi chitatu:** Kukhala ndi mtendere wa mu mtima; kusakaikira Mulungu kokhala ndi chikhulupiliro kukakhazikika mu mtima wa kapolo, mwa iye mumatuluka chiopsezo chomwe chimapereka mantha kwa anthu⁽³⁷⁾ (anthu amamuopa ndi kumupatsa ulemu).

Zomwe zimaMAnGA MAPHUNZIRO AZACHIKHULUPILIRO



Ndithu zikufunika makolo awaphunzitse ana awo zinthu zomwe zingalimbitse chikhulupiliro chawo, ndi kukhonza machitidwe ndi zikhaliidwe zawo, ndikukulitsa kudzimva kwawo kuti iwo ndi mmodzi wa m'bado uno (ummah uno)wa Muhammad, ndiye zoyambilira zomwe zikubwera pansu pa tanthauzo limeneli ndi izi:

1. Kuwaphunzitsa anawo nsanamira zisanu ndi imodzi za chikhulupiliro, ndichidule cha chikhulupiliro molingana ndi malamulo achisilamu (Sharia) mogwirizana ndi chibadwa cha munthu, komanso kupewa kumangowalakatulitsa chabe, zomwe zimachotsa uzimu wa chikhulupiliro, koma ayetsetse kupanga izi munjira ya zichitochito (practical) yomwe ingadzutse mitima ndi kugwedeza ubongo, ndikukonza chikhaliidwe.
2. Kuwaphunzitsa ana zomukonda mtumiki (saw) ndi akubanja lake la mtumiki, azikazi ake ndi ophunzira ake (maswaha-ba ake) onse popanda kupyola muyezo pa iwo kapena kuwapondereza.
3. Kuwaphunzitsa anawo kuti azilemekeza chipembedzo ndi zizindikiro zake (za chipembedzo), kuwachenjeza kutiasa-mazipeputse komanso asiye kusadzilabadira⁽³⁸⁾.
4. Kuwaphunzitsa kuti chikhulupiliro chokakamiza sichimakhalachokwanila pokha pokha pakhale ntchito zabwino zimene zili zopitilira ndi kumvera malamulo a Mulungu komanso adziwe kuti chikhulupiliro chimapunguka chifukwa chonyozera malamulo a Mulungu, ndipo maphunziro azachikhulupiliro oona amakhala ofunikira kwambiri popereka zipatso zabwino pachikhaliidwe, zichito chito ndi mapembedzedwe⁽³⁹⁾.



5. Kudzala chikhulupiliro cha tsiku lachiweruzo m'mitima mwawo ndikulile-mekeza tsikulo, ndikulumikiza zatsikulo ndi ntchito zomwe azipanga kapolo padziko lapansi, kwa yemwe angagwire ntchito ya bwino ndiye kuti adzapeza Jannah, ndipo yemwe angagwire ntchito yoyipa ndiye kuti akalowa kumoto wa malawi.
6. Kutsindika kuti Allah amamuyang'anira kapolo wake, ndikuti iye amawamva ndikuwaona iwo, palibe chimene chimabisika kwa iye (Allah) mu zichitochito zawo.
7. Kuzamitsa kudzimva kwake munthuyo kuti ali pachoonadi, zimenezi zimapangitsa iye kugwiritsitsa chipembedzo chake mwamphamvu ndi mwa ulemelero wake⁽⁴⁰⁾.



NJIRAZAMAPHUNZIRO zODZALIRA CHIKHULUPIIRO

Njira zimenezi tingazigawe m'magawo awiri, gawo loyamba lokalekeza nthawi yotha msinkhu⁽⁴¹⁾, ndipogawo lachiwiri ndi lapambuyo pakutha msinkhu.

Ndiye zina mwa zinthu zimene zimathandiza kudzera mu chikhulupiliro asan- afike pokutha msinkhu ndi izi:

1. Kumufotokozera maina opembedzera omwe iye amawamva kudera lomwe amakhalalo monga- Abdullah, Abdulrahman ndi Abdulkareem – ndi- kuyetsetsa kuwalisa matanthauzo ake mwa chidule, ndikuyikira chidwi akamamvelera Adhana, ndikuwaphunzitsa mau oyenera kutchula tsiku lil- ilonse (dhikiri) ndi madua ndikumapanga panga zimenezo pali iwowo⁽⁴²⁾. Ndikumamukumbutsa mwanayo za mitendere ya Mulungu imene ili pa iye- , makamaka pakudya - chifukwa chakuti zimachitika chitika, ndi kumuphun- zitsa kutchula Mulungu asanayambe kudya ndi kumutamanda Mulungu akamaliza kudya.
2. Kumupangitsa kuti aloweze ena mwa ma sura ochokera mubuku loleme- kezeka la Quru'an, ndikupangitsa kuti amvetse kuti amenewo ndi mau a Mulungu wapamwamba, ndipo masurah oyambirira kuti awadziwe ndi masura monga surat Al fatiha, Ikhlasi, falaq ndi surat Annas, ndizotheka ku- mupanga kuti aloweze ndakatulo ndi nyimbo zomwe mukupezamo zomwe mumafuna kumuphunzitsa mwanayo makamaka matanthauzo achikhulu- piliro cholondola⁽⁴³⁾.
3. (Makolo) azikonda kutchula dzina la Mulungu pa mwanayopakachitika chomwe amachikonda kapena chomusangalatsa, ndipo zikufunika kuti pomuchula Mulungu asalalumikize ndi ukali wa Mulungu ndi zilango zake panthawi imene mwanayu ali wang'ono, asamachulutse kukamba za ukali wa Mulungu ndi zilango zake ndi moto wake.
4. Kumuongolera mwana kuti adziwe kukongola kumene kuli mchilengedwe, ndi mphamvu ndi mgwirizano wake (wachilengedwe), ndi cholinga choti adziwe ukulu wa mlengi ndi kuthekera kwake, komanso azimukonda Mulun- gu; chifukwa Mulungu amamukonda iye ndikumufewetsera chilengedwe.

5. Kumphunzitsa mwana miyambo yakapangidwe kake ka zinthu, ndikumuzoloweretsa kukhala wachifundo komanso wothandizana ndi azinzake ndi miyambo yakalankhulidwe ndi kamvedwe, ndi kudzala mwaiye zipatso za chisilamu kudzera pakumusonyeza anthu abwino, zinthu zomwe zingapangitse kukhala ndi moyo wodzadzidwa ndi zinthu zapamwamba kwambiri, ndikumatengera zinthu za bwino kuchokera kwa anthu omwe amuzungulira⁽⁴⁴⁾.

q w
h r p m i
A x e
m k s q y y
v A



Pomwe mwana uja wakula timaonjezera njira zina zomwe mkati mwake muli kulingalira ndi kuganizira; zina mwaizo ndi izi:

1. Kumuphunzitsa mwana za kukula kwa dzikoli ndi luso komanso ukadaulo womwe Mulungu anaonetsa pakalengedwe ka dziko limeneli; ndicholinga choti mwanayo azimukuza Mulungu ndi kumulemekeza ngati m'mene Mulungu akunenera kuti: **“Kameneko ndi kakonzedwe ka luso ka Mulungu kamene adakonzero chinthu chilichonse mwa ukadaulo. Ndithu Mulungu akudziwa zonse zimene mukuchita”**. (Surat An-Naml: 88).
2. Kumukumbutsa zolinga za Allah pa zichitochito zake, ndizolengedwa zake; ndicholinga choti mwanayo amukonde Allah ndi kumutamanda, komanso ndi cholinga chimene Mulungu analengera usiku ndi usana, kenakonso dzuwa ndi mwezi, komanso chimene analengera ziwalo zimene zimatidziwitsa zochitika (sense organs) monga ngati : makutu, maso, lilime, ndi zina zotero, Mulungu akulankhula mu Qur'u'an kunena kuti **“Kodi salingalira mwa iwo okha (nkuona kuti) Mulungu sadalenge thambo ndi nthaka ndi zapakati pake , koma mwachilungamo”** (Surat Ar Rum: 8).
3. kugwiritsa ntchito mipata imene yapezeka pomuongolera mwanayo kudzera muzochitika za tsiku ndi tsiku mwanzeru kuti azikonda zabwino ndi kutalikirana ndi zoipa, mwachisanzo: akadwala timuuzo kuti azidalira mwa Mulungu, timuphunzitse madua, komanso kumuganizira Mulungu zabwino, ndikufuna machilitso ovomerezeka (Ruqyah), tikampatsa chipatso kapena sweet yomwe waifuna timpemphe kuti athokoze mtendere umenewo ndikumuuza kuti zimenezi zachokera kwa Mulungu, komanso apewe makolo kumuphunzitsa mwanayo matanthauzo a zachikhulupiliro munyengo ya zopweteka makamaka kumbali ya mwanayo, chifukwa iye sakhala ndi kuthekera komvetsa kokwanira kuti asiyanitse⁽⁴⁵⁾.
4. Pakufunika kuti pagwirike ntchito yowadzoloweretsera ana aja zikhalidwe za chisilamu zomwe tikufuna kukwanilitsa, choncho mphunzitsi akufunika azionetsa chikhalidwe chabwino kuti anthu azitengera, ndithu kulumikiza chikhalidwe ndi chipembedzo pa zichitochito zathu zimapangitsa kuti kuphunzitsa kwathu kukhale koona osati komangolongosola kokha ayi⁽⁴⁶⁾, ndipo pakufunika kugwiritsa ntchito tinkhani tomwe tili ndi phindu mkati mwake ndi cholinga chowapatsa ana zinthu zofunikira, ndikutalikirana ndi nkhanu zosafunikira, ndiye pafunikira kubweretsa kankhaniko mu njira ya-fanizo (Drama) komanso mwachikoka, komanso osaiwala kuonetsa njira ndi zikhalidwe zomwe zikupezeka mu nkhanimo, komanso kudzera mutinyimbo, ndizothekanso kudzala chitsanzo chapamwamba ndi makhalidwe abwino, ndizothekanso kuphunzitsa mwana kuti amudziwe mtumiki (saw) kudzera pakumuphunzitsa mbiri ya mtumikiyo; ndicholinga choti azimukonda mtumikiyo ndi kumumvera makamaka zokhudza umwana wakewo,

ndi m'mene amakhalira (mtumikiyo) ndi ana ndi kufewa kwa mtima wake kwa anawo, ndikumufotokozera kaonekedwe kake, ndikumatchula zikhalidwe zake zapamwamba komanso ndikuwafotokozera nkhani za ophunzira amtumiki (maswahaba) ndi azikazi a mtumiki ndi akubanja lake - Mulungu awasangalalire onsewo-.

5. Kukhala pakati kati pamene ukuwaphunzitsa ana chipembedzo, ndipo osawasenzetsa zomwe sangakwanitse, ndipo tisaiwale kuti masewero ndi macheza ndi zimene mwana amazikondetsetsa kwambiri, choncho tisamusenzetse zosephana ndi msinkhu wake komanso nzeru zake, monga kumuchulukitsira maudindo ndi kumuletsa kusewera, zimenezi zimamumana mwana uja zofuna zaumwana wake zachibadwa; chifukwa kupyola muyezo ndi kuchulukitsa kudzudzula kumabweretsa zotsatira zoipa komanso kudzimva uchimo, kawiri kawirizimenezi zimachitika pa mwana woyamba; chifukwa makolo ena amalimbikira kuti ampange mwana wakeyo kukhala chitsanzo chokwanira.
6. Ndizofunika kuti mwana asiyidwe popanda kumulowelera akulu akulu kwa nthawi yayitali, koma kungomukonzera zichito chito (activities) zomwe zingapatse kuthekera kozitulukira zinthu mwa iye yekha malinga ndi kuthekera kwake ndikuidziwitsitsa nyengo yomwe yamuzungulira, mu izi muli kumeretsa ukatswiri ndi chikondi chokonda kuwerenga pa mwanayo.



7. Ndithu kumpatsa mwana chilimbikitso kumabweretsa ubwino pa iye. Ndi-po zimapangitsa mwanayo kugwira ntchito molimbika popanga zinthu zofunikira, zikakhala kuti kukonza ndi kuongolera khalidwe la mwana zikuchitika chifukwa cha chikondi komanso kufunafuna malipiliro kwa Mulungu; zimapangitsa kuti mwanayo apeze chikhalidwe chabwino munjira ya pamwamba, ndipo ndizofunika kumuthandiza mwanayo kuti aphunzire zomwe zili zoyenera kwa iye, choncho amadziwa zoyenera kuti iye achitilidwe komanso kuwachitira ena, zoyenera kuchita ndizosayenera kuchita, akumva ulemero ndi udindo wake, molumikizana ndi chisamaliro (control) chabwino ndipo tipewe kupereka maumboni⁽⁴⁷⁾.
8. Kudzala mu mtima wa mwana kulemekeza buku lolemekezeka la Qur'u'an, kuti azidziwa kupatulika kwa quru'an ndikugwiritsa malamulo ake, pogwiritsa ntchito njira yofewa komanso yachikoka, moti azidziwa mwanayo kuti ngati akuwerenga bwino buku lolemekezeka azakhala mu mlingo (level) umodzi ndi angelo oyera, komanso azoloweretsedwe kukhala ndi chidwi pogwiritsa ntchito miyambo ya kawerengedwe ka Qur'u'an- monga kupanga bisimillah kapena audhubillah, kuyilemekeza Qur'u'an ndikumayimvetsa bwino-, komanso timuzoloweretse mwana kumvera ndime zamu Qur'u'an; chifukwa zimenezo zimabweretsa kuthekera koyankhula chiyankhulo cha chiarabu (Arabic) ndipo zimamulimbikitsa kuwerenga, ndipo ndizotheka kumuphunzitsa ena mwa matanthaunzo amu Qur'u'an omwe ali ndi matanthauzo achikhulupiliro kuchokera mumasurah omwe
9. analoweza monga surat Al fatiha, Ikhlasi, Al falaq ndi Annas, komanso kuchulukitsa tinkhani tamu Qur'u'an yolemekezeka mwachidule, momveka ndi mobwereza bwerezakomanso mukafotokozedwe kosiyana siyani⁽⁴⁸⁾.
10. Ndizothekanso kugwiritsa ntchito njira ya mafunso ndi mayankho, tiikirenso chidwi kuti funsolo lizikhala ndi uthenga womwe tikufuna kufikitsawo, ndipo yankho likhale ndi mau achidule kwambir, oyenera ndi msinkhu wamwanayo ndikumva kwake, izi zimathandiza mwanayo kupeza zikhulupiriro (values) ndi zikhalidwe zabwino ndikusintha zichitochito zake kupititsa ku ubwino.
11. Nzotheka kuphunzitsa pogwiritsa ntchito njira ya kupenta ndi kukongoletsa, chithuzi chomwe tikufuna kuchikongoletsacho chikhale ndi matanthauzo achikhulupiliro chomasithasintha nthawi ndi nthawi, nzothekanso

kuphunzitsa pogwiritsa ntchito mipikisano ya mitundu yosiyana siyana, koma ndibwino kuti mipikisanoyo izikhala yoyenda yenda, chifukwa mwana amakonda mipikisano yoteroyo komanso amatenga nawo mbali⁽⁴⁹⁾.

12. Tiwafotokozere anawo ena mwa ma hadith achikhulupiliro, kapena magawo ena amahadith wo, omwe akuyenera ndi kaganizilidwe kawo mwachidule mowapangitsa kuti achikonde pogwiritsa ntchito ziganizo zachidule zomwe angathe kuzimvetsa malinga ndi nzeru zawo⁽⁵⁰⁾, ndizothekanso kumuphunzitsa mwana mobwereza bwereza ziganizo zomwe zingameretse chikhulupiliro; kuti zikhazikike mwa iye ndikuti azigwiritsa ntchito pa iye yekha, monga; chikachitika chinthu anene kuti “chachitikachi chachitika muchikonzero cha Mulungu, ndipo Allah zimene wafuna amapanga”, “yedzamila mwa Mulungu”, “Mulungu ndi wakutha chilichonse”, ndi ena otero.

Nzothekanso mothandizidwa ndi makolo kapena mphunzitsi

mwana kukongoletsakalasi yake ndi chipinda chake chogona pogwiritsa ntchito mau achikhulupiliro –monga “ine ndine msilamu”, “ine ndi makonda mbuye wanga Mulungu”, “msanamira za chikhulupiliro”, izi ndi njira zophunzitsira zomwe zimakhazikika mu nzeru zake makamaka akamazionaona⁽⁵¹⁾.



- 13.** Timuphunzitse mwana kuti mavuto amamupeza wina aliyense; ndikuti anthu onse apadziko pano Mulungu amawayesa ndi mayesero amitundu yosiyana siyana, ndipo timuphunzitse kuti ndithu Mulungu wapamwamba mwamba samapanga chithu chilichonse pokha pokha ndi cholinga chabwino ndi chapamwamba, ndiponso tidzale mwa iyeyo chikhulupiliro choti yemwe amabweretsa zabwino ndikutchinga zopweteka ndi Mulungu, ndipo chifundo chake chimaposa mkwiyo wake, komanso timufotokozere kuti chipulumutso nthawi zonse chimabwera pambuyo pa mavuto, ichi ndi chizolowezi cha Mulungu chokhazikika, ndikuti tikulitse mwa mwanayo kumuganizira Mulungu zabwino zokha zokha; ndithu zimenezi pazokha ndi mapemphero (ibada), ndipo tikhazikitse mwaiye kuti zomwe amatisankhira Mulungu ndi zabwino kwambiri kuposa zomwe timadzisankhira tokha, ndipo munthu amangofunika kumangopilira, ndikupanga zinthu zomwe zili zovomerezeka pachipembedzo pofuna kuthana ndi mavuto amenewa, komanso azisangalatsidwa ndi chikonzero cha Mulungu nthawi zonse, ndikuyembekezera malipiro kwa Mulungu pa zimenezi. Pomaliza timuphunzitse kugwiritisa nchito madua; imeneyo ndi geni (business) ya phindu kwa kapolo (wa Mulungu) nthawi zonse⁽⁵²⁾.




ZIPANGIZO ZOPHUNZITSIRA (za maphunziro)



Zina mwa zipangizo zophunzitsira zomwe zimathandizira kudzala chikhulupiliro mu mtima wa mwana ndi izi:

1. Kukhala ndi chitsanzo chabwino; chitsanzo chabwino chimatengedwa kuti ndi imodzimwanjira zikulu zikulu komanso zofunikira popereka zotsatira, kumeneko ndiye kuyika chizindikiro chakuya mwa mwanayo, ndipo mtumiki (saw) ananenetsa kwambiri kufunikira kwa chitsanzo chabwino mu umoyo wa mwana, monga momwe tikumvera kuchokera muhadith yomwe anailandira Abdullah bun Aamir (r.a) iye adati: anandiyitana mayi anga tsiku lina pomwe mtumiki (saw) anali limodzi ndi ife, mayiwo anati ee! iwe Abdullah tabwera ndikupatse china chake ndiye mtumiki anati: **“Mukufuna mumpatse chiyani?”** mzimayi anati ndimafuna ndimpatse tende, ndiye mtumiki anati: **“koma mukapanda kumpatsa kathu mulembedwa kuti mwanama”** (Abu Daud-4991). Muhadith ina iye anati **“yemwe angamuitane mwana kuti iwe tabwera ndikupatse ichi kenako ndiye osampatsa ndiye kuti wanama”** (Ahmad -9724), chitsanzo chabwino ndinjira yopambana komanso yothandiza.

2. Ulaliki woona; ulaliki ungathe kuperekedwa munjira zingapo, kutheka kuperekedwa munjira ya chindunji yomwe ili ya chizolowezi, kuthekanso kupereka kudzera mukupereka zitsanzo, kapena kupereka ulalikiwo mkati mwakankhani, kapena kudzera munjira yakukambirana, ndizina zotero, kotero tikuyenera kumusankhira mwanayo mtundu wa ulaliki womwe siungamutopetse⁽⁵³⁾.



3. Kumunyengelera ndi kumuopseza; mukuyankhula kwina : **“njira ya malipiro abwino ndi chilango”**, ndipo iyi imatengedwa kuti ndi imodzi mwa njira zapamwamba zomwe nzeru zimakhuzidwa nazo mwa changu, chifukwa zimakhudza mwa chindunji muchibadwa cha munthu chomwe analengedwa nacho, chibadwa chakukonda kupeza phindu, ndikudana ndi mavuto ndikuyesa kuzitchinga zoipazo pa iwo, koma zimenezi zikufunikira kuchitika mwachangamu komanso mwachoonadi mopanda kuonjezera kapena kupungura, mtima wa mwana ndi wofewa kwambiri, choncho sizimafunika kumuopseza; chifukwa mtima utha kulandira zinthu zosiyana, pamenepa pazafunika kuchulutsa mbali yomulimbikitsa ndi kumunyengelera, mu msinkhu umeneu mwana amafunikira kumunyengelera osati kumuopseza ayi⁽⁵⁴⁾.
4. Kumuphunzitsa (training) ndi kumuzoloweretsa kupanga panga zinthu zomwe waphunzira (practice); kumudzoloweretsa mwana kutiazikhala ndichidwi chomusangalatsa Mulungu ndikumuopa Mulungu ndi kumuchitira manyazi, ndi kumudalira iye nthawi zonse, ndikuona kuti chilichonse chili m’manja mwa Mulungu; zonsezi zimampatsa mwana mphamvu ndi kulimba pamayesero ena alionse, komanso chimapereka chisangalalo ndi chikhulupiliro zomwe zingadekhetse mtima wake ndi kuuika mtima wakewo kukhala pa mtendere.
5. Kubwereza bwereza; iyi ndi njira imene ngakhale maphunziro apano ndi lutha lomwe linachitikakumbuyoku (experience) zimalimbikitsa kufunikira kwake pamaphunziro komanso pokhazikitsa maphunziro mwa munthu⁽⁵⁵⁾.
6. Kukambirana; kukambirana ndi mwana kumakulitsa kumvetsa kwake ndi kutsegulira ngodya zosiyanasiyana za maphunziro, koma pakufunika kulemekeza nzeru zamwana ndimwanayo, ndikumamumvetsera bwino lomwe ndikumakambirana naye mwabata, ndicholinga choti kukambirana kukwanilitse mgwirizano wopambana ndi waphindu. Kudzera mukuteromo, kumuphunzitsa mwanayo ndi kumuongolera kumatheka⁽⁵⁶⁾.
7. Buku; kotero ndizofunika kwambiri kuti papezeke nyumba yowerengera-mo ma buku (library) yokonzedwa bwino molingana ndi zofuna za mwana pa maphunziro, pachikhalidwe ndi pa chikhulupiliro, ndipo ndibwino kuti ikhale laibulaleyo yamitundu yosiyana siyana – monga yomvelera, yoonera ndi yamanambala-, zofunikanso kwambiri kuti mu ma laibulale amenewa mukhale mitundu yosiyanasiyana ya timkhani; chifukwa nkhani ndi njira yophunzitsira, yaphindu komanso yofunikira⁽⁵⁷⁾, ndipo kudzera mumbiri ya mtumiki ndi maphunziro ake (sirah) muli tinkhani tokhala ndi cholinga, taphindu komanso tabwino.

8. Sayansi ngati njira yatsopano yophunzitsira; iyi ndi njira yatsopano yomwe imathandizira kufalitsira maganizo, kuwayandikitsira komanso kuwakhazikitsira pa mwanayo; kuti athe kuwamvetsa ndikuwazindikira matanthauzo ake, chifukwa chamaganizo ndi mapata amenewa maphunziro amakhala akuperekedwa munjira yooneka komanso mmitundu yachikoka yomwe imapangitsa mwanayo kuti asachokepo ndi kuchilandila ndi mtima wonse.
 9. Chikoka chachibadwa mwa iye; mwa mwana muli zikoka zosiyansiyana zomwe zingathe kugwiritsidwa ntchito, zina mwaizo ndi izi: kusewera, kuthandizana ndi zina zotero, kudzera mumasewero amwana, mwanayo amatha kudziwa dzikoli ndi zimene zamuzungulira, ndi kufotokoza za m'mene akuonera ndikudziwira dzikoli. Ndiye nzotheka kugwiritsa ntchito pomufotokozerana mwana uja matanthauzo oona okhudza umoyo podzala chikhalidwe mu mtima wa mwana, zimenezo zingachitike pogwiritsa ntchito njira yophweka komanso yoyenerera, monga: kuonerera, kupeza phindu pa zochitika zikachitika pochenjeza ndi kumuongolera mwana⁽⁵⁸⁾, ndithu zimasiya mwa iye zotsatira zamphavu.
 10. Dua (kumupempha Allah); ndi chizindikiro cha kuonetsa umphawi ndi ukapolo pa mbuye wake ndi kuti iye akufunikira thandizo lochokera kwa Allah ndi kulakalaka ma ubwino a Allah, moti Allah analimbikitsa akapolo ake kuti azimupepha iye ndipo anawalonjeza kuti adzawayankha, Allah wapamwamba akunena kuti: **“Ndipo mbuye wanu wanena kuti: ndipempheni ndipo ndikuyankhani”**. (Surat Ghaafir: 60).
- Ndipo Dua ndi chida chachikulu cha mphunzitsi chopezera zolinga zake pa maphunziro, icho ndi chida chomwe amachigwiritsa ntchito aphunzitsi akulu akulu kwambiri omwe ndi atumiki a Mulungu (madalitso ndi mten-dere za Mulungu zipite kwa iwo) ndi cholinga choti akhazikike pachikhu-lupiliro ndi pa tauhid' Allah akunena kuti **“Ndipo kumbukirani pamene**

Ibrahim adanena kuti: oh! mbuye wanga uchiteni mzinda uwu (wam-akkah) kukhala wa mtendere: ndipo nditalikitseni ine ndi ana anga ku-machitidwe opembedza mafano”.(Surat Ibrahim: 35). Choncho pempho (Dua) yamwana ndichimodzi mwazizindikiro zikulu zikulu zosonyeza kuti mwanayo analedwa bwino.

11.

Kuyesera ndikutsatiza; mwana mwachibadwa chake amakonda kuyesera zinthu, choncho apatsidwe mpata mwachitsanzo wotsogolera pa mzikiti, azipempheretsa ndi kuwerenga Quru’an, azipanga khutubah, aziyimandi-kumalankhula, kapena akhale mphunzitsi ndiye aziphunzitsa ndikuma-fotokozera, ndi zina zotero, zimenezi zimakhazikika kwa mwanayo matanthauzo, ndipo amasunga ulemmerero wazithu zimenezi.



ZOMUYENEREZA KUTI AKHALE MPHUNZITSI



1. Kukhala wa chifundo ndi kuleza mtima; maphunziro sapereka zipatso za bwino akapanda kulumikizana ndi kuleza mtima, mpaka mitima itakhala ndi chisoni, taonani swahaba uyu Aqra'u bun Habisi atamuona mtumiki (saw) akumukisa Hassan ndi Hussein ndipo Aqra'u analankhula kuti: ndithu ndithu ine ndili ndi ana khumi (10) ndipo sindinamukisepo angakhale m'modzi mwaiwo, ndipo mtumiki anati **"Yemwe sachitira chifundo ena nayeso samachitilidwa chifundo"** (Bukhar -5997), analankhulanso mtumiki (saw) kuti: **"Anthu achifundo Allah amawachitiranso chifundo, choncho chitirani chifundo zolengedwa zadziko lapansi, akuchitirani chifundo yemwe ali kumwamba (Allah)"**. (Abu Daudu-4941).

2. Kuleza ndi kukhululuka; mtumiki (saw) anafika nalo pamwamba khalidwe limeneli, monga hadith imene anailandira Anasi mwana wa Maliki (r.a) akunena kuti: **"tsiku lina ndikuyenda ndi mtumiki (saw) atavala chovala chomwe chinapangidwa Kunajirani chokhuthala mmbali mwake, ndiye kunadzabwera munthu wachimdzimidzi namukoka mtumiki chovala chake chija mwamphamvu mpaka ndinaona phewa la mtumiki (saw) litakalidwa ndi kolala la mkanjowo chifukwa chakukoka mwamphamvu, kenako ananena kuti Ee!, iwe Muhammad talamula kuti ndipatsidwe ineyo gawo lachuma cha Mulungu chomwe ukusunga, ndiye mtumiki anamutembenukira iye naseka, kenako analamula ophunzira ake kuti amupatse iye chumacho"**. (Bukhar -5809).

Mwazinaso zimene zikulumikizana ndi kuleza ndi kukhululuka, Mulungu akunena kuti: **"Gwiritsa kukhululuka (kukhala ndi khalidwe lokhululuka) ndipo lamulira zabwinondi kudzipatula (kuzochita) zaumbuli"** (Surat Al Araf: 199), ndiye pofuna kuti kuleza mtima kukhale koona; mtumiki (saw) analimbikitsa kuti anthu asamapse mtima ndipo analetsa, muhadith yoonadati: Munthu wina wake anamupempha mtumiki kuti: **"ndilangize"** ndiye mtumiki (saw) anati: **"Osapsa mtima ; ndipo (mtumikiyo) anabwerezereza mau amenewa kambiri mbiri, kenako anamuuzanso kuti :"****osapsa mtima"**. (Bukhar -6116).



- 3.** Kupilira; mphunzitsi akufunika azipilira ndipo asamapupulume pamene akuphunzitsa ana ake ndipo mphunzitsi asafulumizitse kuti aone zotsatira ndikupeza mwachangu zimene zikufunikira, moti mpaka kuyamba kutaya mtima ndikumaona ngati akulephera kukwanilitsa ayi, ndiye mphunzitsi akakhala wosapilira; alingati munthu wapaulendo yemwe alibe kamba.
- 4.** Chilungamo; chifukwa iye (mphunzitsi) akamasiyanitsa pakati pa ophunzira popanda chifukwa chomveka kutenga mbali komanso kulowelera kwa ana mu phunzirolo kumachepa, kupondereza pachili chonse ndi chithu chochititsa manyazi.
- 5.** Kukhulupilika; mphunzitsi akuyenera kukhala wokhulupilika ndi wonena zoonpa pa ophunzira ake, ndipo kukhulupilika ndimbiri ya atumiki omwe amadzafalitsa uthenga wa Mulungu, ndipo ndichofunikira chachikulu pofuna kukonza ndi kulongosola ntchito komanso pofuna kupeza zolinga zake ndi kupambana kwake.
- 6.** Kusamala malamulo amulungu (kumuopa Mulungu); chifukwa yemwe angasamale malamulo a Mulungu; Mulungu amampatsaiye kuthekera komwe samayembekezera, kusamala malamulo a Mulungu kumayendera limodzi ndikuthekera kochokera kwa Mulungu ndi ubwino ndi kupambana konse padziko lapansi pano ndi ku umoyo umene uli nkudza.

- 7.** Kuyeretsa ntchito (kupanga mapemphero ndicholinga chosangalatsa Mulungu yekha); chifukwa ntchito ikakhala yosachitira Mulungu yekha idzabwezedwa kwa mwini wakeyo, kutanthauza kuti sadzalandira malipiro abwino kwa Mulungu ndipo sadzapeza chilichonse mu ntchito yakeyo kupatula minyama ndi kutopa.
- 8.** Maphunziro; chifukwa yemwe waphunzira amadziwa zomwe zikufunika (kuchitakuti zimuthandize) panopa ndi mtsogolo mwake, pomwe ena amaononga zapanopa ndikuyipitsanso mathero ake.
- 9.** Luntha (kuchiyika chithu m'malo ake); mphunzitsi akamaika chithu malo ake, ndithu zimenezi zimabweretsa zipatso zabwino, komanso maphunziro akewo amabala zipatso, ntchito yaikulu ya mphunzitsi ndiyo kulowa mu mtima wa mwana ndikuugwiritsa ntchito pomuongolera ndi kumphunzitsa zabwino.
- 10.** Kuikhulupilira ntchito ya maphunziro; ndithu maphunziro ndi mphatso ya mtengo wa patali ya umoyo komanso uzimu, ndipo amene sakhulupilira ntchito ya maphunziro sangakwanitse kupereka mphatso ya pamwamba imeneyi⁽⁵⁹⁾.
- 11.** Kupititsa patsogolo; mphunzitsi aziyikira mtima popititsa patsogolokutheker kumene kuli mwa mwanayo kuti afike pa mlingo womwe ungapangitse kuti akwanilitse udindo wake pa maphunziro







NSANAMIRA ZA MAPHUNZIRO **Aza** **CHIKHULUPIIRO**



ZILIPO

Zilipo zisanu ndi imodzi:

Msanamira yoyamba:

Kukhulupilira mwa Mulungu mmodzi yekha

Nsanamira ya chiwiri:

kukhulupirira angelo

Nsanamira ya chitatu:

kukhulupirira ma buku a Mulungu

Nsanamira ya chinayi:

kukhulupirira atumiki

Nsanamira ya chisanu:

kukhulupirira za tsiku lomaliza

Nsanamira ya chisanu ndi chimodzi:

kukhulupirira za chikonzero cha Mulungu

Msanamira yoyamba:

Kukhulupilira mwa Mulungu mmodzi yekha:



Chibadwa cha munthu, nzeru zake ndi malamulo a Mulungu zimasonyeza kuti Mulungu alipo, moti chilengedwe china chilichonse pachibadwa chake chimakhulupilira za mulengi wake. Ndipo kudzera munzeru; zimavomereza kuti zolengedwa zonsezi alipo amene anazipezeketsa, pomwe kudzera m'malamulo a Mulungu; tikupeza kuti zipembedzo zonse zomwe zinachokera kumwamba zinavomereza kuti kuli mulengi.

Mu kukhulupilira mwa Mulungu muli zinthu zinayi:-

choyamba: kukhulupilira kuti Mulungu alipo.

chachiwiri: kukhulupilira zaumbuye wake, kuti iye ndi mbuye, Mlengi, wopereka, wodyetsa, ndi woyendetsa chili chonse.

chachitatu: Iye yekha ndiye woyenera kupembedzedwa mu umodzi wake ndi kuti alibe wofanana naye.

chachinayi: kukhulupilira maina ake ndi mbiri zake zomwe zimatsindika zakukwanira kwake ndi ubwino wak.

Choncho timuphunzitse mwana zinthu zinayi zimenezi kuti akule akumudziwa Mulungu ndi kumukuza ndi kumukonda, nsanamira imeneyi (ya kukhulupilira mwa Mulungu) ndi manthu wa nsanamira zina zotsarazo.

CHIFUKWA CHIYANI TIMAWAPHUNZITSA ANA KUKONDA MULUNGU

1. Chifukwa Allah wolemekezeka ndi amene anatipezeketsa ife, natilenga mkalengedwe kabwino natipanga ife kukhala apamwamba kuposa zolengedwa zina, ndikutipatsa ife mtendere wa pa mwamba kwambirichimene chili chisilamu-, komanso anatipatsa ma ubwino ochuluka osalin-gana ndi m'mene tilili, pambuyo pake ndikutilonjezanso Jannah; kukhala malipiro antchito zathu zomwe, komanso mphatso yopatsidwa kuchokera kwa Mulungu, iye ndi mwini kupereka maubwino anthawi zonse padziko lino ndi ku umoyo wosatha.

2. Chifukwa chakuti chikondi chimabweretsa kulemekeza ndi kuopa mwa chinsinsi kapena moonekera, Pali kufunikira kwa kuti ana athu azilemekeza mbuye wawo komanso azimuopa osati azingooopa chilango chake ndi moto ayi, mapemphero awo azikhala chowasangalatsa chawo ndi chowateteza kukusochera.
3. Chifukwa chakuti Mulungu ndi wamoyo mpaka kale kale yemwe sadzamwalira, yemwe saodzera kapena kugona iye amakhala ndi anthuwo nthawi zonse, komanso iye ndi amene amawateteza iwowo kuposa m'mene amachitira makolo awo, choncho kuyedzamira kwawo mwa Mulungu ndikumukonda kwawo kumatengedwa kuti ndikofunikira kwambiri, kuti adziwe kuti ali ndi chochiyedzamira champhamvu yemwe ndi Mulungu wapamwamba mwamba.



4. Chifukwa iwo akamukonda Mulungunayikondanso Quru'an, iwo azilimbikira kupemphera.

Ndipo akadziwa kuti Mulungu ndi wabwino amakondanso zabwino ndiye kuti azipanganso zonse zomwe zili zabwino, ndipo akadziwa kuti Mulungu amakonda anthu olapa kwaiye, oziyeretsa, ochita zabwino, opereka chaulele, opilira, oyedzamira mwa Mulungu, osamala malamulo a Mulungu amalimbikira kuti atchuke ndi mbiri zimenezi, oterowo amafuna kupeza chisangalalo cha Mulungu ndi chikondi chake komanso ubwezi ndi Mulungu, ndikuti Mulunguyo aziwateteza iwo⁽⁶¹⁾.

Ndipo akadziwa kuti Mulungu sakonda anthu achinyengo, okanira, odzikweza, opsola muyeso, opondereza ndi anthu oyipa; iye amayetsetsa kupeza mbiri zonsezi malinga ndi kuthekera kwake chifukwa chomukonda Mulungu ndi kufuna kumusangalatsa.

5. Chifukwa kumukonda Mulungu zimatanthauza kuti Mulunguyo alipo, zimezezi zimapangitsa kuti apeze mpumulo, kudekha ndi kukhazikika, ndipo samadandaula kapena kubanika, pakutero amapeza mtendere wa mu mti-ma ndi thupi kumatenda amaganizo ndi ziwalo, koma chofunikira kwambiri kuposa zimenezi ndiko kutetezeka kumachimo⁽⁶²⁾.

TINGAWAPHUNZITSE BWANJI ANA ATHU KUKONDA MULUNGU

1. Njira yokhayo yodzalira chikhulupiliro mwa mwana ndikugwiritsa ntchito njira yokhudzika (sense organs), kutanthauza kuti: ife timadalira ziwalo (sense organs) polimbitsa chikhulupiliro cha mwana pa mbuye wake, moti timagwiritsa ntchito chikhalidwe choonekera chomwe chamuzungulira mwanayo monga: dzuwa, mvula ndi pempho (dua)-, kudzera muzimenezi timamuphunzitsa mwanayo kuti kuli Mlengi yemwe akuyendetsa dziko limeneli ndipo timamulimbikitsa kuti azifunsa zomwe sakudziwa⁽⁶³⁾, ndipo timayesetsa kuyika chithuzi thuzi chachikhulupiliro m'maso mwa ana kuti azitha kuona maumboni oti Mulungu alipo kuchokera pazomwe akulongo-soleledwa ndi kuphunzira pamaphunziro⁽⁶⁴⁾.

Choncho tiyesetse kuwalitsa luso la Mulungu lodabwitsa ndi lapamwamba, monga m'mene Mulungu akutiongolerera kuti tizona ndikulingalira za chiyambi chakalengedwe kamunthu, Mulungu akunena kuti **"Aganizire munthu kuti kodi adalengedwa kuchokera kuchiyani?"** (Surat At Tariq: 5), akunenanso kuti **"Ndimwa inu nomwe; kodi simuona (simulingalira)?"** (Surat Adhariyat: 21), komanso tizilingalira za chakudya cha munthu

kuti Mulungu anachipezeketsa bwanji, ndi kufotokozera ndondomekoyomwe chayenda (steps), Mulungu wapamwamba mwamba akunena kuti **“Alingalire munthu (m’mene chilili) chakudya chake”** (Surat Abasa: 24), komanso tionetse ukadaulo wa Mulungu pa zolengedwa zakezi zomwe zimasonyeza ukulu wake ngati m’mene Mulungu akunenera kuti **“(Kodi akunyozero kulingalira zisonyezo za Mulungu), sakulingalira za ngamila (camel)kuti idalengedwa motani?” Ndi thambo (limene akuliona nthawi zonse) m’mene lidatukulidwira (kutali popanda mzati)?” Ndi mapiri ndi momwe adakhazikitsidwira, Ndi nthaka momwe idayalidwira”**.(Surat Al Ghashiyah; 17- 20).

Nzotheka kuyandikitsa matanthauzo akulu akulu amenewa ndikudabwitsika kwa chilengedwe ndi ukulu wa Mlengi ndi luso lake (Mulunguyo)munzeru za anawo malinga ndi misinkhu yawo yosiyana siyana pogwiritsa nchito zipangizo zofotokozera momveka, zosiyana siyana zomwe zikupezeka pogwiritsa ntchito luso lamakono (technology)⁽⁶⁵⁾, choncho mwana pachibadwa chake adzamukonda aliyense yemwe anamulengela iye zinthu zazikulu zikulu zonsezi ndikumuphunzitsa iyeyo (maphunziro okhudza zimenezi).




2. Kumuphunzitsa mwana mayina oyera a Mulungu ndi mbiri zake zomwe zimasonyeza kukwanira kwake kwa Mulungu ndi ubwino wake, ndipo Mulungu ndi wachifundo komanso wachisoni, yemwe chisoni chake chimakwanira chilichonse, ndipo Iye Mulungu ndi wokhululuka yemwe amakhululuka zolakwika, ndipo iye amakhululuka ndi kufufuta zolakwikazo, Iye ndi wopereka yemwe amapereka ngakhale popanda wina wake kupempha kapenanso chifukwa, ndipo iye ndi muongoli yemwe amaongolera akapolo ake ku zonse zothandiza, iye ndi wachikondi yemwe amakondedwa ndi kukonda, ndipo popanda chikaiko, kumudziwa Mulungu kumeneku kumamuthandiza iye kuti amukonde Mulunguyo⁽⁶⁶⁾.
3. Tipewe kulankhula mau oti: mukapanda kumvera mau angawa Mulungu akulangani; Pali kusiyana komuphunzitsa mwana kuti Mulungu amamulanga yemwe akunyozero, ndi kulumikiza chilango cha Mulungu ndi kumvera Mulungu nthawi zonse, ndikumamuopseza nacho chimenecho, ndithu zimenezi zimamulepheretsa mwana kuganiza mwakuya ndi mwa ukadaulo wa Mulungu ndi ukulu wake, sizimafunikira pophunzitsa kudalira kumuopseza mwanayo za Mulungu, koma ndi zokakamizidwa komuphunzitsa mwanayo kukonda Mulungu ndi kumukuza ndikumulemekeza⁽⁶⁷⁾, tisamupatse Mulungu zomwe zingabweretse chithuzi thuzi choipa cha Mulungu pa mwanayo.
4. Mwana akamawaona makolo akupemphera mapemphero aswalaat ndi ena otero muzinthu zimene zili zokakamizidwa, kapena akuchinyalanyaza chinthu choipa (chaharam); kawiwri kawiri mwana amafunsa chifukwa chomwe akumapangira zimenezi, ndiye pakufunika kuti payankho lawolo papezeke zakutchulidwa za chikondi ndi kumvera Mulungu, ukhoza kukhala mphunzitsi poyendera kutsatira ndi kumukonda Mulungu wapamwamba mwamba, chifukwa mwana amatsatira makolo ake, izi ndi zimene zimadzala chikondi mmitima ya ana ndi kuwafotokonzera ana aja za Jannah ndi mitendere ya muyaya yomwe Mulungu wawakonzera akapolo ake olungama ku Jannah.

5. Mwana akafika msinkhu womamvetsa matanthauzo a zinthuzomwe zili zokakamizidwa kwa iye; ndithu iye aphunzitsidwe kuti kumukonda Mulungu ndi kokakamizidwa; chifukwa Mulunguwolemekezeka ndiyemwe anatilenga ife mukalengedwe kolongosokandipo anatipatsa zosiyana siyana natiyika ife kukhala apamwamba kuposa zolengedwa zake zina, natipatsa mtendere wachisilamu⁽⁶⁸⁾, ndipo timuphunzitse mwana kuti mitendere yonse yomwe yatizungulira imachokera kwa Mulungu, timuphunzitsenso m'mene angatamandire Mulungu pamitendere imeneyi ndi kumuthokozaza ndikumupemphanso zoonjezera, ndipo kuyang'ana mitendere yotereyi kumabweretsa chikondi⁽⁶⁹⁾.
6. Kumuthandizira njira zomwe zingamuthandize kubweretsa chikondi cha Mulungu ndi mtumiki wake monga mau azichitochito ndi zina zotero⁽⁷⁰⁾



Nsanamira ya chiwiri: kukhulupirira angelo



Ndithu mu kukhulupilira mwa angelo mukupezeka zinthu izi: kuvomereza kuti angelowo alipodi, kukhulupilira omwe tawadziwa maina awo mwa iwo, kukhulupirira nkhani yoona iliyonse yokhudza iwo, komanso kuwakonda iwo. Ndipo ena mwa matanthauzo a maphunziro omwe akufunikira kuti adzalidwe mu mtima wa mwana okhudza angelo ndi monga:

1. Kuwaphunzitsa kuti iwo (angelowo) ndi zolengedwa za Mulungu zinalengedwa kuchokera kudangalira, Aisha (Mulungu asangalare naye) anati: adanena mthenga wa Mulungu (saw) kuti: **“Analengedwa Angelo kuchokera kukuwala (dangalira), ndipo zinalengedwa ziwanda kuchokera kumoto, komanso analengedwa Adamu kuchokera ku chomwe munauzidwa (kudothi).** Apa zidzakhala zokwanira kungofotokoza mosonkhanitsa (general) ngakhale osafotokozero pakalengedwe kake.
2. Kuwaphunzitsa maina a angelo omwe tikuwadziwa, ena mwa maina awo ndi monga: **Jibril**, yemwe ndi wodalilika komanso mtsogoleri wa angelo onse, ndipo iye ndi amene anavumbulutsa buku lolemekezeka la Quru'an (kuchokera kwa mulungu kunka kwa mtumiki Muhammad, pomwe **Mikail** ndi mgelo yemwe anapatsidwa ntchito yogwetsa mvula, ndipo **Israfil** yodzaimba lipenga tsiku la chiweruzo.

Timuphunzitsenso mwana kuti kuli angelo omwe anyamula mpando wachifumu (arishi) wa Mulungu, kulinso ena omwe amalemba ntchito zathu, ndipo ena anapatsidwa ntchito yotitetezera kuzosiyana siyana padziko pano, ndi ena otero.

3. Kumufotokozero kuti chiwerengero cha angelo ndi chochuluka zedi, ndikuti yemwe amadziwa kuchuluka kwawo ndi Mulungu yekha basi, ndipo iwo (angelowo) ndi zolengedwa zomwe zinapangidwa kuti zizingomvera Mulungu ndikupanga zokhazo zomwe Mulunguyo wazilamulira kuti zichite, ndi kuti aliyense mwa angelowo ali ndi ntchito yomwe anapatsidwa kuti azigwira ndipo sangaisiye ntchito imeneyo.
4. Ndipo iwo sachimwa, iwo amapembedza Mulungu mosalekeza ndipo sapumira kapena kuipidwa ngakhalenso kudzikweza ndipo iwo amakonda anthu okhulupilira, kuwapulumutsa, kuwapemphera kwa Mulungu, kuwatetezera; ndipo iwo amatsata malo omwe pakutchulidwapo Mulungu ndikumakhala nawo (anthu omwe akutchula Mulunguwo).
5. Kuwapangitsa ana kuti azikonda angelo, izi zingatheke kudzera powapangitsa anawo kuti amvetse bwino za chibadwa cha angelo chokonda zabwino ndi chidwi chawo pa anthu okhulupilira, izi zidzadzala moyo wa ubale ndi chikondi mwa anawo pa zolengedwa za madalitso ndi zosachimwa zimenezi (**angelo**); chifukwa iwo amakhala akumuyeretsa Mulungu (**Tasbeeh**), kumupempha chikhululuko Mulungu (**Istighfar**), komanso kupempha zabwino kwa Mulungu (**dua**) kuti zipite kwa anthu okhulupilira ndiponso amawauza nkhani zabwino anthu okhulupilira omwe akhazikika pachoonadi namagwira ntchito zabwino kuti akalowa kuminda ya mtendere(**Jannah**), komanso angelowo amawapemphera madalitso anthu okhulupilira, kuwapulumutsa kuchokera kwa adani ndikuwalimbikitsa⁽⁷¹⁾.

Ndipo angelo ndi omwe amasunga ntchito za anthu, chifukwa Mulungu anawatumiza iwowo kudzatetezera akapolo ake, Mulungu akunena kuti “(**Munthu aliyense**) **alinalo gulu (la angelo) patsogolo pake (omwe) amamulondera (ndi kulemba zomwe akuchita) mwalamulo la Mulungu**”.

6. Kuwaphunzitsa kuti kukhulupilira mwa angelo zimafunika kuwalemekeza, chifukwa iwo ndi akapolo a Mulunguolemekezeka, sanyozera lamulo la Mulungu ndipo chomwe Mulunguyo wawalamula iwo (angelowo) amapanga, ndipo ndizokakamizidwa kuwachotsera angelowo mbiri zimene siziri zoyenera pa iwo.

7. Kulimbikitsa ukhondo wapathupi pa anawo, chifukwa angelo amanyatsidwa ndi zinthu zomwe anthunso amanyatsidwa nazo. Jabir mwana wa Abdullah (r.a) anasimba kuti mtumiki (saw) adati: **“Munthu akadya anyezi kapena adiyu (mukulankhula kwina anati: munthu akadya anyezi, kapena adyo, kapenanso kurath (leek), asayandikire malo omwe akupempherera anthu (ochuluka), chifukwa angelo amayipidwa ndizomwe anthu amaipidwa nazo”.**(muslim -564).
8. Kuwafotokozera kuti kupezeka kwa angelo ndi kukhulupilira mwaiwo kuli ndizolinga zakuya zochuluka monga:
 - Kutu munthu adziwe kuti Mulungu ali ndi kudziwa ndi kuthekera kwakukulu komanso nzeru zapamwamba kwambiri.
 - Kutu msilamu adziwe kuti alindi chitetezo, podziwa kuti ali ndi asilikali omwe akumamutetezera ndi kumamupulumutsa kudzera muchilamulo cha Mulungu.
9. Timudziwitsenso mwana kuti mgwirizano wathu ndi angelo pakalengedwe kawo, kupezeka kwawo, komanso mmene amatiyang'anirira, umamudziwitsa (mgwirizano umenewu) munthu kuti iye ndi wofunikira kwambiri komanso wamtengo wapatali, ndipo umachotsa mwaiye maganizo oti iye ndi wopanda pakekapena wonyozeka, ndi chimenechi munthu amadziwa mlingo wake, ndipo amayetsetsa kukwanilitsa udindo wake waukulu womwe anapatsidwa.



Nsanamira ya chitatu:

kukhulupirira ma buku a Mulungu

Ndithu mukukhulupilira mabuku a Mulungu mukuyenera kupezeka mfundo zi-kubwerazi:


1. Kukhulupilira kuti pali mabuku omwe anatsika kuchokera kwa Mulungu, ndipo icho ndichimodzi mwa chifundo chachikulu cha Mulungu pa akapolo ake; chifukwa mugulu lililonse la anthu analitumizira buku loti anthu ake aongokere, ndipo malamulo ake amakhala olingana ndi anthuwo, choncho mwana afotokozeredwe momveka bwino kuti kutsitsa kwa mabuku ku-meneku ndi mtendere waukulu zedi; chifukwa mabukuwo ndiwo amene atidziwitsa za Mulungu, zatsiku lomaliza, zabwino komanso zoipa.
2. Kuvomereza maina amabuku omwe tikuwadziwa mwaiwo, monga: buku la (**Suhuf**) lomwe linavulutsidwa kwa Ibrahim, **Torah** kwa Musa, **Zaboor** kwa Davide (Daud), ndi **Injeel** (chipangano chatsopano) kwa Yesu (Issa) komanso **Quru'an** kwa Muhammad, madalitso ndi mtendere zipite kwaiwo onse.
3. Kutumiza mabuku amenewa amavomerezana lina ndi linzake ndipo satsutsana kapena kusemphana, Mulungu akunena kuti “(**buku la Qur'an**) lomwe likuyikira umbonimabuku omwe adalipo patsogolo pake” (Surat Al Maida: 48).
4. Kukhulupilira nkhani zomwe zili zoona m'menemo, ndipo kumudziwitsa kuti mabuku akale anasinthidwa ndi kusokonezedwa ndi anthu, chifukwa iwo (mabukuwo) anali ndi nyengo yoyikika komanso kwa anthu anyengo yokhayo basi, moti Mulungu sanawateteze mabuku amenewo ngati m'mene amaitetezera quru'an ayi.
5. Kukhulupilira kuti **Qur'an** inabwera kudzafuluta mabuku akale onsewo, ndikuti malamulo a Qur'u'an ndiwo akuyenera kugwiritsidwa ntchito ku-fikira tsiku la malipiro, moti nzokakamizidwa kutsatira zomwe zalembedwa m'menemo, kuloleza zomwe zalolezedwa m'menemo, kugwiritsa ntchito mavesi achindunji ndi kuimika manja pamavesi ovuta kuwamvetsa, ndi ku-malekeza momwe Qur'u'an yalekeza ndi chiphunzitsa chake⁽⁷²⁾.

Zina mwa zinthu zofunikira kwambiri kuti zipezeke mukukhulupilira mabuku a Mulungu, ndi izi: kumpangitsa mwana kuti aloweze **Quru'an** yolemekeka

kuyambira ali wang’ono, pambuyo pake- mwazomwe zimathandizira kuonjezera nzeru mwa mwana ndiko kuti- akwanitse kugwiritsa ntchito Quru’an- yo, ndipo mphunzitsi adzadzitse mu mtima wa mwana nyengo ya mavesi a Quru’an, chifukwa Quru’an imatiyitanira kuti tizilingalira ndi kuganizira za kalengedwe ka thambo ndi nthaka, kalengedwe ka munthu ndi zomwe zatizungulira, ndicholinga choti chikhulupiliro chathuchikwere ndikuti maphunziro athu asakanikirane ndi ntchito, ndipo kuloweza Quru’an yathu yolemekezeka ndi kumva komanso kuwadziwa matanthauzo ake zimamufikitsa munthu pa nzeru zapamwamba zedi⁽⁷³⁾. komanso zimazoloweretsa lilime la mwana kulankhula mwa mfundo zothyakuka ndi momveka bwino kwambiri, izi zimatheka pamene akukonza lilime lake powerenga quru’an mwadongosolo, komanso zimameretsa kuganiza mwa uzimu- monga: kuopa Mulungu ndikudzipereka mwathunthu kwa Mulungu, kufunitsitsa zabwino kuchokera kwa Mulungu, ndikufewetsa mitima ndi maganizo-, ndipo zimazoloweretsa mwana kugwiritsa ntchito maphunziro ndi miyambo ya mu Quru’an yolemekeka pa zichito chito zonse zamoyo wakewatsiku ndi tsiku, komanso zimaphunzitsa mwana kukhala ndi moyo woongoka ndi makhaliidwe apamwamba, phindu linanso amapeza malipiro aakulu ndi ulemerero waukulu kuchokera kwa Mulungu wapamwamba mwamba pamene mwanayo akukhala nawo pa mabwalo oloweza Quru’an⁽⁷⁴⁾.

TINGAMULIMBIKITSE BWANJI MWANA KULOWEZA QUR’AN

1. Timufotokozere maubwino a Quru’an ndi maubwino akuiloweza, a kuiwerenga ndi kuyiphunzira komanso ndi kuigwiritsa ntchito, monga m’mene ananenera mtumiki (saw) kunenakuti **“Muziwerenga Quru’an chifukwa iyo idzabwera tsiku lachiweruzo kudzawapemphera (dua) omwe amaiwerenga”**. (Muslim- 804), anatinso mtumiki (saw): **“adzauzidwa munthu wowerenga Quru’an kuti werenga numakwera kumwamba ndipo uziililira ngati m’mene umachitira uli padziko lapanisi, ndithudi malo ako akakhala pamene utasiyirepo”**. (Tirmiz-



2914), anatinso (saw): **“Fanizo la wokhulupilira yemwe amawerenga Quru’an ali ngati chipatso chonunkhira bwino komanso chokoma bwino, pomwe fanizo la wokhulupirira yemwe sawerenga Qur’anali ngati tende, sanunkhira koma amakoma bwino, pomwe fanizo la achiphamaso (munafiq) yemwe amawerenga Quru’an ali ngati chipatso chonunkhira kwambiri koma chowawasa kwambiri, ndipo fanizo la achiphamaso yemwe sawerenga Quru’an ali ngati chipatso chomwe chilibe fungo lililonse komanso chowawasa kwambiri”** (Bukhar- 5427), ananenanso mtumiki (saw) kuti: **“Wabwino kwambiri mwainu ndi amene waiphunzira Quru’an ndi kuwaphunzitsanso (Qur’an yo) anthu ena”** (Bukhar- 5027), ndipo timutchulire zitsanzo zina za ophunzira ake (maswahaba) omwe amaikira mtima pa Quru’an, izi ndi njira zikulu zikulu zogwedzera mtima wofuna kutengapo mbali pa Quran⁽⁷⁵⁾.

2. Tiwalembetsere m’masukulu ndi m’magulu olowezeramo Quru’an, mmizikiti, kapena kumufunira mphunzitsi wa Quru’an, kukonza zomulimbikitsira maphunziro akewo ndi mphoto, ndikukhazikitsa mipikisano kuti ana ophunzira azipikisana.
3. Tikuyenera kuwafewetsera kalowezedwe kawo ka Quru’an kuchiyambi chawo ndicholinga choti aziikonda ntchito imeneyi, tiyambe ndi juzu amma chifukwa iyi ndi yomwe ili ndi masura aafupi bwino komanso omveka mofananirako katchulidwe, zomwe zimapangitsa kuti Quru’an ikhazikike mwa mwanayo mosavuta⁽⁷⁶⁾, ndipo masurah (ma chaputala) amu juzu amma amenewa amakamba kwambiri zachikhulupiliro, kotero amakonza chikhulupiliro ndi makhalidwe a anawo, komanso kuteteza moyo ndi thanzi lawo, chifukwa Quru’an yolemekeka ndi chikumbutso cholembedwa, kuonjezerapo pa izi, ndithu Quru’an imakonzanso lilime ndi kulionjezera kuthekera kofotokoza bwino polankhula.





4. Kumayesetsa kufotokozera mwachidule Quru'an yo pamene mwana akuiwerenga ndi kuiloweza; ndicholinga choti ndime za mu Quru'an zitsegule mtima ndi nzeru zake, ndipo munthu aliyense asaganize kuti mwana si woyenera kumutanthauzira Quru'an ayi, chifukwa mwa mwana muli kuthekera kodabwitsa kwa kuloweza ndi kumvetsetsa⁽⁷⁷⁾.
5. Timuphunzitsenso kuti Quru'an ndi machiritso, chifundo komanso madalitso, Mulungu akunena kuti **"Ndipo tikumatumiza ndime zina za Quru'an zomwe ndi machiritso ndiponso ndi chifundo kwa anthu okhulupilira"**. (Surat Al Isra: 82), ndi kuti yemwe angailoweze yonse kapena gawo lina la iyo; atha kudzichiza yekha ngakhalenso kuwachiza ena pogwiritsa ntchito Quru'anyo.

Nsanamira ya chinayi:

kukhulupirira atumiki

Ndithu kukhulupilira mwa atumiki ndiko kukhulupilira koti iwo sadane-nepo bodza ndikuti zonse zomwe ankanena- kupatula pa zomwe anapekeredwa ndi anthu- ndi zoo-na komanso kukhulupilira maina a omwe tawadziwa mwaiwo, ndikuti Mulungu anawasankha iwo kuko-kera mwa anthu awo, kuti akhale osiyana nawo pamakhalidwe ndi panzeru zawo, ndicholinga choti aziwauza anthuwo uthenga wa Mulungu, Mulungu akunena kuti **“Ndi-po sitidatumize mtumiki aliyense (ndi chiyankhulo china) koma ndi chiyankhulo cha anthu akewo kuti awafotokozere momveka bwino”**.

(Surat Ibrahim: 4), chifukwa mtumiki

akanakhala wochokera mwa angelo anthu sakanamumvetsa, kotero sizoyenera kwa ife kusiyanyitsa pakati pa atumikiwa pokhulupilira ena mwaiwo ndikuwakana ena, koma tiwakhulupilire onsewo, chifukwa atumiki onse amanena zoona pa utumiki wawo komanso amalamulira anthu awo zoona zokha zokha, ndipo iwo anali otetezedwa pa ntchito yawo yofalitsa uthenga wa Mulungu, koma sitikukakamizidwa kugwiritsa ntchito kupatula malamulo omwe anatsika kwa mtumiki womaliza wa iwo yemwe ndi Muhammad (saw), ndipo zina mwa mfundo zamaphunziro zokhudza chikhulupiliro chimenechi zomwe zikuyenera kudzalidwa mwa mwana ndi izi:



1. Kuwalongosolera Ana kuti ndithu Mulungu anatomiza mu fuko (ummah) lililonse mneneri wochokera mwa iwo, kuti awaitanire anthuwo kuti azipembedza Mulungu mmodzi yekha ndi kuti azikanile zina zonse zomwe zimapephedzedwa zosakhala Mulungu, ndikuti atumiki onse ndi oyenera kuvomerezedwa, ochita ubwino ndi olungama, osamala malamulo a Mulungu ndi okhulupilika.

2. Kufotokoza momveka kuti atumiki onse amaitanira ku zofanana zomwe ndi phata la kapembedzedwe ndi maziko ake, uku kunali kumupatula Mulungu kuti ndi wayekha pa mitundu yonse ya kupembedza- pa chikhulupiliro, mau ndi zichito chito-, komanso zochikanira chilichonse chomwe chimapembedzedwa chosakhala Mulungu.

3. Kufotokozanso momveka bwino zolinga zomwe anatumizira aneneri kuzolengedwa zake, monga zolinga izi:

- kuti zolengedwazo zimupembedze Mulungu yekha ndikumupatula kuti iye ndi mmodzi,
- kuti awaongolere anthu kunjira yoongoka,
- kwadziwitsa anthu zoyenera kuchita padziko pano za chipembedzo ndi za dziko lapansi komanso
- kuwatulutsa mu mdima ndi kuwapititsa kudangalira,
- kuwatsogolera anthu ndikukwanilitsa malamulo a Mulungu pa iwo,
- ndi cholinga choti anthu azitsatira atumikiwo ndikumapanga zinthu zawo monga momwe atumikiwo akupangira.

4. Pakuyenera kudziwa chifundo cha Mulungu wapamwamba mwamba ndi kuti iye amawalabadira akapolo ake; moti mpakana anawatumizira aneneri owaongolera anthuwo kunjira yake ndikuwalimbikitsa kuti azimuthokoza Mulungu wapamwamba mwamba pamtendere waukulu ngati umenewu, ndikuti aziwakonda atumiki ndi aneneri amenewa omwe anagwira ntchito yofalitsa uthenga wakewu ndi yolangiza akapolo ake, chifukwatu anthu angakhale atapatsidwa kumvetsa ndi nzeru zapamwamba bwanji sangakwanitse ndi nzeru zawo zokhazo kuika ndikuyendetsa ndondomeko yokomera anthu onse kukhala ogwirizana, othandizana ndi opereka china chilichonse kwa yemwe ali woyenera kupatsidwa, koma atumiki amaphunzitsa anthu zinthu za phindu kwa anthuwo komanso amawaletsa zomwe zingawapatse mavuto⁽⁷⁸⁾



5. Mudzalidwe kumukonda mtumiki (saw) m'mitima ya ana, kuti athe kumumvera ndikumutsata mapazi ake ndikumulemekeza, ndikutinso asakonde cholengedwa china chilichonse kuposa m'mene akumukondera mtumikiyo, komanso azikondana ndi okhawo amene amamukonda mtumiki, ndikudana ndi aliyense wodana ndi mtumikiyo⁽⁷⁹⁾, ndiponso azilemekeza dzina lamtumiki likatchulidwa namufunira madalitso ndi mtendere wa Mulungu, komanso azilemekeza mbiri ndi ma ubwino ake chifukwa iye anali wachifundo chochuluka komanso chisoni ndipo azimulemekezanso mtumikiyo akafika mwanayo kumanda ndi kumzikiti wamtumiki potsitsa mau ake- Mulungu akamudalitsa pompatsa zimenezi (kuthekera kokazonda manda ndi mzikiti wake {saw}).

TINGAMUPHUNZITSE BWANJI MWANA KUTI AZIMUKONDA MTUMIKI(SAW)

1. Tikuyenera kuwalongosolera motsindika kuti Mulungu wapamwamba mwamba amakonda mtumiki wake (saw), ndipo iye anamusankha ndikumulemekeza mtumikiyo kuposa anthu onse, ndipo Mulunguyo anatikakamiza kumukonda mtumiki ameneyo, ndipo timuphunzitse mwanayo kuti kumukonda mtumiki ndichizindikiro chomukonda Mulungu wapamwamba mwamba, moti yemwe angamukonde mtumiki ndiye kuti amamukondanso Mulungu mwachoonadi⁽⁸⁰⁾.
2. Kumukumbutsa kuti mtumiki anali wachifundo kwa zolengedwa zonse powaongolera ndi kuwafikitsira chipembedzo chimenechi, ndipo azaonet-sanso chifundo chimenechi pa okhuluplira powapangira pempho (**dua ya shafa'a**) tsiku lachimaliziro.
3. Kumuweregera nkhani zina zochokera mu mbiri ya mtumiki (saw) yonukhira ndi cholinga choti mwana adziwe kuti mtumiki ndi chitsanzo chabwino ndi chapamwamba choyenera kuti munthu wina aliyense azitsatira. Auzidwenso (anawo) zodabwitsa zomwe mtumiki anapanga, zikhaliidwe zake zapamwamba, m'mene amawapulumsira oponderezedwa, kufewa kwake ndi amphawi, ndi momwe amawalangizira anthu zochitira ubwino ana amasiye, komanso chifundo chake pa ofooka⁽⁸¹⁾, ndipo izi zifotokozeredwe pogwiritsa ntchito mau ophweka molingana ndi msinkhu wamwanayo, ndipoosatuluka mu zomwe zikugwirizana ndi nzeru za anawo; ndicholinga choti azimvetse bwino ndi kuzisunga , ndipo tiyesetse kusintha njira ya kaphunzitsidwe ndicholinga chofuna kukwanilitsa zofunikira za msinkhu wa mwana molingana ndi misinkhu ya ana athu, komanso tionetsetse kusiyanakomwe kulipo pakati pa ophunzira okha okha ndikusiyana kwanyengo yomwe ophunzirawo akukhala⁽⁸²⁾.

4. Ana aziona pa makolo awo ndi anthu amene awazungulira kumulemekeza mtumiki ndi zichito chito zake komanso mau ake; potsatira mwachidwi zomwe mtumiki amachita, ndikumamufunira zabwino kwa Mulungu akamatchulidwa (mtumikiyo). Makhalidwe amakolo ndi zichitochito zawo, ndi imodzi mwanjira zikulu zikulu zophunzitsira mwana, nthawi ina iliyonse akapanga sunnah ina yake aziwauza ana akewo kuti: umu ndi mmene amapangira mtumiki (saw).

Ndithu kuphunzira kudzera mukuonera kumapereka chithuzi thuzi pakaleledwe koonaka ana, komanso pachikhulupiliro cholongosoka, ndipo mtumiki (saw) ndicho chitsanzo chapamwamba chomwe aphunzitsi akuyenera kumachitsatira ndikuyenda muchiongoko chake komanso kukwanilitsa ma sunnah (ziphunzitso zake) moonekera limodzi ndi ana akewo⁽⁸³⁾.

5. Kupangitsa mwana kuti aloweze ena mwa mahadith (mau amtumiki {saw}) oona omwe amasonyeza kuti chisilam ndi chokwanira komanso ndi chabwino, ndi omwe akusonyeza za makhalidwe a mbiri yabwino ya mtumiki ndi ophunzira ake (maswahaba ake), mahadith amapereka chizindikiro chachikulu pa chikhulupiliro ndi chikhalidwe komanso kukonza munthu⁽⁸⁴⁾, nzothekanso kuchititsa mipikisano bola mahadith ake akhale afupi afupi omveka bwino matanthauzo ake komanso okamba za makhalidwe ofunikira mu msinkhu wa ophunzirawo komanso ayetsetse kugwiritsa ntchito njira zachikoka, komanso mphatso ndikuyamikira munjira zosiyanasiyana.

6. Kuwafotokozera ana nkhani za ophunzira ake (maswahaba) zonena momwe iwo amakhalira ndi kulemekezera mtumiki (saw) ndi nsanje yawo pa iye, makamaka pa Maswahaba omwe anali achichepere mwaiwo, monga nkhani ya Anasi (r.a) ndi kulimbikira kwake pomutsatira mtumiki (saw),

monga tsiku limene telala wina anamuyitana mtumiki kuti akadye chakudya chomwe telalayu anakonza, Anasi adati: **Ndinapita naye mtumiki (saw) kukadya nawo chakudya chimenecho ndipo anamubweretsera buledi wa tirigu, nsuzi, momwe munali nyama yang'ombe yophika komanso nyama yofutsa (yofwafwaza); Anasi adati ndiye ndinaona mtumiki akutsata nyama yofwafwazayo (dubaa-u) mumbale yonse, kuchokera tsiku lime-neli ndinayamba kukonda (dubaa-u)".**

Thumamah anasimbanso kuti Anasi anati: **"Ndipo ndinayamba kumamusonkhanitsira mtumiki dubaa-u yo ndikumamuikira kumbali yake".** (Bukhar- 5439).

kotero mphunzitsi ayesetse kulongosola mmene maswahabah (Mulungu akondwere nawo onsewo) amamukondera mtumikiyo ndi mmene amaziperekera nsembe panjira yake, ndipo awasimbire nkhani zosiyana siyanangatzimenezi⁽⁸⁵⁾

7. Kumuphunzitsa zotsatira zakumukonda mtumiki wa Mulungu kumeneku, monga: hadith ya Anasi (r.a) yoti ndithu munthu wina anafunsa mtumiki (saw) za qiyamah kuti kodiibwera liti qiyamah (tsiku lachiweruzo) Mtumiki adati : **Nchiyani chimene wapanga chokonzekera qiyamah?” munthu ujaanati: palibe chilichonse kupatula kumukonda Mulungu ndi mtumiki wake, apa mtumiki anati iwe udzakakhala ndi yemwe umamukonda” Anasi adati: sitidasangalatsidwepo ngati m’mene tinasangalalira ndi mau amtumiki akuti: iwe udzakakhala ndiyemwe umamukonda , anatinso Anasi: ine ndimamukonda mtumiki (saw), Abubakar ndi Umaru, ndipo ndikulakalaka kuti ndikakhale nawo limodzi chifukwa chakuti ndimawakonda ngakhale sindimatha kugwira ntchitozangati zomwe iwo amagwira”.** (bukhar- 3688).
8. Kumuthandiza mwana kuti athe kuzitulukira mwaiye yekha zachilendo zokhudza kumukonda mtumiki, monga: kulemba ndakatulo, kankhani, ulaliki, nkhani (article) ndi kulimbikitsa mipikisano yosiyana siyana yokamba zakumukonda mtumiki (saw)⁽⁸⁶⁾.



Nsanamira ya chisanu:

kukhulupirira za tsiku lomaliza

Ndithu mukukhulupilira za tsiku lomaliza mukupezeka zinthu izi:

- kukhulupilira zainfa ndikuuka kwa akufa,
- kudzawerengedwa ntchito zathu ndi kudzalipidwa,
- ka mlatho kochepa kwambiri kakuthwa ngati (lezala) kamene azikaoloka anthu,
- sikelo (yomwe azikayezera ntchito za munthu),
- Jannah (nyumba ya mtendere) ndi moto.

Ndipo mwana amayamba kuzimvetsa bwino zina mwazithu zokhudza tsiku lomaliza akatha msikhu, ndipo ngati sanafike pa msinkhu umenewu ndi bwino kumawafotokozera mwachidule kwambiri, moti tizingomufotokozera kuti pa mbuyo pa moyo uno kuli moyo wina, ndikuti Mulungu analenga Jannah kukhala malo okakhalamo anthu okhulupilira, komanso moto kukhala malo okakhala anthu okanira⁽⁸⁷⁾.

Ndipo ena mwa matanthauzo amaphunziro omwe akuyenera kudzalidwa mwa mwana okhudza kukhulupilira za tsiku lomaliza ndi awa:

1. Mwana adziwe kuti ndithu Mulungu wapamwamba mwamba, adzaukitsa akufa onse tsiku la chiweruzo kuti akapeze malipiro awo antchito zomwe anagwira padziko lapansi, ngati zinali zabwino akalipidwanso zabwino, koma ngati zinali zoipa akalipidwanso zoipa.
2. Mwana adziwe kuti tsiku limeneli Mulungu wapamwamba mwamba adzapezeketsa Jannah yomwe adailenga kukhala malo a ulemelero, achisangalalo komanso

amuyaya, kuti akhale malipiro a akapolo ake okhulupilira, ndiponso adzapezeketsa moto umene adaulenga kuwakonzera anthu okanira. Anawo aphunzitsidwe zimenezi powakopa za mitendere yomwe Mulungu anaika ku Jannah kuwakonzera anthu okhulupilira.

3. Kumukambira mwana nkhani ya infa ndi tsiku lomaliza mofewetsa moonetsa chifundo cha Mulungu, chikhululuko chake ndi kufewa mtima kwake pa akapolo

ake, ndi cholinga choti musachulutse maganizo oopsa mwa mwanayo⁽⁸⁸⁾. Izi zingatheke kuzilumikiza ndi zolengedwa zina zilizonse zamoyo zomwe zimadutsa ma sitejingati omwewa, koma kuti munthu ndi wopatulika, chifukwa Mulungu anamusankha iye pomupatsa malamulo ndi kumufewetsera zolengedwa zonse kukhala panso pa ulamuliro wake, komanso anamulonjeza malipiro pazimenezi.

4. Kumufotokozera mwana kuti ndithu Mulungu samalora kupondereza, ndipo samamusiya wopondereza osampatsa chilango ayi, komanso samasiyawoponderezedwa osam'bwezera zomwe waponderezedwazo ayi, sasiyanso wolungama osamupatsa malipiro abwino ayi, pomwe ife timaona anthu opondereza padziko lapansi pano mpaka amamwalira akuponderezabe, choncho pali moyo wina pambuyo pa moyo uno kumene adzalipidwe wolungama aliyense zabwino ndi kukalandidwa woipa, ndipo aliyense akapeza chomwe amayenera kupeza⁽⁸⁹⁾.

Nsanamira ya chisanu ndi chimodzi: kukhulupirira za chikonzero cha Mulungu

Ndithu mukukhulupirira za chikonzero cha Mulungu mukupezeka zinthu izi:

- kukhulupirira kuti kuzindikira kwa Mulungu ndikokwanira,
- ndipo chopezeka chilichonse anachilemba kale chisanapezeke,
- zoti iye ndi Mlengi wa chilichonse,
- komanso kuti ali ndi chifuniro chokwanira.

Koma kuti mwana sangathe kumvetsa za chigamulo ndi chikonzero cha Mulungu pamene akadali wang'ono, ndipo ena amaonanso kuti mwana sangakwanitse kumva matanthauzo achigamulo ndi chikonzero cha Mulungu pokha pokha akapitilira zaka pafupi fupi zisanu ndi zinayi (9) zakubadwa kwake⁽⁹⁰⁾, koma pali mfundo zamaphunziro zomwe zikuyenera kudzalidwa mwa mwana zokhudza chigamulo ndi chikonzero cha Mulungu chimenechi, ndipo zina mwa izo ndi izi:

1. Kutu ndithu phata la nkhanu imeneyi ndi hadith yomwe inabwera kudzera mwa mwana wa Abbas yemwe ndi Abdullah bin Abbas, iye adati tsiku lina ndinali pambuyo pa mtumiki (saw) ndipo anati: **“Oh mwana iwe, ndithu ine**

ndikufuna ndikuphunzitse mau awa: “Umusunge Mulungu ndipo iye akusunga, umusunge Mulungu umupeza patsogolo pako, ukafuna kupempha uzimupempha Mulungu, ukafuna thandizo uzipempha kwa Mulungu, ndipo dziwa kuti angakhale anthu onse atasonkhana kuti akuthandize pa china chake, sangakwanitse kutero pokha pokha pachokhacho chimene Mulungu anakulembera kale, ndipo atasonkhana kuti akuzunze ndi china chake, sangakwanitse kutero pokha pokha pachokhacho chimene Mulungu anakulembera kale kuti chikuzunze, zolembera zinanyamulidwa kale (zitalemba zimenezi), ndipo mapepala ake anauma”.(Tirmiz- 2516),

Ndipo muhadith ina mtumiki (saw) anati: “Umusunge Mulungu umupeza patsogolo pako, uzipangitse kuti udziwike kwa Mulungu (pogwira ntchito zabwino) pamene uli pa mtendere, Mulungu adzakudziwa pamene uli pamavuto (adzakuthandiza), ndipo dziwa kuti chomwe chakuphonya si chinali choti chikupeze, ndipo chomwe chakupeza sichinali choti chikuphonye, choncho dziwanso kuti chipulumutso chimadza kamba kopilira ndipo kufewetseredwa kuchipsinjo kumadza pambuyo povutika kaye, ndipo pamene pali zopweteka pamakhalanso zokoma”,(Ahmad- 2803), hadith ya mtumiki imeneyi imatengedwa kuti ndi gwero la maphunziro, ndipo muli ziongolero zabwino zochochera kwa mtumiki wolemekezeka (saw) kupita kwa anthu (ummah) ake onse za m’mene angamaonetsera chidwi pa kaleledwe kabwino ka ana awo pachukhulupiliro cholongosoka⁽⁹¹⁾.

2. Nzofunikira kwambiri kupewa kuilowa kwambiri limodzi ndi mwana nkhani ya chigamulo ndi chikonzero cha Mulungu pa msikhu umeneu, chifukwa zomwe mphunzitsi angathe kufikitsa kwa mwana pankhani imeneyi ndi monga izi:



- * kufotokoza momveka bwino kukula ndikuya kwa kuzindikira kwa Mulungu kuyambira kale,
- * kuti Mulungu ndi wakutha chilichonse ndipo wazungulira chilichonse,
- * kuti iye ndi Mlengi wachilichonse,
- * kuti iye ali ndikuthekera kwachina chilichonse chomwe wafuna.

Ngakhalekuti munthuyonsoanamupatsa ufulu wosankha ndi udindowokwan-ira pa ntchito zake zodzisankhira, akuyenera kudzalipidwa zabwino kapena ku- langidwa pazimenezi. Ndipomwana auzidwe izi mwachidule, koma ngati anawo atadzadzidwa ndi mafunso okhudza mutu umeneu, mphunzitsi azayenera ku- fotokoza m'mene angathere koma mwa mulingo wabwino womwe nzeru zam- wanayo zingathe kuitolera nkhaniyi (kuimvetsa).


3. Kumuphunzitsa mwana kuti azipempha kwa Mulungu osati kwa aliyense ayi, ndipo thandizo azipempha kwa Mulungu yekha, chifukwa Dua (pem- pho) iliyonse imayenera izilunjika kwa Mulunguwapamwamba mwamba kokha basi, aphunzitsidwe kuyedzamira mwa Mulungu yekha komanso ku- pilira pa chigamulo ndi chikonzero cha Mulungu.
4. Mwana aphunzitsidwenso kuti Mulungu safunira iye (mwanayo) kupatula zabwino zokha zokha, moti iye (mwana) alipanyengo yomwe Mulungu an- amuyikira iye kuti akhale padziko pano ndipo azikumana ndi zokhazo zom- we Mulungu anamukonzera, kotero moyo wake sungamakhale wobanika kapena wodandaula, ndipo azikhala wosangalatsidwa ndi chigamulo cha Mulungu akamakumana ndi zowawa (zokhoma), iye amakhulupilira ndi mtima wake wonse kuti: “Palibe chomwe chingatipeze kupatula chokhacho chimene Mulungu anatilemba” (Surat at Taubah: 51).
5. Aphunzitsidwenso kuti Mulungu wapamwamba mwamba ndi yemwe amayendetsa chilichonse, ndipo iye amapangachomwe wafuna ndiponso amasankha chomwe wafuna, chifukwa iye ali ndi ufulu wopanga chilichonse mu ufumu wake ndi pazomwe amazilamulira. Izi zidzapangitsa kuonjezera mgwirizano wake ndi mbuye wake ndikulunjika kwa iye pazilizonse, zotsati- ra zake adzakoleka malingaliro, mapemphero (madua) ndi chiyembekezo chake pa Mulunguyo.
6. Kukhulupilira za nsanamira imeneyi zimapangitsa mwana kukhala ndi mti- ma wosakondera ndi wodekha nthawi iliyonse yomwe wokhulupilira wadzi- wa kuti zonse zomwe zimamupeza (zabwino ndi zoipa) zonsezo zimakhala ndi ubwino paiye ndikuti palibe choipa champakana kale kale; zimenezi zimapangitsa mtima wa mwanayo kukhala wodekha ndi wokhazikika mkati mwake, izi zidzapangitsa iye kukumana ndi mavuto ake, zotopetsa zake ndi ziphinjo zake, ali ndi mtima wolandira chigamulo ndi chikonzero cha Mu- lungu, zotsatira zake amapereka zichito chito zake m'manja mwa Mulungu nakhala wodekha mu mtima ndim'maganizo momwe⁽⁹²⁾.

Yemwe angakhulupilire chikhonzero cha Mulungu samadandaula kapena kusowa chochita, ndipo sapsa mtima pamavuto kapena zikamugwera zok- homa koma m'malo mwake amazipereka kwa Mulungu namayembekezera malipiro abwino kuchokera kwa Mulungu ndipo akamugwera mavutowo

nthawi yomweyo amafulumira kutchula mau a Mulungu ngati m'mene akunenera mwini wake **“Choncho auze nkhani yabwino opilira, omwe mavuto akawapeza amati ndithudi ife nga Mulungu , ndipo kwa iyeyo ndiko tidzabwerera, otero ndi amene ali ndi madalitso ndi chifundo chochokera kwa mbuye wawo, ndiponso iwo ndi amene ali oongoka”**. (Surat Al Baqarah: 155- 157).

7. Tingathe kuthandizana pobweretsa zina mwa nthano komanso tinkhani tomwe tikuonetsa kuti anthu ake anapanikizika ndi chikonzero cha Mulungu pa iwo, ndipo pambuyo pake anapeza zabwino chifukwa cha chikonzero chimenechi, moti mpakana zinthu ndi nyengo kwa iwo zinasitha napita ku ubwino.
8. Chidule cha kukhulupilira muchikonzero cha Mulungu ndiko kukhulupilira kuti Mulungu amadziwa chilichonsempanda kupatula (in general) ndi mwatsatane tsatane (in detail). Ndithu iye analemba zomwe anazidziwa nkale mwa zinthu zomwe zidzachitike mtsogolo monse pazolengedwa zake kufikira tsiku lachiweruzo, zimenezi adazilemba mu lauhul-mahfudh ndikuti zochitika zonse sizingachitike pokha pokha Mulungu akafuna komanso akachipanga.





**CHIYAMBI CHA
KAYANKHIDWE
KAMAFUNSO**



Ndithu

Ndithu Namalenga mwini ulemele-
ro wonse adamulenga mwana kukhala
wokonda kufunsa mafunso; ndicholinga
choti athire mu nzeru zake mlingo wauku-
lu wa matanthuazo ndi maphunziro, ndi-
po msinkhu wa umwana umatchedwa
msinkhu wa mafunso, chifukwa zambi-
ri mwa zomwe mwana amakamba pa
msinkhu umeneu ndi mafunso.

Ndiye ana amadzizindikira kuti iwo sadziwa chilichonse chokhudza zitnhu zomwe zawazungulura, pa chifukwa choti umbuli umabweretsa mantha; ndithu anawo zimawakankhira ku maphunziro ndi kufuna kudziwa chilichonse pogwirit-sa mphamvu zake zonse, moti tipeza kuti mwana wa zaka zitatu amafunsa mako-lo ndi achibale ake akulu akulu milu yankhani nkhanu ya mafunso tsiku ndi tsiku, ndipo mosakaika mayankho awo pa mafunso amenewa amasintha chinachake mwa iwo, komanso amamunyamula iye kuchoka pamene ali ndikumuika pena, izi timazona kudzera mu kasinthidwe ka kafunsidwekake ndi mitu yomwe iku-fusidwa kawiri kawiri.

Ndithu inu mumakhala mukumva mau akubwerawa nthawi zambriri kuchokera kwa ana: nchiyani? chimapezeka kuti? chinasanduka bwanji? Chinachokera kuti? Nchiti? kodi mumadziwa? Ndithu iye amafuna kudziwa chilichonse chomwe chingabweretse chidwi chake (mwanayo), ndipo amafuna kumvetsa⁽⁹³⁾, zinthu zomwe amazona ndizomwe amazimva, iye atha kulimvetsa yankholo kapena ayi, angathenso kumvetsera mwachidwi kwa nthawi yokwanira kapena ayi?.

Ndithu mwana amadziwika ndi mtima wokonda kutulukira zinthu zachilen-do, ichi chimatha kuonjezereka malinga ndi nyengo yomwe mwanayo akukha-la, komanso malinga ndi mipata (mwayi) yomwe iye akupatsidwa, pa chifukwa ichi; ndithu ife timakhala odabwa tikayerekeza mafunso athu pamene tinali ana ndimafunso omwe anawo akufunsa panopa; malinga ndi kusiyana kwa nthawi, malo komanso kupita kutsogolo kwa maphunziro, ndipo mosakaika njira yaka-phunzitsidwe yomwe aphunzitsi amagwiritsa ntchito imasintha china chake moonekera makamaka popititsa patsogolo mafunso a ana kapena kuchepet-sa (mafunso), moti mphunzitsi amapereka mpata kwa mwana namalandira mwa nsangala mafunso omwe ana akufunsa, (mphunzitsi) yemwe samatha nkuyankha komwe mafunso a ana namakana kuyankha kapena kumawayankha mwaukali ana sangamufunse iye funso lililonse⁽⁹⁴⁾, ngakhale kuti tonsefe tima-vomereza kuti sizikufunika kuti mwana adziwe chilichonse ayi, koma kuti chomwe chikufunika kwambiri ndichoti asamaope kufunsa zina mwazithu zomwe zimachitika pa umoyo wake, ndipo chithu china chofunikiranso ndi chakutianawo samaona kuti tikuwasala kapena kuti sitimawakhulupira.

Ndipo chofunikira kwambiri kuposa zonsezi ndi ichi: ana aziona kuti iwo ali ndi kuthekera kothandizira maganizo akamalankhulana ndi anthu apa banja lake⁽⁹⁵⁾.

ZIFUKWA ZOMWE ZIMAPANGITSA ANA KUKHALA NDI MAFUNSO OCHULUKA



Nzotheka kuzitchula zifukwa zomwe zili zofunikira kwambiri zomwe zimapangitsa mwana kufunsa mafunso mochuluka motere:

1. Kufunitsitsa kwa mwana kuti azitulukire zithu zachilendo ngati njira yokwaniritsa zofuna zamsinkhu wake komanso nzeru zake.
2. Khumbokhumbo lomwe ana amakhala nalo lofuna kuchimvetsa chilihonse chomwe chamuzungulira monga maonekedwe a zinthu ndi zinthu zenizenizo.
3. Ana amakhala obanika ndi amantha pa zinthu, izi zimachitika kamba koti iye amakhala kuti sankachidziwitsitsa icho mmbuyo monsemu, mwachitsanzo: mwana amatha kuopa zinyama angakhale zomwe sizingamupange upandu uliwonse, pachifukwa chimenechi mwana amafunsa mafunso ochuluka kuti apeze mtendere ku izo.
4. Kuonjezereka kwa kuthekera kwake pa chilankhulo, mwana akamalu-mikiza mafunso – lina pambuyo pa linzake-; sikuti kumakhala kufunitsitsa kupeza yankho ayi, koma ndi khumbo khumbo lake lofuna kuyesetsa kuyankhula ndi kuwawalira anzake kuthekera kumeneko, komanso kufuna kutenga mbali pa zochita za anthu a ku deralo.
5. Kuonetsa kukhuzidwa ndi mpata womwe wapezeka wokambirana ndi kuthandizana pakati pa makolo ndi ana.
6. Kukamaonjezereka kudalira kwa mwanayo pa iye mwini ndi pa makolo ake, komanso kuonjezereka kwa kudzilemekeza kwa iye mwini⁽⁹⁶⁾.

CHIBADWA CHA MAFUNSO A ANA



Kuti tithe kuwamvetsa bwino mafunso a ana: tikuyenera kusiyanyitsa pakati pa mafunso a nzeru ndi a chiyanikhulo, ndi pakati pamafunso a umoyo; chifukwa pa mtundu wamafunso woyambawo mwana amafunitsitsa kudziwa kapena kuuzidwa zachithu china chake, pomwe pa mtundu wachiwiriwo iye amangofuna kupenza chomwe chingapangitse kudekhetsa mtima wake, osati yankho leni lenilo ayi, moti chimene amafuna mwana ndi kumuzindikiritsa choonadi chachikulu chomwe ndi: cholinga chenicheni chomwe mafunsowo abwelera (chomwe chapangitsa kuti wofunsayo afunse), ndipo ife sitingathe kudziwa zonse zofunikira mufunsolo, kapena kulimvetsetsa bwino bwino ndi kuzindikira zonse zomwe funsolo likufunsa, pokha pokha kudzera mukudziwa zomwe zapangitsa mwanayo kuti afunse funsolo, moti funso pa lokha silingapereke matanthauzo onse omwe akufunika, koma kudzera munyengo yomwe yamuzungulira mwanayo ndi zomwe zimapangitsa kuti afunse, tigathe kudziwa matanthauzo ake onse, zofuna zake komanso kufunikira kwake (kwa funsolo). Ndithu mafunso a ana amagwira ntchito zitatu zofunikira pomukonza mwanayo, ntchito zake ndi izi:

1. Kukwaniritsa kulungama kwa mtima wa mwana, mafunso ambiri amwana amawatenga kuchokera mu mtima (m'mene akumvera mumtima mwake).
2. Kuganiza mwa mfundo; chifukwa mwana amayetsetsa kudziwa zachilendo, pogwiritsa ntchito zomwe akudziwa, amathanso kudziwira zomwe samazidziwa kapena kulumikizira ndi zina (zomwe amazidziwa kale).
3. Kudziwa zinthu zomwe zamuzungulira ndi zinthu zina zofunikira kwambiri pa umoyo; monga kudziwa zikhalidwe ndi miyambo komanso zichitochito zomwe zimapezeka mu zikhalidwe za anthuzamdera lomwe mwanayo akukhala⁽⁹⁷⁾.

MITUNDU YA MAFUNSO A ANA



Nzofunikira kwambiri kuti tiyesetse kuwagawa mmagulu mafunso omwe ana amakonda kufunsa, chifukwa mayankho ake amakhala osiyana malinga ndikusi-yana kwa maguluwa, ndipo tingawagawe motere:

1. Mafunso okhudza chiyankhulo monga: chifukwa chiyani zinthu izi zi-matchedwa ndi maina amenewa? Chifukwa ninji sitimasitha maina amene-wa? Chifukwa chiyani sitimapeka chiyankhulo china.
2. Mafunso okhudza kupezeka kwa zinthu monga: kodi tinachokera kuti? Nan-ga tikupita kuti? Kodi ana amachokera kuti? Kodi imfa ndi chiyani? Tandilon-gosolereni zokhudza dzikoli? ndi mafunso ena otero.
3. Mafunso oukira: mafunso oterewa amazungulira pakuti: chifukwa chi-yani ana saloledwa kulowelera nkhani za akulu akulu? Mafunso obwera mosonyeza kuyesera kukhala ngati akulu akulu- nthawi zambiri- kudzera m'mafunso.
4. Mafunso oyesa (amayeso): awa ndi mafunso omwe ana amafunsa ndi chol-inga chofuna kuyesa kuthekera komwe ofunsidwawo ali nako, komanso ndi cholinga choti adzudzule kufooka komwe angakupeze pa ofunsidwawo, izi zimakonda kuchitika kawiri kawiri pofuna kuwayerekeza ofunsidwawo ndi akatswiri ena omwe anawo akuwadziwa kapena amene amawakonda, ndi-po nthawi zambiri mafunso amenewa amazungulira pa kuthekera kwa an-thu ndi chuma komanso kwathupi lokha.

5. Mafunso osonyeza kubanika kwa umwana: nthawi zambiri ana amafunsa mafunso ofuna kuchotsa kubanika komwe kukupezeka mwa iwowo, ndipo ambiri mwa mafunso osonyeza kubanika omwe amawapezapeza ana ndi: okhudza kusowa kwa mmodzi mwa makolo awiri, kapena mitundu ina yakunyanyalitsana.
6. Mafunso ofuna kudziwa zinsinsi za thupi: ndipo oyambilira mwa mafunso amenewa amakhala okhudza kusiyana kumene kuli pakati pa thupi la mwamuna ndi mkazi.

Kugawa mitundu ndi magulu amafunso kumeneku kungathandize wofunsidwayo kudziwa chomwe chapangitsa anawo kuti afunse mafunsowo, chifukwa iwo safunsa funso chabe ayi, koma kuti pamakhala chomwe akufuna achimvetse m'moyo wawo⁽⁹⁸⁾.

CHIFUKWA CHIYANIMAKOLO ENA SALABADIRAMAFUNSO A ANA?

Ndithu kusalabadira mafunso a ana, nthawi zina kumachitika chifukwa chakunyansidwa kapena kusakhutitsidwa ndi mafunsowo, nthawi zina zimachitika chifukwa cha kusadziwa yankho ndi kufunikira kwa funsolo, kapena kusadziwa ntchito yomwe funsolo lingagwire mumtima wa wofunsayo kapena kumbali ya maphunziro, koma zimachitika kamba ka zifukwa zina, ndipo zofunika kwambiri mwa izo ndi monga:

1. Wamkulu akaona kuti funso la mwanalo ndi lodabwitsa, kapena lopanda pake, kapena mwanayo akupanga zamacheza, izi zimapangitsa wofunsidwayo kuti asalabadire funsolo kapena kulikhalira tcheru; kotero akulu akulu amakhala akuwaphwanyira ana ufulu woganiza kudzera mu njira yawo yosazungulira ndi yomveka bwino yogwirizana ndi umwana wawo, ndiye kuwaphwanyira ufulu kumeneku akulu akulu amakutenga ngati chida chawo cha nzeru, kuiwala kuti mwana amafunsa funso lophweka komanso lopanda milandu, mkati mwake muli cholinga chofuna kuzindikira kapena kudziwa chilengedwe chomwe chamuzungulira kuphatikiza apo cholinga cha mumtima mwake chomwe chapangitsa kuti afunse chomwe akufuna kupeza pompompo, chomwe chili kubwezeretsa mtima wake m'malo mwake womwe unasuntha kanthawi kena kake.
2. Akulu akulu akadziwa kuti funso lomwe mwanayo wafunsa ndi lovuta; makamaka kuti likakhala funsolokuti ndi lokhudza mbali ina ya zinthu zolletsedwa kudelarokapena kumakhalidwe achikhalidwe china chake, moti silikufunika kuliyanika kufikira atafika msikhu wina wake. Ndiye kuvuta ndikukolana kwa mafunso a ana kumeneku kumapangitsa akulu akulu kuso-
wa choyankha. Pachifukwa chimenechi akulu akulu akuyenera kudzikonz-

keretsa okha mokwanira kuti azitha kuyankha moyenera mafunso ngati amenewa.

3. Nthawi zina kuchuluka ndi kubwera mwakathithi kwa mafunso kumapan-gitsanso akulu akulu kusawalabadira mafunsowo. Koma akadakhala kuti akulu akulu amakhala akudziwa zakufunikira kwa mafunso amenewa iwo sakadatero, m'malo mwake iwo akadawalimbikitsanso anawo kuti apitilize kufunsa mafunso awo, bwenzinso anawo akuganiza mwaubwino.
4. Chinanso chomwe chimawapangitsa akulu akulu kuti asacheukire kape-na asalabadire mafunso a ana ndi chakuti mafunso a ana ena samakhala achindunji.
5. Kuthekanso makolo kuthawa mafunso a ana akakhala kuti sakudziwa zom-we anawo akufuna kudziwazo. Nde tikuwauza makolo otere kuti; muku-yenera kufufuza mayankho amafunso a ana anu komanso muwafotokoz-ere mayankho mosawabisira komanso mosawanamiza⁽⁹⁹⁾.
6. Zikakhalakuti zomwe anawo akufunsa ndi zopitilira msinkhu wa nzeru zawo kotero kuti mayankho ake angafune kusanthula kwa pamwamba ndi kovuta, zikatero makolo amayamba kuganiza kuti kodi mwana ameneyu walipeza kuti funso limeneli⁽¹⁰⁰⁾, kenako amalisiya funsolo osaliyankha.

KODI MAKOLO ANGAKWANITSE BWANJI kuyankha MAFUNSO A ANA?

Ndithu nzoyenera kwa makolo kupereka mayankho olondola amafunso a ana. Komanso akuyenera kukonza njira zosiyana siyana zamikambirano zokhudza mafunso a ana pankhani ya chikhulupiliro, namawathandiza anawo kuti azi-lankhula maganizo awo okhudza chipembedzo, ndicholinga choti ayike mwaiwo kukhazikika ndi kukhutitsidwa, komanso kuzindikira kolondola pa chipembedzo, zomwe zingateteze chipembedzo chawo cholondola komanso chosapunguka kapena kupyola muyeso⁽¹⁰¹⁾. Sikuti makolo akukakamizidwa kuzindikira mayankho amafunso onseolondola a ana pa chipembedzo ayi, koma kuwalongosolera anawo momveka bwino msanamira za chikhulupiliro kuti akule ali pa chikhu-lupiliro champhamvu mwa Mulungu⁽¹⁰²⁾, ndipo ndibwino kumuuza mwana wamkulu mwaiwo kuti azilemba mafunso a mwana, ndipo nchapafupi kwa iye kuulandira udindo umenewu, makamaka akaona chidwi ndichilimbikitso, ndipo anawo adzaona kuti zimenezi ndi zosangalatsa kwa iwo.

Komanso kumbali ina timakhala tikudzala mwa ana akulu akulu kufunikira kwa funso lililonse, ndikutinso mafunsowa amapereka ulemelero ndi udindo, chon-cho iwo amafunsa, komanso timadzala mwa iwo chidwi pa mafunso a ana awo mtsogolo akadzakhalak makolo.



Kumbali inanso: timakhala ndi mulu wa mafunso omwe angatithandize kufu-fuza mayankho ake, komanso angathandize kudziwa mafunso omwe abale ndi azilongo awo adzidzafunsa pambuyo pake nakozekeerera chile. Mwana adzakh-ala wosangalala tikamadzampatsa yakho la zomwe amafunsa mmbuyomu, ndikuonetsa chidwi chofuna kumpatsa yankho la bwino la mafunso ake, kud-zasintha mwa iye chinthu chachikulu - Mulungu akaloleza kuteru -, komanso mg-wirizano wathu ndi iye udzapita patsogolo, ndipo mwana ameneyu adzawatenga makolo ake ngati gwero loyamba ndi lodalilika la maphunziro ake muzaka zili mkudza m'malo motenga maphunziro ake kuchokera m'malo okaikitsa makam-aka akadzakula⁽¹⁰³⁾.

Apa pali mfundo yoyenera kuti makolo achenjere nayo, yomwe ndi: kufunika kosiyanitsa pakati pa mitundu iwiri ya mafunso;

- **Mtunduwoyamba:** mafunso ofunikira kwambiri omwe mwanayo aku-mawabwereza bwereza, atha kufunsa kwa anthu angapo m'banjamo, ndi-po mafunso amenewa amathanso kutulutsa mafunso ena.
- **Mtunduwachiwiri:** mafunso osafunikira kwambiri, omwe titati tiyambe kukambirana naye mwanayo nkhani Ina yakeangathe kuliyiwala funso-lo, komabe tiyesetse kuliyankha, kapena kumufufuzira yankho kapena kumpatsa munthu yemwe angayankhe bwino funsolo, mukutero muli ku-konzekera maphunziro ndi kufunikira kwake. Pomwe mafunso osafunikira kwambiri aja; palibe kathu kuwasiya makamaka akakhala okhudzazinthu zoti yankho lake sangathe kulitolera mwanayo.

MAZIKO OKUTHANDIZIRA KUYANKHA MAFUNSO A ANA



Pali maziko ndi miyambo ingapo yoyenera kwa makolo kuigwiritsa ntchito ndi kuilingalira poyankha mafunso a ana, ena mwaiwo ndi awa:

1. Kulemekeza: makolo omwe amatchera khutu kumvetsera mafunso a mwanamapangitsa mwanayo kuchimva mu mtima mwake kuti makolowo nawonso amalemekeza ndi kukhudzidwa ndi mavuto amwanayo limodzi naye, kuthandizana naye kumeneku kumampatsa mwanayu kukhazikika kwa mtima ndi kulongosoka kwake pakutero mwana amadzidalira yekha mwachangu, ndikukhala wosamala pofunsa mafunso komanso kusanja nfundopolankhula pamene akukambirana.
2. Kudalira komanso chitetezo; makolo ayesetse kuyankha mafunso a ana awo mwakuya pogwiritsa ntchito mau odziwika ndi ozolowereka kwa anawo, komanso pofewetsa zomwe akuwauza anazo mogwirizana ndi dongosolo la maphunziro abwino. Ndithu zoti yankho linali loona zimaonekera kumape-to kukapezeka kukhazikika kwa mtima.
3. Kuthetsa zomwe zimapangitsa mwanayo kufunsa; makamaka zomupangit-sa zake zikuchokera mu zomwe zikumuchitikira kapena komwe akukhala, mwachitsanzo: mwana yemwe akumva kubanika ndi kusokonezeka chifuk-wa cha kubadwa mwana watsopano m'banjamo amatha kufunsa kuti: kodi ana amachokera kuti? Sizingatheke kumuthetsera vuto lakeli pongomuy-ankha zomwe ukudziwa ayi, koma pakufunika kumuthandizira pakuphwet-sa chomwe chamupangitsa kuti afunse funso loteleri, ndikuonetisa chidwi chapaderapazimenezi⁽¹⁰⁴⁾

Ndithu chinthu chapamwamba chomwe akulu akulu angapereke kwa ach-ichepere ndiko kuwathandizira kuwalitsa nzeru zawo, osati kumangowakambi-ra nkhani ndi nthano komanso osati kudzera muzikhalidwe zolondola zokha ayi, komakudzera mukuwaphunzitsa kuganiza ndikuwapatsa mitu yoti alingalire, ndikuwazoloweretsa kuti asamakhutitsidwe ndi zinthu zoonekera ndi zapam-wamba zokha ayi, koma kuwapangitsa kuti aziganiziranso koposera pazimen-ezo⁽¹⁰⁵⁾, ndipo pakufunika kulolerana mwaubwino ndi mkambirano womanga komanso wokhala ndi masomphenya ndi kuthandizana pamaganizo⁽¹⁰⁶⁾, ndipo makolo akuyenera kuwafunsa anawo mafunso omwe angawapangitse anawo kulingalira.

Tingathenso kugwiritsa ntchito yankho la mafunso mwaluntha, makolo apempho mwana kapena kumupatsa mwana ganizo lofunsa funso lake pa mkumano wapa banja lonse, kenako makolo apereke mwayi woyankha funsolokwa onse, funsola likakhala funso wamba kapena si la tcheru, koma chofunika kwambiri kuonesetsa kuti mwanayo asapatsidwe chitozo kuchokera kwa mkulu wake chifukwa chakulephera kufunsa funso labwino (kufoila), koma ngati zitachitika zote-rozo, khola lidzayenera kuimira mbali ya mwanayo kwinaku akumuchemerera chifukwa chachangamu chake chofunsa funso ndi kufunikira kwa aliyense kofunsa mafunso, ndi mowakumbutsa mau aMulungu onena kuti: **“Ndipo kuzindikira komwe mwapatsidwa ndi kochepazedi”**.(Surat Al Isra: 85).

Ndipo kudzera mu kuyankhana mafunso pagulu kumakwanilitsa zolinga zomwe zimakwanilitsidwa kudzera m’mafunso a mwana.



KUPHUNZITSA pogwiritsa ntchito nKAMBIRANO



Ndithu njira yoyenera yamaphunziro kwa ana ndi njira yokambirana yomwe imatheka kudzera mu kukambirana mafunso ndi mayankho; chifukwa njira imeneyi imathandiza kutsegula kapena kutakasula lilime ndikupeza luso lodzapangira maphunziro, ndiye kukambirana ndi kumene kumayandikitsa luso limeneli ndi kupezeketsa zolinga zake⁽¹⁰⁷⁾, ndipo nthawi yamkambiranoyi mwana akuyenera kulemekezedwa, ichi chidzachotsa mwa mwana mantha, maganizo, kubanika komanso matenda amu mtima monga kuponderezedwa ndi kusolidwa, mwana akamamva mpumulo wa mu mtima panthawi yokambirana, amachotsa mantha, matenda ndi zotopetsa zomwe zili mu mtima mwake, magulu onse awiri akapeza zifukwa zavuto nalankhulana aliyense mosapsatira kapena mosaphiphiritsa zakukhosi kwake, zikatero kuthetsa vuto kumakhala kosavuta, chimodzi modzinso kupambana kumakhala kosavuta⁽¹⁰⁸⁾.

Ndithu kukambirana kwa pakati pa mwana ndi makolo ake zimabweretsam’banjamo maubwino monga:

- I. Kuzindikira; kotero mwana amaziandikitsa chifupi kwambiri kwa anthu ena am’banjalo.
- II. Chiyanjano; kukambirana kumaonjezera chiyanjano pakati pa anthu am’banja limodzi, ndipo amakondana komanso amayandikirana kwambiri.
- III. Kufewerana mtima; tikutanthauza kuti sitimakambirana ndi cholinga chongofuna kukwaniritsa chomwe tidakhazikitsa (zoti tizikambirana) kokha ayi, koma timafuna kukwanilitsa tanthauzo leni leni la kukambirana, lomwe ndi kugwiritsa ntchito liwu lokoma ndi nyengo yoyenera⁽¹⁰⁹⁾.

Kuchokera muzimene talongosolazi tikupeza kuti kuphunzitsa pogwiritsa ntchito kukambirana kuli ndi maubwino awa:

1. Kumpatsa mwana ufulu woganizira ndi kuzitulukira zachilendo paiye yekha, pakutero zimamulimbikitsa iye kuyambitsa zamakono ndikukweza umunthu wake.
2. Nkophweka kuphunzira mu njira imeneyi chifukwa simafuna zambiri, ndipo mwana amakwanitsa mwa mtima m’malo ndimosayalutsidwa.

3. Kumalowetsa m'mitima ya ana nsangala ndi kudzimva kuti iyeyonso payekha ndi wokwanira, komanso zimawaphunzitsa anawo kuwamvetsera ena akamalankhula.
4. Kumapereka mpata woganizira ndi kufufuza mwa iye yekha, moti amaona zinthu mukaonekedwe kosiyana siyana, ndipo kumamuzoloweretsa kuganiza mwa mfundo zomveka ndi za ndondomeko (logic).
5. Kumadzutsa chidwi (attention) pa mwanayo ndikuchotsa pa iye kubalalika ndi kubhoweka, ndipo zimampangitsa kukhala ndi chidwi ndi kutenga mbali kapena kuchitapo kathu⁽¹¹⁰⁾.

CHITHUNZITHUNZI CHA MAFUNSO A PA MKAMBIRANO



Pali kabweredwe kochuluka ka mafunso omwe tingathe kuwafunsa ana, monga:

- a) (Chikuchitika nchiyani?), kafunsidwe aka kamapangitsa mwana kufufuza pa zomwe zamuzungulira, kotero izi zidzamuthandiza iye kuzilongosola mwa chidunji zinthu zomwe zamuzungulira.
- b) (Ukufuna chiyani?), funso ili limathandiza kudziwa cheni cheni chimene aku-funitsitsa.
- c) (Umapanga bwanji chimenechi?), funso lotere limathandiza mwanayo kuti aziganiza mwa ufulu kapena kuti momasuka, komanso limalimbikitsa maganizo ofufuza yankho lake.
- d) (Chifukwa chiyani zimachitika zoterezi?), funso ili limamuthandiza mwanayo kupitiliza pazinthu zooneka ndi kumafufuza zifukwa zake, choncho amayamba kusanthula ndi kufufuza mgwirizano wa pakati pa zinthu.
- e) (Zikadzattere tidzatani?), funsolotere limamuthandiza mwana uja kuganiza kachikenanso ndi kusinkha sinkha mwanjira zosiyana siyana pazochita.

Mafunso ofunsa mwana alipo amitundu yosiyana siyana, koma kuti mafunso abwino omwe amabala zipatso zofunika pamaphunziro ankambirano ndi ana akufunika akhale ndi zinthu izi:

1. Funso likhale lalifupi bwino m'mene ungathere.
2. Likhale lomveka bwino ndi la chindunji lokamba ganizo limodzi.
3. Likhale loyenera ndi msinkhu wa mwana, nthawi, malo ndi nyengo yomwe mwanayo akukhala.
4. Yankho lake likhale loti ndi lolondola komanso lolakwika munthawi yomweyo, koma likhale funso lomwe lingagwedeze ndi kutakasula nzeru za mwanayo, moti likhale lomampatsa mwanayo nthawi yosinkha sinkha⁽¹¹¹⁾.



NJIRA ZOYANKHIRA MAFUNSO A ANA



Takamba kale mmbuyomu mitundu ndi kabweredwe ka mafunso a ana, pano tsopano tikambe zokhudza mayankho, poti pali njira zambiri mbiri zoyankhira mafunso a ana potengera nthawi ndi malo komanso nyengo yomwe funsola lafunsidwira, ndipo zodziwika bwino mwanjira zimenezi ndi izi:



1. Kuyankha pakamwa pompo pompo mwa chindunji, uwu ndi mtundu umodzi mwa mitundu yomwe ili yodziwika kwambiri yoyankhira mafunso, moti mwana amafunsa mafunso ndipo woyankha amayankha kapena kupereka yankho la pakamwa pompopompo, ndipo kawiri kawiri yankho limeneri limakhala lachangu ndi lachidule.
2. Kupereka yankho kudzera mukukamba ka nkhani kakafupi; iyi simakhala njira yachindunji poyankha mafunso, ndipo nkhaniyo imakhala yogwirizana kwambiri ndifunso lomwe lafunsidwalo, ndipo nthawi zambiri ana amakonda mtundu wakayankhidwe umeneu ndipo amamvetsera mwachidwi kwambiri.
3. Kuyankha mojambula; nthawi zina mwana amafunsa funso lomwe kuyankha kwake kumafunikira kugwiritsa ntchito zithunzi zoti ziwalitse yankholo, monga mafunso odziwira zinthu chifukwa zithunzizimagwira ntchito yaikulu komanso yodalilika kwambiri podziwira zinthu, makamaka zikakhala zithunzi za mitundu mitundu ndi zachikoka.
4. Kuyankha pogwiritsa ntchito kuona; zimatheka mwana kufunsa funso lomwe kuyankha kwake kungafunike kugwira ntchito yotengana ndi mwanayo kupita kumalo ayankholo; kuti akadzionere yekha ndi maso ake ndikupeza yankholo mwa iye yekha, monga yankho la funso lokhudza zinyama za kuderalo, nanga zimakhala bwanji? Ndipo zimadya chiyani? Nanga zimberekana bwanji⁽¹¹²⁾.

MALANGIZO OYENERA KUWATSATIRA NTHAWI YOYANKHA MAFUNSO



1. Uyetsetse kuti mwanayo akhutitsidwe pogwiritsa ntchito kukambirana ndi mafunso, komanso osamangodalira njira ya kumuuza yankho ayi, ndipo pamapeto pake tikuyenera kuonetsetsa kuti mwanayo wakhutitsidwa nalo yankholo komanso wasangalatsidwa nalo.
2. Unene zoona payankho lako ndipo usamunamize mwana wako, chifukwa chakuvuta kwa funso, ndipo uyetsetse kupewa kumpatsa mwana maphunziro olakwika- muli monse zingakhalire -, yankho lako likakhala loona zot-satira zake mwana amakudalira kwambiri.
3. Uyetsetse kufewetsa yankho lako kuti limveke mosavuta molingana ndi nzeru za mwanayo, ndipo upewe kukhwimitsa kosokoneza (kobalalitsa) nako nzeru za mwanayo, komanso upewe kumupatsa maphunziro opun-guka, ponena kutimwanayo sanakule kotero sangakwanitse kumvetsa bwino bwino, chifukwa maphunziro amayenera kukhazikika mu nzeru za mwanayo⁽¹¹³⁾.
4. Usamutenge mwana wako ngati wozerezeka, chifukwa iye angathe kum-vetsa zomwe ukufuna kumuphunzitsa ngati mungasankhe njira yabwino, ndipo uyetsetse kuyankha funsolo mwachindunji ndi mosakhotetsa, ku-pangira kuti mwana angatuluke mu nkhani yomwe ikunenedwa.
5. Usamadzudzule momuyalutsa kapena kumunyoza pafunso lake muli monse m'mene lingakhalire, koma muonetsereni nthawi zonse kuti ndi-nu okonzeka kumuyankha mafunso ake⁽¹¹⁴⁾, chifukwa mnyozo umapangitsa mwanayo kudzimva kuti iye ndi wosakwanira moti samadzidalira pa iye yekha ndipo zimapangitsa kuti asamakonde kufufuza.
6. Osabanika ndi mafunso amwana okhudza Mlengi, ndi kusadziwa kwake zakupezeka mlengi, ndipo usathawe kumuyankha mwanayo; chifukwa ku-tero kudzampangitsa iye kukafufuza yankholo kwina (komwe mwina ndi kosayenera).

7. Usazengereze kumuuza mwana kuti adikire kuti ufufuze yankho, kuti uoneke ngati munthu ofufuza maphunziro ndi bwino kusi yana ndikuti uoneke ngati munthu wongozitcha kuti ndi wozindikira koma ulimbuli, si-chochititsa manyazi kumuuza mwana wako kuti dikira ndikufufuzire yankho lolondola⁽¹¹⁵⁾.
8. Uzilandira mafunso a ana mwachidwi ndi motchera khutu bwino ndipo usamazengereze kapena kusawalabadira ndithu kuwafungatira ndi kuwa-kumbatira ana ako ndi mtima wako moonekera, zimenezi zimamuthandiza iye kwambiri kuti alandire kulongosola kwako pa zinthu zomwe zimamuvuta kumvetsa⁽¹¹⁶⁾.
9. Ukakhala kuti watangwanikadi muuze mwanayo mwa mtendere kuti nthawi imeneyo simukwanitsa kumuyankha mafunso ake chifukwa sinthawi yoyenera, komabe uyetsitse kumuyankha mwachangu ukamaliza kutangwanikako.
10. Upewe kufotokozero, kutalikitsa ndi kutambasula kopanda pake komanso kosafunikira. Mayankho a mafunso a mwana wa zaka zisanu ndi chimodzi amafunika akhale ofupikirako poyerekeza ndi mayankho amafunso a mwana wa zaka khumi kapena kupitilira, zimenezi makamaka pa mafunso omwe amafuna kuyankha motambasula ndi kupereka maumboni – ngati mmene zimakhallira pa mafunso okhudza zinthu zobisika ndi mafunso ena omwe amakhala ovuta -, pomwe mafunso ena mayankho ake amakhala odziwika, omwenso amatheka kuperekedwa ku misinkhu yonse ya ana⁽¹¹⁷⁾.
11. Uzilumikiza mayankho a mafunsowo ndi zinthu zochitika zomwe mwana amazidziwa ndi kuzimvetsa bwino, ndipo upewe zinthu wamba zomwe zimavuta kuzimvetsa pa nsinkhu umenewu; ndipo uyesitse kumupatsa mayankhowo maumboni akapezeka pofuna kutsindika maphunzirowo pa mwanayo, ndipo yankholo likhale la nzeru ndi logwira mtima (logic)⁽¹¹⁸⁾.
12. Kugwirizana makolo onse pa maphunziro omupatsa mwanayo, tikutanthauza osatsutsana maganizo pomupatsa mwana maphunziro.
13. Osayankha funso la mwana ndi funso linzake, monga bambo kuyankha funso ponena kuti: “mukutanthauza chiyani?”, apa mwana amakhumudwa poona kuti sanakwanitse kufikitsa funso lake kwa bambo ake, chifukwa mwana amakhulupilira kuti makolo amayenera kumva zonena za mwana wawo popanda kufotokozero, choncho kholo likafuna kumvetsa funso la mwana wake, ndibwino kugwiritsa ntchito chiganizo chobwereza zomwe mwanayo wanena, monga: “ukutanthauza zakuti zakuti?”.

- 14.** Asadzikundikire okha (makolowo)ganizo pomuyankha mwanayo funso lina lake, chifukwa mwanayo akadzapeza yankholo kuchokera kwa anthu ena koma nakhala kuti likusemphana ndi lamakolo lija, panthawi imeneyi padzafunika kumupatsa mwanayo yankho logwira mtima ndi lolondola mwa njira yachidule lomwe lingapangitse mwanayo kudalira makolo ake-wo osati kudalira anthu enawo ayi ⁽¹¹⁹⁾.
- 15.** Uyesetse kukambitsana osati kumangolongosola wekha ayi, ndipo uzichu-lutsa kupereka zitsanzo ndi kukamba tinkhani, komanso kugwiritsa ntchito mabuku omwe amakhala ndi maphunziro ochuluka kwambiri okhala ndi zithunzi (encyclopedia) ⁽¹²⁰⁾, ncholinga choti afikitse kumvetsetsa tanthau-zolo munzeru za mwanayo, ndipo uyesetse kugwiritsa ntchito masewero a thupi, sewero, kujambula, kuganizira, kuimba/kulakatula, mafunso oten-thetsa ubongo akudula ndikumata, kujambula ndi kamera, ndi zina zote-ro⁽¹²¹⁾, ndithu kusinthasintha kumamanga ndi kupititsa patsogolo kugan-iza kwa mwanayo komanso kumapangitsa maphunziro kukhazikika mwa mwanayo.
- 16.** Mafunso ena sangatheke kuyankhidwa pakamodzi, koma pangonopan-gono mwandondomeko, akamafunsa zochuluka ma-yankhonso amaonjezereka molingana ndi nsinkhu wake, mtundu wa mafunso ake ndi mlingo wa kumvetsa kwake⁽¹²²⁾.



- 17.** Mwana akamakula mpaka kufika potha nsinkhu, zimakhala bwino kumamufunsa maganizo ake poyamba ndi zomwe wafunsazo, nde timamufunsa iyeyo funso lakelo, kuti tiwone mmene angachitire ndi funsolo, kudzera mmene angachitire ndi funso lakelo tingathe kuyamba kumuyankhano, ndipo tisayerekeze kumupanga mwana kuti aziganiza mofanana ndi mmene ife timaganizira; chifukwa zimenezo zidzamuyika mwanayo pa mlingo wosakhala wake ⁽¹²³⁾.

ZOLAKWIKWA PA MAPHUNZIRO POYANKHA MAFUNSO



- Kusalabadira mitundu ina ya maphunziro yosiyana siyana; pali mbali zina za maphunziro monga mbali ya chikhulupiriro, ya makhaliidwe, yongodziwira zinthu (academic), choncho kukakamira mtundu umodzi nasiya mtundu wina, kapena kusatenga mitundu yonseyo mwa mlingo wofanana, kusaphunzitsa mwandondomeko, komanso kuchulutsa

kumudzudzula ndi kumukalipira mwana chifukwa chakuti china chake chikumuuvuta, komanso kukonda kumangolankhula tokha pophunzitsa osakambirana ndi ophunzira, kufulumira pophunzitsa, kusazilondalonda zomwe waphunzitsa kwa ana, komanso kusamveka bwino pophunzitsa ndi polangiza, komanso kusmphana pakati pa zolankhula ndi zichitochito zathu, kupereka uthenga wosayenera ndi wopanda phindu⁽¹²⁴⁾,

zonsezi ndi zolakwika zomwe zimaononga ma phunziro ndi chikhulupiriro mumtima ndi mmaganizo mwa mwana

**ZITSANZO
ZA MMENE
TINGAYANKHIRE
MAFUNSO A
ANA OKHUDZA
CHIKHULUPIIRO**



Ndithu

Ndithu mayankho omwe abwera mu gawo ili choyambirira akulunjika kwa makolo ndi aliyense yemwe amakhala akuyankha mafunso a ana , monga aphunzitsi , alangizi , oyanganira maphunziro ndi onse oyanjanitsa anthu, amenewa tikuwapempha kuti awasanje ndi kuwaumba mayankho amenewa molingana ndi misinkhu, maphunziro ndi kuthekera kwa nzeru za mwanayo, chifukwa ife sitingakwanitse kuika yankho limodzi loyenera ana a misinkhu yonse yosiyana siyana pa zaka, nzeru ndi kuthekera , pachifukwa ichi, chimene chimakhala chofunikira kwa ife ndi yankho lenilenilo osati mau a yankho wo ayi⁽¹²⁵⁾, komanso tikuyenera kumasinthasintha kayankhulidwe ka yankholo pakati pa kuyankha mwachindunji ndi mopanda chindunji; ndi cholinga choti tipereke mlingo waukulu wa chithunzithunzi kwa wowerenga, ndipo iye malinga ndi udindo ndi ntchito yake atenga chenicheni cha mayankho amenewa nabwerezeka kasanjidwe ndi kaumbidwe kake molingana ndi njira yomwe ili yoyenera ndiyapamwamba komanso yabwino kwambiri kwa mwana wake.

Ndipo pofuna kuyankha mafunso a mwana okhudza chikhulupiro, makolo akuyenera kukhala ndi mlingo wokwanira wa maphunziro a chipembedzo wow-
aloleza iwo kupereka matanthauzo oyambirira omwe angawafotokozere ana awo
zinthu zobisika mwa njira yolingana ndi nzeru ndi kuthekera kwa anawo, ndipo
zovuta zomwe a zamaphunziro amakumana nazo si kusonkhanitsa maphunziro
kokha ayi, koma kuwaika (maphunzirowo) mukakhaliidwe kotu nzeru za anawo
zithe kuwalandira ndi kuwamvetsetsa, komanso kuwabweretsa moyenera ndi
nthawi komanso ndi nyengo yomwe mwanayo amakhala.

Ndipo zikubwerazi ndi zina mwa zitsanzo za mafunso omwe amabwerabwera pa
lilime la ana, ndipo dziwani kuti awa simafunso onse ayi, koma ofunikira kwam-
biri mwa iwo ndiponso omwe amafunsidwafunsidwa kwambiri, ndipo taye-
setsa kuika mayankho abwino kwambiri okha okha malinga ndi kuona kwathu, ndi-
po sitikudzichemerera kuti amenewa ndi mayankho apamwamba kwambiri ayi;
koma kuti izo ndi zitsanzo zoti makolo atha kuzitenga ngati poyambira, ndipo
tikukutsimikizirani kuti mayankho amenewa mutha kuwakonza, kuwapungula
kapena kuwaonjezera.

CHENJEZO:

Yemwe angaganize kuti iye sangakwanitse kuphunzitsa ana ake, kuopera kuku-
mana ndi mafunso ovuta; ndiye kuti iyeyo ndi wolakwitsa, khalidwe limenelo (
lokonda kufunsa mafunso ovuta) kwa ana ndi chizindikiro cha thanzi lawo kuti
akukula mwa chilengedwe komanso kuti nzeru ndi kuthekera kwa kuganizira
kwawo kukukula mwa dongosolo, ndi kuti pakapezeka vuto, ndiye kuti ndi chi-
fukwa cha kulephera makolo kukwaniritsa makulidwe a mwana wawo ndi kulep-
hera kutsegula ngodya za nzeru zake ndi kulandira kwake zinthu zobisika ndi
zooneka zomwe zamuzungulira⁽¹²⁶⁾. Choncho makolo ndi aliyense yemwe ama-
yanganira mwana adzayenera kulimbikira kumpatsa mwanayo mayankho ogwira
mtima olo kangachepe, chifukwa yankho logwira mtima pang’ono limathandiza
kudekhetsa mtima wake, maganizo ake ndi kukhala kwake ndi anthu, pomwe
mayankho olakwika amaonjezera mwana kubalalika, ndipo kubalalika kumeneku
kumapangitsa kusokonekera kwa khalidwe la mwanayo, ndi kuperevera kugan-
iza kwake komanso kachitidwe kake ka zinthu.

Ndithu mavuto akulu akulu samadza nthawi imodzi, olo moto umayamba ndi
lawi lalingono, choncho; makhalidwe ambiri oyipa pa munthu amaoneka ngati
njere yayingono yothiridwa ndi kuzengereza ndi kuimikira imikira, ndipo kam-
akulirakulira kamba ka kusalabada chifukwa chotengeka ndi umoyo mpaka kuku-
la namerera mizu mu mtima moti siingatheke kuchoka kapena kuzulidwa⁽¹²⁷⁾.

MAFUNSO OKHUDZA KUKHULUPIRIRA MWA ALLAH



Ndithu mafunso omwe amakonda kuzungulira kwambiri mmutu wa mwana akakhala wachichepere kwambiri ndiwo mafunsa okhudza Allah. Ndipo pano tibweretsa ambiri mwa mafunso amenewa omwe ana amakonda kufunsa kwa makolo awo:

Kodi Allah (MULUNGU) ndi ndani?

Choyamba, tisadikire kuti mpakana mwana atifunse zokhudza Allah, koma timu-fotokozere mwachangu za Allah nthawi zonse komanso pa zochitika ndi pam-pata (opportunity), ndithu yankho lolondola la funso la mwana lokhudza Allah ndi mbiri zake lidzamanga maziko a Tauheed(umodzi wa Allah) ndi kukhulu-pirira Allah (mwini ulemelero wonse) mu nzeru za mwana komanso mu mtima wake, pachifukwa chimenechi, ndithu njira ya pamwamba kwambiri ndiko kuzi-panga nzeru za mwana kuti zisiye kuganiza za maonekedwe a Allah mwini wakeyo koma aziganiza za mitendere ndi kud-abwitsika kwa chilengedwe zomwe Allah walenga zomwe zikusonyeza kuti Allah alipo, monga kumwamba ndi thambo, nyenyezi, dzuwa ,mwezi, n-yanja ,mitengo, ndi zina zotero ⁽¹²⁸⁾, ndikumudziwitsa ma ubwino a Allah pomulenga iye ndikumulengeranso ziwalo, monga :maso, makutu, pakam-wa , lilime, mikono, miyendo ndi ziwalo zake zina. Ndipo timuuzze kuti mitambo imeneyi anailenga ndi Allah, chimodzi-modzinso nthaka, mitengo yonse, ndi zina zotero, kufikira mwana atazolow-era ndikusangalatsidwa nawo mawu amenewa, ndipo akamatifunsa kuti kodi Allah ndi ndani? Tizimuyankha mwa chidule kuti iye (Allah) ndi amene adalenga anthu ndi zinthu zonse zom-we zatizungulira, kenako timupatse zitsanzo zochulukira pa chimenechi.



Tikamaliza kumudziwitsa ndi kumuonetisa zolengedwa za kumwamba ndi za pansi pano, namudziwitsa dongosolo ndi kasanjidwe ka ukatswiri ka zinthu zimezezi, tidzamuuze mwanayo kuti: kodi waliwona dongosolo la kasanjidwe kame-neka, ndithu yemwe anapanga zimenezi ndi Allah, ndithu tikatero iye adzam-udziwa mbuye wake mozindikira ndi mwa maumboni. Timuuzenso kuti Allah ndi amene analenga chilichonse ndipo iye (Allah) safanana ndi chilichonse, ndipo iye ndi wachifundo, wodyetsa ndi wopereka, komanso ali ndi maina ndi mbiri za-bwino ndi za pamwamba zokha zokha, choncho iye akuyenera kupembedzedwa ndipo asaphatikizidwe ndi china chilichonse, komanso timuuze kuti Allah ama-konda kwambiri ana moti anawalamula akuluakulu kuti azithandiza , kuyangan-ira ndikuchitira ubwino ana ndi anthu onse,ndipo iye akatiwerengera pa ntchito zomwe tagwira zabwino ndi zoipa zomwe potilipira sawab (zabwino) kapena chi-lango, moti iye ndi amene amamulipira munthu wochita zabwino molingana ndi ubwino wake, komanso woipitsa molingana ndi kuipitsa kwake. Ndipo ndi bwino kuwaphunzitsa anawo ma Surah (ndime za mu Korani zazifupizifupi; chifukwa masurah amenewa ali ndi mayankho abwino abwino okhudza Allah ndi mbiri zake, moti iye ndi Allah yemwe: sanabereke kapena kuberekedwa, ndipo alibe wofanana naye⁽¹²⁹⁾.

Nzothekanso kumufunsa funso loti: “kodi ndi ndani yemwe anakugulira zovala zokongola zimenezi?”Ndipo iye adzayankha kuti: “bambo anga”, nanga ndi ndani yemwe amakuperekeza popita ku sukulu? Iye adzayankha kuti bambo anga, nan-ga ukadwala ndani amene amakuperekeza kwa dotolo? Iye adzati bambo an-ga,nanga ndi ndani yemwe amakutenga kupita kokasangalala nthawi ya tchuthi? Iye adzati bambo anga, nde kuti bambo ako ndi amene amakupangira zonse? Iye adzati: inde.

Zikatero muuzeni mwanayo kuti tsono Allah ndi amene amatiyang’anira tonsefe (iweyo, ife kuphatikizanso bambo akowo), iye ndi amene analenga chilichonse, zonse zomwe umazona mmbali mwako ndi zolengedwa ndi Allah, dzuwa ndi mwezi, mitambo, Nyanja ndi mapiri, kulenga anthu,zinyama ndi mbalame, ku-lenga angelo ndi ziwanda,Allah ndi amene analenga dziko lonseli, ndipo Allah ndi wopereka komanso wachifundo, amatiyanganira ndi kutisamalira, amatikonda ndi kumatibweretsera maubwino nthawi zonse.



Kodi Allah amafanana ndi munthu?

Ayi safanana naye,iye safanana ndi chilichonse, iye ndi amene analenga ine, iweyo ndi anthu onse, analenga mitengo, mitsinje,Nyanja ndichina chilichonse pa dziko lapansi pano, kwa iye ndi kumene kumachokera mphamvu za pamwam-ba , akafuna china chake amangochiiza kuti: “chitika” ndipo chimachitikadi. ndi-po Allah ndiwosiyansiratu ndi munthu, munthu sangathe kulenga munthu nzake, koma Allah zimenezo amakwanitsa, ndipo angathe kupanga chilichonse chomwe

wafuna, nde chifukwa cha kuti palibe amene angathe kumuona Allah pa umoyo uno wa dziko la pansi, palibe amene angamufotokoze Allah (maonekedwe ake), ife sitingakwanitse kumuona Allah (chifukwa iye) ndi dangalira lamphamvu, kuthekera kwa maso athu ndi koperewera.

kenako timpemphe mwanayo kuti apite akayang'ane ku ma dangalira (rays) adzuwa ndipo asakasizine ayi, kenako timufunse kuti: kodi ungakwanitse kuyang'ana (china chake) ku dzuwako? Ndipo iye adzatsutsa, choncho tidzamuuzazi kuti: mwana wanga wolemekezeka, dziwa kuti dangalira lochokera kwa Allah sitingathe kukwanitsa kupilira kuliyang'ana, koma tikakalowa ku Jannah tikamuona Allah muchilolezo chake.

Pamenepa mwana atha kukutsutsa ndi kuonetsa kusakhutitsidwa ponena kuti: zimatheka bwanji Allah yo osafanana ndi chilichonse? Apa pazafunika kumuuzazi mogwira mtima koma modekha ponena kuti: ndithu nzeru zathu ngakhale zitakhala zazikulu ndi zomvetsetsa kwambiri chotani, zidzakhalabe nzeru za umunthu ndizosakwanira, zimadziwa zokhazo zomwe Allah anafuna kuti zidziwe, ndipo zomwe Allah sanafune kuti nzeru zathu zidziwe sizingadziwe, moti nzosatheka kuti tidziwe zinthu zonse, chifukwa tidzakhalabe anthu. Timuuzenso kuti: Allah akanakhala munthu ngati ife nde kuti bwenzi akumadwala monga mmene ife timachitira, bwezinso akumadya, kumwa ndi kumwalira ngati mmene anthu amachitira, koma Allah samapanga nawo kapena kumuchitikira chilichonse mwa zimenezi, iye ndi wopezeka nthawi zonse, ndipo iye ndi mlengi wa mitambo, nthaka ndi chilichonse chimene chili pa dziko pano, choncho Allah safanana ndi chilichonse.

Tingathenso kumufunsa mwanayo kuti: kodi ifeyo anthu tingathe kuchiuza chinthu kuti “chitika!” nachitikadi? Mwana adzayankha kuti ayi, zikatero ife limodzi ndi mwanayo tidzatulutsa ganizo loti: ndithudi Allah simunthu ngati ife ayi koma iye ndi mlengi wamkulu kwambiri.

Timuuzenso kuti kumva kwathu kuli ndi malire, timangomva zokhazo zimene zikupezeka pa mtunda wina wake, tikanakhala kuti timamva china chilichonse tikanatopa, maso athunso ndi ofooka, timangoona zokhazo zimene zili pa mtunda wina wake, ife sitingathe kuona zomwe zili kuseli kwa chipupa – mwachitsanzo-, ndiye mmene kulili kumva ndi kuona kwathu kuti ndi kofooka, chimodzimodzinso nzeru zathu ndi zofooka chifukwa sizimazindikira zinthu zonse (zimangozindikira zinthu zochepa zokha).

Ndithu nzeru za munthu ndi zofooka, moti kuyambira pamene Allah adalenga munthu kufikira lero, gawo la zimene munthu samazidziwa limakhala lalikulu kwambiri kuposa gawo la zomwe amazidziwa, ngakhale nzimu womwe umapezeka mthupi la munthu ameneyu –mwachitsanzo– ngakhale tili nawo pafupi kwambiri, koma sitimaudziwa kwenikweni kapena kuuyerekeza ndi china chake,

ngati izi zikuchitikira pa chomwe chili mwa ife, kuli bwanji za chomwe chili kunja kwa ife?, kotero, ndithu nzeru za munthu zidzakhala zofooka , sizingathe kudziwa mmene Allah amaonekera; kotero maonekedwe a Allah sungawadziwe kudzera mu zithunzi kapena , nzeru ndi kuganizira chabe ayi, koma kudzera mu malamulo a Allah okha tingathe kudziwa, Quru'an yanenetsa zimenezi motere: “ **Palibe chilichonse chofanan ndi iye, iye ndi wakumva zonse komanso amaona zonse**”. (Surat Ash Shura: 11).

Kuchokera pa mawu amenewa, tikupeza kuti ndithu Allah safanana ndi ife-kapena chilichonse ⁽¹³⁰⁾, zimenezi zikusonyeza kuti Allah ndi wamkulu kwambiri yemwe tikuyenera kumukonda, kumupempha komanso kumuopa, ndipo ukulu umenewu ukukwanira kupangitsa kuti kukamuona iye ku Jannah kukakhale chonyaditsa chapamwamba kwambiri mu Jannah yonse.





Kodi yemwe adamUlenga Allah ndi ndani?

Zikadakhala kuti alipo yemwe adalenga Allah, inenso nkadafunsa kuti: ndani adalenga mlengi? Sichoncho? Koterokutiyenera kudziwa kuti zina mwa mbiri za mlengi ndi zakuti: iye sadachite kulengedwa ndipo iye ndi amene adalenga zolengedwa zonse, akadakhala kuti iye adachita kulengedwa sitikadamupembedza kapena kutsatira chiphunzitsondi malamulo ake, ndiye funso lonena kuti ndani adamulenga Allah silolondola ndipo lilibe tanthauza, mwachitsanzo, mmodzi wa iwo atakufunsa kutalika kwa nzere wachinayi wa chinthu cha mizere itatu (triangle)? palibe choyankha pamenepo chifukwa triangle ili ndi mizere itatu yokha, nde pamene pakulakwika mu funso loti analenga Allah ndi ndani? Ndi liwu loti: “adamulenga” lo motsogozedwa ndi liwu loti: “Allah” lo, chifukwa mawu amenewo sangayendere limodzi ayi, chifukwa wopembedzedwa salengedwa, ndipo ntchito yolengedwa ndithudi imakhala pa zolengedwa pokha, palibe amene angakwanitse kumulenga Allah, akadapezeka ameneyo nde kuti Allah nayenso akadakhala cholengedwa, koma Mulugu ndi wopezeka nthawi zonse, alibe chiyambi ngakhalenso mathero.

Olo titayesera kuika mtsutso woti kuli mlengi wa Allah (wapamwambamwamba), ndiye kuti anthu azingofunsana funso lomweli loti adalenga mlengi ndani? Choncho lizingopitilira osafika pa mathero a mtsutsowo, zosatheka kupezeka mlengi wa mlengi, ndipo pofuna kuyandikitsa zedi titenga chitsanzo cha msilikali ndi chipolopolo, iye akafuna kuombera azipempha chilolezo kwa nzake yemwe ali kumbuyo kwake, nayenso kuti apereke chilolezo akuyenera kupempha chilolezocho kuchokera kwa amene ali kumbuyo kwake, ndikumayenda choncho mpaka kopanda polekezera, funso nkumati: kodi msilikali uja adzaombera? Yankho nkumati: ayi, chifukwa sadzapeza msilikali yemwe adzapereke chilolezo choti iye awombere, pomwe tcheni chija ngati chingafike pa munthu yemwe pamwamba pake palibenso wina woti angapereke chilolezo chowombera ndiye kuti adzaombera, koma kupanda kupezeka munthu ameneyu, ndiye kuti anthuwo olo atachuluka motani chipolopolo chimenecho sichidzaombedwa, iwo adzakhala ngati ma ziro (zero) ukawandanditsa, olo atachuluka mopanda mapeto, iwo adzakhalabe opanda nambala ya chilendo (adzakhalabe ziro), pokha pokha kutaikidwa kumayambiriro kwakeko nambala ina yosiyana ndi ziro, monga (1) ndi manambala ena ⁽¹³¹⁾.



KODI ALLAH ADACHOKERA KUTI NANGA ALI NDI ZAKA ZINGATI?

Ngati iwe - m’bale wanga wolemekezeka – ukudziwa kuti Allah sadalengedwe; ndithudi chimodzimodzi iye sadabeleke kapena kubelekedwa, alibenso chiyambi ngakhalenso mathero, koterokutalibe zaka zakubadwa ngati momwe zikhalira kwa ife anthu, chifukwa Allah ndiye mlengi wamkulu wolembera kwambiri, mwini

mphamvu komanso wolimba, mwini ulemerero ndi wachifundo yemwe ali ndi maina abwino okhaokha ndi mbiri zabwino komanso zokwanira osati zopunguka, Allah ndi amene anapezeketsa dzikoli ndi zolengedwa zonse.

Kodi Allah asanapezeke kunali ndani?

Funso limeneli ndi chimodzimodzi ndi lija lonena kuti adamulenga Allah ndi ndani, ili ndi funso lolakwika chifukwa Allah ndi woyambirira ndipo pasanapezeke Allah panalibe chilichonse, komanso iye ndiwomaliza pambuyo pake palibe chilichonse, Allah akunena kuti⁽¹³²⁾ **“Iye alibe chiyambi, wamuyaya, woonekera, wobisika kwambiri (saoneka) ndipo iye ndi wodziwa chilichonse”** Surat: Al-Hadid: 3) ndithu nthawi ili ngati malo sizingaike malire a Allah, ndipo nthawi ndi chimodzi mwa zolengedwa za Allah, kotero zolengedwa sizingaike malile kapena kumuzungulira mlengi wake, Allah ali ndi mbiri zonse zabwino ndi zokwanira, apa tikuyenera kuchenjera ndikulandira langizo (wasiyyah) la mtumiki (SAW) lomwe Abu Hurairah adamumva mtumiki akunena kuti: **“Satana amatha kumufikira mmodzi wa inu ndikumamufunsa kuti kodi ndani adalenga chakuti? Nanga chakuti anachilenga ndi ndani? Mpaka amafika pofunsa kuti: ndani analenga mbuye wako? Pakafika pamenepa, iye adzitchinjirize mwa Allah kenako aziwale (zomwe amafunsidwa ndi satanazo)”** (Bukhar 3276), kudzitchinjiriza mwa Allah ndi kutembenezira maganizo amwana ku zinthu zina mosakhala mwachindunjiku, ndicholinga choti asapitirize mafunso amenewa, nakonso ndi umodzi mwa mitundu yakuyankha kofunikira pa nkhani imeneyi, pomwe kutembenezamaganizo a mwana ndi kuwatalikitsa ku zimenezi si kuti ndi chifukwa choti ulibe yankho ayi, koma kutseka molowera manong’onong’o a satana

Kodi Allah ndi wamwamuna kapena wankazi?

Tikuyenera kuzitalikitsa nzeru za mwana kuti zisamaganizire kwambiri za maonekedwe a Allah, ndipo tiziongolere nzeru zake kuti ziziganizira zinthu zomwe zingamubweretsere phindu, apa tsopano zidzakhala bwino kumuza momveka kuti kukhala mwamuna kapena mkazi ndi zinthu zosiyanitsira magulu ndi mitundu ya zolengedwa za moyo, izi ndi zina mwa zomwe Allah anazipatsa zolengedwa zake, Allah akunena kuti: **“Ndipo iye ndi amene adalenga mitundu iwiri: chachimuna ndi chachikazi”**. (Surat Al-Najim: 45) pomwe Allah ali pamwamba pa onsewo.

komanso kuli zolengedwa zina zomwe sizimalowa nawo mmagulu amenewa, monga: angelo, kumwamba, mitambo, mphepo ndi madzi, zimenezi sizimatchedwa zazimuna kapena zazikazi, choncho ngati zikutheka kupezeka zolengedwa zina zosalowa nawo mmagulu amenewa, nde kuti Allah ndi amene akuyenera kwambiri kusapezeka nawo mmagulu amenewa: **“Palibe chilichonse chofana na ndi iye, iye ndi wakumva zonse ndiponso woona zonse”** (Surat Shura: 11).



KODI NCHIFUKWA CHIYANI TIMAKHULUPIRIRA KUTI ALLAH ALIPO? NANGA TINGATSIMIKIZE BWANJI ZIMENEZI?

Kukhulupirira mwa Allah ndi chibadwa cha munthu wina aliyense chimene palibe yemwe angachitsutse ndipo ma umboni oti Allah alipo ndi ochuluka zedi, ndipo anthu adakatulukirabe ma umboni pamwamba pa maumboni ena, wina aliyense mwa anthuwo molingana ndi mbali yake ya maphunziro imene akufufuza, ndipo umboni wa chibawa cha munthu umatsimikizira kuti Allah alipo, Allah akunena kuti: **“Dzikakamize wekha kuchilengedwe chimene (Allah) adalengera anthu,(ichi ndi chipembedzo cha chisilamu chomwe nchoyenerana ndi chilengedwe cha Munthu)”**. (Surat Al Rum: 30) tonsefe timamva mumtima mwathu kuti muli mphamvu ina yake yomwe imauza mtimawo za ukulu, mphamvu ndi chisamaliro cha Allah pa ife, pomwe maumboni okhudzika ochokera mmaphunziro akutsimikiziranso kuti pa dziko pano pali dongosolo la kuya ndi la mtengo wapatali, ndipo dongosolo limeneli pali amene analiika; chifukwa zolengedwa zonsezi ndi ndani anazipezeketsa?

Kutheka kuti zinangopezeka mwangozi popanda wozipezeketsa, ngati zili choncho nde kuti palibe angadziwe mmene zinapezekera zinthu zimenezi, chimenecho ndi chiyembekezo choyamba. Pomwe chiyembekezo chachiwiri ndi choti: zinthu zimenezi zinadzipezeketsa zokha ndipo zimadziyang'anira zokha, ndipo chiyembekezo chachitatu ndi chakuti: pali amene anazipezeketsa ndi kuzilenga.

Ndiye tikayang'ana ziyembekezo zitatu zonsezo, tipeza kuti chiyembekezo choyamba ndi chachiwiricho nzosatheka, zikatero nde kuti choyambacho ndi chimene chingakhale choona komanso chomveka, zoti pali mlengi yemwe adazilenga (Allah), ndipo izi ndi zomwe Allah adazinena mu Qur'ani ponena kuti: **“Kapena adalengedwa popanda Mlengi kapena iwo adadzilenga okha, kodi iwo ndi amene adalenga thambo ndi nthaka? Koma iwo sakhulupilira kweni kweni”**. (Surat Al Tur: 35 -36).

Ndipo ena mwa maumboni osonyeza kuti Allah alipo ndi izi: kuyankha kwa Allah ma dua (mapempho) a anthu, ukatswiri wa kalengedwe ka mitambo ndi nthaka, Allah akunena kuti: **“Ndithudi mukalengedwe kakumwamba ndi dziko lapansi ndikusinthana kwausiku ndi usana, ndizisonyezo (zoti kuli mlengi wa zimenezi) kwa eni nzeru”**. (Surat Al Imran: 190), komanso poona ukadaulo wa kalengedwe ka munthu, Allah akunena kuti: **“Ndimwainu nomwe kodi simuona?”**. (Surat Adharyat: 21). Ndi kalengedwe ka nyenyezi, mapiri, zinyama, ndi zina zotero, zonsezo zimasonyeza ukatswiri wa Mulungu pa zolenga zake.

Ndithu zizindikiro zoti Mulungu alipo zili pali ponse: pa dzikoli, m'mitima kapena mmaturupi (a anthu ndi zinyama), ndizipatso zonse zikusonyeza kuti kuli Mu-

lungu m'modzi wayekha (yemwe adazipezeketsa zonsezi) ndipo kupezeka kwa zolengedwa zonsezi kukusonyeza kuti kuli ndi cholinga chapamwamba zedi chomwe Mulungu adazilengera ndipo zonsezo zimapembedza Mulungu (Allah) yekha yemwe alibe chophatikizana nacho⁽¹³³⁾.

Ndizothekanso kumusimbira mwanayo nkhani ya Abu Hanifah (R.a) atamupempha anthu ake kuti awatsimikizire zoti kuli Tauhid ya Rububiyah (zoti Mulungu yekha ndi amene amalenga ndi kumasamalira zomwe walengazo) Abu Hanifah anati kwa anthuwo tisanakambe nkhani imeneyi tandiuzeni zachombo chomwe chimadziyendetsa chokha pa mtsinje wa Dijlah (Tigris) nichikatenga chakudya ndi katundu wina pachokha nabweleraso pachokha, ndikumaimanso chokha kenako ndi kutsitsa katunduyo chokha ndikumabwelera, zonsezo chombocho chimapanga chokha popanda wochiyendetsa komanso wochiyang'anira (Tandiuzeni kuti zimatheka bwanji zimenezi?) ndipo iwo adati zimenezo sizingatheke komanso sizidzatheka mpaka kalekale, Abu Hanifah adat: ngati sizingatheke zimenezo pa Chombo; kuli bwanji dziko lonseli m'mene lakuliramu kuyambira kumwamba mpaka pansi pano!⁽¹³⁴⁾ Ndithu nzosatheka kuti kalengedwe kaluso kadziko lime-neli kakhale kopanda Mlengi wakutha kwambiri komanso wozindikira zedi.

Nzothekanso kumufunsa mwana kuti kodi ukamamva kupweteka m'mimba siuja umazindikira kuti uli ndi njala, kenako ndikumafunafuna chakudya wekha wekha kuti uthetse njalayo? Komanso ukamva ludzu siuja iwe umafunafuna chakumwa chimenechingathetse ludzu limeneli?ndipo ukanunkhitsa fungo labwino siuja umasangalatsidwa nalo iwe? pomwe ukamva fungo loipa siuja umanyasidwa? Komanso ukamaona maluwa, mitambo ndi chilengedwe chomwe chatizungulira, kodi simumasangalatsidwa nacho ndi kukupatsa chimwemwe?

Chimodzimodzi m'bale wanga wolemekezeka tonsefe timazindikira mwaife tokha kuti timafunikira wachikulire kwambiri kuti tizimudalira nthawi iliyonse tikafuna kuti tipeze mpumulo ndi chitetezo, chifukwanthawi imeneyi timayamba kubanika ndi kudandaula; ndithudi mwaife tokha mwachidziwikireni kuti timathawira kwa Mulungu ndikumupempha iye, ndipo tikakhala pa mtendere timamutamanda iye pa mtendere umeneu.





Kodi Mulungu amamva, kuona kapena kulankhula ngati ife?

Ndithu Mulungu amalankhula, kumva komanso kuona, Mulungu akunena kuti: **“Ndithu Mulungu wamva mau a (mkazi) akubwezerana bwezerana nawe(mau) pazamwamuna wake”**(Surat Al mujadilah: 1). adanenaso kuti: **“Mulungu adati musaope ndithu ine ndili nanu pamodzi ndikumva ndiponso ndikuona”** (Surat twaha: 46) adatiso: **“Ndithu iye (Mulungu) akuona zonse zimene muchita”** (Surat Hudu: 112), koma singati m’mene ife timalankhulira kapena kumvera ndi-kuonera ayi, chifukwa Mulungu ndiwosiyana ndi zolengedwa zake, iye amamva mau ngakhale atakhala mauwo alankhulidwa mobisika chotani, amaona chilichonse angakhale chitalikira motani, Mulungu amaona ndi kumva chilichonse koma kuona ndi kumva kwakeko sikumafanana ndi kumva kapena kuona kwa zolengedwa zake chifukwa kuona ndikumva kwa zolengedwa ndi kofooka komanso kopunguka chifukwa Mulungu akulankhula Kunena kuti: **“Palibe chilichonse chofanana ndi iye, iye ndiwakumva zonse komanso woona zones”**. (Surat Ashura: 11).

Ndipo ndibwino kuzilumikiza zimenezi ndi khalidwe la chindunji, monga kufunsa kuti: ngati Mulungu ali wakumva ndi kuona mwamphamvu, kodi tikuyenera kukamba zomwe sizingamusangalatse ndiye atione tili pakaonekedwe komwe iye samakafuna?!(¹³⁵).

Kodi Mulungu samva njala kapena ludzu?

Mulungu (mwini mphamvu ndi ulemelero wonse) ali ndi mbiri zokwanira zokha zokha ndipo alibe mbiri iliyonse yopunguka. Ndithu njala ndi ludzu ndi zizindikiro zakufoka ndipo sizifunikira kumpatsa Mulungu, komanso Mulungu safuna chakudya kapena chakumwa(¹³⁶); chifukwa Mulungu ndi amene analenga chilichonse kotero safunikiranso chilichonse mwazimenezo, kotero iye akanafunikira chinthu china chake sakanakhala Mulungu. Inde Mulungu ndi chikhomo samadya komanso safunikira chakudya ndi chakumwa, iye alibe nazo ntchito zimenezo, komanso iye ndi amene amapemphedwa ndi zolengedwa kuti azithandize, monga kuzidyetsa, kuzimwetsa ndi kuzipangira zokhumba zake.

Ndizothekanso kumuza mwanayo kuti: ndithudi Mulungu palibe chomuyerekezera ndi zolengedwa zake, ndipo sizoonza kuti chilichonse chomwe ife tingapange ndi kuchitulukira chingakhale mbiri yathu kapena maonekedwe anthu ayi, si choncho? Mulungu samamva njala kapena ludzu, ndilorenindikufunseni funso: kodi amene amapanga njinga ndi ndani? Iye adzayankha kuti “kampani yopanga njinga”; zilibwino kwambiri, tabwera mwana wanga tilingalire limodzi kuti njinga izimufunsa yemwe anaipanga kuti: umadya chiyani? Umamwa chiyani? Ungayiyankhe chiyani? Ndingaiuze kuti zimenezo sizikukukhudza, upin-

dula chiyani ukadziwamo, kodi yankho lako lizaonjezera chiyani ku ntchito yake yeniyeni yanjinga yoyenda mwachangu ndi mopanda ulesi, chabwino (zilibwino kwambiri), chimodzimodzi –mwana wanga – Mulungu anatilengera ntchito yochepa ngatim'mene Allah akunenera: **“Sindidalenge ziwanda (majini) ndi anthu koma kuti azindipembedza”**(surat adhariat: 56). Choncho mafunso amenewa sangatithandize kupeza ntchito ina yoonjera pantchito yomwe Mulungu anatilengera, koma mmalo mwake mafunso amenewa atisokoneza nzeru zathu kuti tisashe kugwira ntchito yomwe adatilengera. Kodi nanga njingayi idzalunjika liti kwa ifeyo kutipempha thandizo? Ikazaonongeka china chake, ndithu iyo idzalunjika kwa okonza kuti akakonze choonongekacho, chimodzimodzi ife timalunjika kwa Mulungu pomupempha tikaona kuperewera pakupembedza kwathu, kapena likatigwera vuto lina lake.



Kodi mphamvu za Mulungu ndi zochuluka bwanji?

Ndithu ife tikamanena zamphamvu kapena kuthekera komwe kuli koperewera; ndiye kuti tikutanthauza mbiri yofooka, chifukwa pothera mphamvu ime-neyo ndipamene padzayambire kufooka, ndipo kufooka sikumakhala pa Mulungu choncho kuthekera kwa Mulungu ndikopanda malire ndipo palibe chomwe chingamufuole iye kapena kumulepheletsa, Mulungu akunena kuti: **“Kodi siukudziwa kuti Mulungu ngokhonza chinthu chilichonse”** (surat bakara: 106) ndipo akafuna chithu amangoti **“chichitike”** ndipo chimachitika.

Mulungu ndi wakutha chilichonse; chifukwa iye ndi Mlengi wachili chonse, sichingamukanike chili chonse chadziko lapansi ndi kumwamba komwe.

Pomwe kuthekera kokhala ndi malire ndikwa zolengedwa, chifukwa kumeneko ndikuthekera kochita kulengedwa. Pomwe kuthekera kwa Mlengi; kulibe malire kapena kupunguka. Choncho; Mulungu yekha ndi amene akuyenera kupembedzedwa ndi kupemphedwa; chifukwa iye yekha ndi amene ali ndi kuthekera koyankha ndikuthandiza zofuna zazolengedwa, kuwadyetsa ndikuwakwanilitsira zofuna zawo komanso kuyendetsa zichitochito zawo⁽¹³⁷⁾.



Kodi Mulungu amakhala kuti nanga ndi wamkulu motani?

Pambuyo poti mwana wamvetsa pansi pansi zoti Mulungu ndi amene adamulenga komanso kuti Mulungu amakonda ana kwambiri, ndikuti iye anamupatsa mwanayo mitendere yochuluka, ndizotheka nthawi imeneyo kumulongosolera kuti Mulungu alipo ndipo amapezeka kumwamba, Mulungu akunena kuti: **“Kodi muli m'chitetezo kwa amene ufumu wake uli kumwamba”** (Surat al muluku: 16), iye (Mulungu) alikumwamba koma kuzindikira kwake kuli paliponse, Mulungu akunena kuti: **“Ndipo iye alinanu paliponse pamene muli”** (Surat Al Hadid: 4), ndipo si zoyenera kwa ife Kunena kuti Mulungu ali pali ponse ayichifukwa

kutero zizanthauza kuti Mulungu ali mkati mwachili chonse, zimenezo sizoonay; ndithu ife timagwiritsitsa zomwe zili muchiphunzitsa, Mtumiki (saw) anamufunsapo kapolo wachikazi kuti: **“Kodi Mulungu amakhala kuti?” iye adati: “kumwamba”, Mtumiki (saw) adati “nanga ndine yani?” iye adati: “Mthenga wa Mulungu”, Mtumiki adati: “Mmasuleni ukapolo chifukwa iye ndi wokhulupirira”.**(Muslim -537).

Ndiye ngakhale iye amakhala kumwamba komabe amakwanitsa kutiona ndikutimva malo ali onse, ndipo timutsimikizire mwanayo nthawi zonse kuti Mulungu amamuona iye nthawi zonse, umeretse chimenechi mu mtima wamwana ndipo chikhale chomulondera iye (mlonda wake), pomwe zokhudza kukula kwake: Mulungu wapamwamba mwamba asafanizidwe ndi cholengedwa chilichonse, chifukwa Mulungu ndi wamkulu kuposa chili chonse, kuposa zolengedwa zonse moti pakapezeka zolengedwa zazikulu zikulu ndithu Mlengi wake ndi wamkulu kuposa izo; ndipo iye ndi amene adzazule mapiri, ndi kugwedeza Nyanja, amawalamula madzi kuti azilowa munthaka, ndipo zonse zomwe zimachitika padziko pano zimachitika muchilamulo chake ndi chifuniro chake, ndithu Mlengi safuna thandizo lochokera kuzolengedwa zake, thambo ndichimodzi mwa zolengedwa za Mulungu ndipo kupezeka kwake (Allah) sikuti kwagona pa kupezeka kwa thamboko ayi, ndipo iye sapeza phindu lililonse kuchokera ku thambolo, chifukwa Mulungu ndi wolemvera kwambiri kuposa wina aliyense ndipo safuna thandizo la chilichonse⁽¹³⁸⁾.



KODI ZIMATHEKA BWANJI IFE ALLAH AMATIONA POMWE IFE IYE SITIMAMUONA

Ndithu maso omwe Mulungu anatipatsa pa dziko lapansi pano ndi ofooka sangathe kuona zochuluka; pa chifukwa ichi mudzaona munthu akugwiritsa ntchito zipangizo zoonera zinthuzazing’onozing’ono (microscope) ndi zipangizo zina zokulitsira zinthu, ndiye ngati munthu akulephera kuziona zinthu zolengedwa, kusamuona Mulungu kudzakhala koposa, ndithu kuthekera kwa munthu pa dziko la pansi lino sikungamuthandize kuti amuone Mulungu, iye sitingakwanitse ku muona Mulungu koma timamukhulupirira, timakhulupiriranso kuti Mulungu ndi wachifundo komanso amatikonda, ndiwamphamvu komanso ali ndikuthekera kopanga chilichonse, ndipo amadziwa chilichonse, ndiponso akudziwa kuti ife pa nthawi ino tikukambirana za iye, ndithu Mulungu safanana naye kutalitali, choncho iye amationa tonsefe nthawi imodzi ngati mmene zimakhallira munthu akakwera pamwamba pa nyumba yosanjikizana amatha kumawaona anthu onse omwe ali munsewu pomwe iwo samamuona iye, choncho Mulungu amationa koma ife sitimamuona iye.

Ndithu pali zinthu zambiri zomwe sitingathe kuziona koma izo zilipo, ndipo timuuzze mwana kuti: ndithu maso athuwa sangathe kuona zinthu zonse ayi, ife

sitimatha kuwaona mawu ngakhale timawamva, sitingaone mphepo ngakhale imatikhudza (imatiomba), ndiye maso athuwa sangathe kumuona Mulungu pa dziko pano, koma ku Jannah – mu chifuniro cha Mulungu- tikakhala kumeneko ndi maso abwino kwambiri omwe akakwanitse kumuona Mulungu wapamwambamwamba, choncho Mulungu akulankhula kunena kuti: **“Maso samufika iye (samuona); koma iye amawafika maso (amawaona pamodzi eni masowo). Iye ngodziwa zobisika kwambiri ndi zoonekera”**. (Al ani’am:103).



KODI ALLAH AMAKWANITSA BWANJI KUWAONA ANTHU ONSE KUMACHITA KUTI IWO NDI OCHULUKA KWAMBIRI?

Kuti tithe kuliyanika funso limeneli, timutenge mwanayo tikaime naye pa msewu, numufunsa kuti: uziwayang’ana anthuwo kenako undiuze kuti waona angati, tiwerenge limodzi anthu omwe ungawaonewo, kenako tikwere pa nyumba yaitali ndikumuuza kuti aziwerenga omwe akuwaona, kenako tikwere naye nyumba yaitali kwambiri ndikumuuza kuti aziwerenga anthu omwe akuwaona, kenako timupatse magalasi kuti azitha kuwaona anthuwo ndi kuwawerenga bwinobwino.

Kudzera mu chitsanzo chimenechi, tidzatha kumuwalitsira mwanayo kuti ndithudi ife sitingathe kuyeza bwino zinthu patokha pogwiritsa ntchito miyezo ya umunthu wathu, choncho timufotokozere iye kuti kuthekera kwa Mulungu ndi kwa kukulu kwambiri kuposa kuthekera kwa zolengewa zake zonse, ndipo tiike mu nzeru za mwanayo nthawi zonse mawu awa: **“Kodi siukudziwa kuti Mulungu ngokwanitsa kupanga chinthu chilichonse”**. (Baqarah :106).

Tingathenso kumufunsa funso lokhudzika ili: kodi umakhulupilira kuti nyere zimathana ife m’mene tilili kapena zimangotiyerekeza kapena zimangooka zithunzi? Iye adzayanka kuti nyere imangokwanitsa kuona mbali chabe yaying’ono kwambiri yachala chathu chachikulu chakumiyendo, mwinsano ingathe kuganizira kuti chalacho ndi phiri kwa iyo. Chabwino, nanga ukuganiza kuti nyere ingathe kufunsa kuti umakwanitsa bwani kutiona ife tonse pakamodzi? Yankho lako lidzakhala lonena kuti: zimenezo ndi zachikhalire: chifukwa zikugwirizana ndi kuthekera kwako komwe Mulungu anakulengera.

Nyerere kuthekera kwake ndi kochepera, ndipo patha kupezeka nyumba zochuluka za nyere m’malo osiyana siyana padzenje limodzi, ndipo nzophweka kwa iwe kuwaona malo onsewa nthawi imodzi, pomwe nyere ndikuthekera kwake kochepera kuja siingathe kuona momwe iwe ungaonere, ndiye monga m’mene tagwirizanira kale kuti Mulungu safanana ndi china chilichonse, komanso kuti iye amatha chilichonse, choncho sizoyenera kumufunsa Mulungu ndikuthekera kwathu kochepaku zinthu zoti kwa iye ndizosakaikitsa, chifukwa kuthekera kwa

Mulungu ndi kwakukulu kwambiri kuposa kuthekera kwa zolengedwa zonse, chifukwa Mulungu akunena kuti: **“Kodi sukudziwa kuti Mulungu ngokhonza (ngokwanitsa) chinthu chilichonse”** (Surat AlBakara: 106).



Kodi Mulungu amawaonanso anthu ndimum’dimamomwe?

Tingathe kumupatsa mwana filimu kuti aonere makamaka mwa ma filimu omwe amaonetsa asilikali a pamtunda omwe amaona pogwiritsa ntchito ma galasi oyang’anira ukafika usiku, ndipo timuonetsenso ma filimu oonetsa zina mwa zinyama ndi mbalame zomwe zimaona usiku, komanso ena mwa ma filimu omwe amaonera ndi masewero omwe amasewera mumatha kupezeka zipangizo zojambulira monga (laser) zomwe zimaonetsa za kuseli kwa zinthu komanso zimationetsa zinthu zomwe zili mu mdima, pambuyo pake timuuzze mwanayo kuti: ukumuona munthu (cholengedwa) wofooka mmene akumakwanitsira kuona mu mdima nthawi zina? Kuli bwanji mbuye wathu amene anamulenga munthu ameneyu ndi zolengedwa zonse⁽¹³⁹⁾, ngati Mulungu anatipatsa kuthekera kopanga zachilendo zimenezi, kodi angalephere- iye amene ali wakutha ndi woyang’anira – kupanga zimenezo? Kumachita kuti ndi wakutha komanso wamkulu kwambiri, ndipo kuthekera kwa Mulungu palibe amene angakutchinge kapena kukulepheretsa.



KODI ALLAH AMAKWANITSA BWANJI KUTIONA TIKAKHALA MNYUMBA ZATHU, MAKOMO NDI MAWINDO ALI OTSEKEDWA?

Timuonetse mwana zithunzi zakuchipatala kenako timufotokozere kuti ndithu munthu yemwe Mulungu adamulenga adakwanitsa kuliona fupa litatsekedwa bwino bwino pogwiritsa ntchito chipangizo cha x-ray, kuli bwanji Mbuye wathu yemwe adalenga munthuyo? Ndithudi Mulungu amationa tikakhala m’manyumba mwathu titadzitsekera makomo onse, ndithu Mulungu safanana ndi chilichonse, iye salingati munthu yemwe zipupa zimamulepheretsa kuona, Mulengi sangakhale ngati cholengedwa; chifukwa Mulungu ndi wakutha chilichonse, ndipo ndizoyenera kulilumikiza yankho limeneli ndi zichito chito zamwanayo polimbikitsa mbali yakuzilondera ndikuchimva kukoma chipembedzo mu mtima mwake mwanayo⁽¹⁴⁰⁾.



KODI ALLAH AMADZIWA BWANJI NTCHITO ZATHU? NANGA AMAKWANITSA BWANJI KUYANG'ANIRA ANTHU ONSE?

Mwana akuyenera kudziwa nthawi zonse kuti Mulungu ali ndi mbiri zabwino ndizokwanira zokha zokha, adziwenso kuti kuthekera kwa Mulungu kulibe malire, iye ndi wakutha zedi, Mulungu akunena kuti: **“Kodi sukudziwa kuti Mulungu ngokhonza (ngokwanitsa) chinthu chilichonse?”** (Surat Al Bakara: 106), ndiye chifukwa chakuti Mulungu ali ndi kuthekera kwa kukulu palibe chimene chimamukanika padziko lapansi pano ndi kumwamba komwe, ndizosatheka kuyerekeza kuthekera kwa Mulungu ndi kuthekera kwa zolengedwa, kuthekera kwa zolengedwa ngakhale kungakule bwanji, kuthekera kwa Mulungu kudzakhala koposa kwambiri. Pofuna kuyandikitsa tanthauzo limeneli: nzotheka kumpatsa chitsanzo chazojambulira video (video camera) m'mene chimakwanilitsira kujambula ndikusunga kakang'ono ndikakakulu kena kalikonse komwe diso lake (camera) laona, ndipo Mulungu ali ndi kuthekera kwakukulu kwambiri koposa chilichonse, iye amatha kuyang'anira anthu onse nthawi imodzi, chifukwa kuthekera kwake kulibe malire, ndipo Mulungu amadziwa ndipo kudziwa kwake ndi kokwanira komanso kopanda malire pa china chilichonse ⁽¹⁴¹⁾.



Tithanso kumupatsa chitsanzo ichi: tiyerekeze kuti pali kampani yayikulu uku-funa uziyang'anira ogwira ntchito mmenemo, ndipo mwawayikira ma kamera iwo asakudziwa, ndipo mwayamba kuwayang'anira mwachinsinsi kudzera pa ma sikilini (screen/video monitor) oonetsa kalikonse kochitika pa kampaniyo nthawi imodzi, ngati kapolo kapena cholengedwa chofooka chomwe Mulungu adachilenga chikukwanitsa kupanga zimenezo, ndiye akalephere yemwe adalenga kapolo ameneyo ndicholengedwa chimenechi kuwaona akapolo ake onse nthawi imodzi?.

Kodi Nchifukwa chiyani munthu amamwalira ndipo Mulungu samwalira?

Ndithu infa ndi chikonzero cha Mulungu chomwe anakonzera zolengedwa zake Mulungu akunena kuti: **“Chamoyo chilichonse chidzalawa infa, kenako mudza bwezedwa kwa ife”**. (Al Akabut: 57), ndiye kufa kwa munthu ndichiyambi cha moyo uli nkudza, ndipo umenewo ndiwo moyo umene uli wofunikira kwambiri.

Ndithu infa ndi chizindikiro chosonyeza kufooka chomwe wamoyo wolengedwa aliyense chidzamupeze, ndiye kufooka sikumapezeka mwa mulungu, chifukwa Mulungu sadalengedwe ndipo sadzamwalira, pomwe munthu ndi wolengedwa ndipo amamwalira, ndithu umoyo wa Mulungu sufanana ndi umoyo waife, umoyo waife umatha ndi ifa, ndipo zolengedwa zonse zidzamwalira, adzatsale ndi Mulungu yekha, ndithu moyo wa Mulungu ndi wokwanira ndipo ukuyenera kukhala ndi mbiri zonse zakukwanira, makamaka mbiri yoti iye ndiwa moyo yemwe sadzafa⁽¹⁴²⁾.

KODI ALLAH AMANDIKONDA NGATI MMENE INE NDIMAMUKONDERA

Mulungu ndi wokhululuka ndi wachifundo amawakonda anthu abwino okhazikika ndi onena zoonza, Mulungu akunena kuti: **“Allah awakonda iwo, nawonso amukonda Allah yo”** (surat Al Maida: 54), ndipo zizindikiro zachikondi cha Mulungu pakapolo wake ndi izi:

Mulungu amawalemekeza iwo ndikuwachengetera, ndikuwayendetsera zichito chito zawo, kuwadyetsa ndi kuwakhululukira, ndipo aliynse amachikhudza chifundo cha Mulungu ndi ulemelero womwe Mulungu anamupatsa, ndipo Mulungu amamukonda kapolo wake yemwe amamumvera iye ndikudziyandikitsa kwa iye ndipo amagwiritsa ntchito mphamvu yake yonse kuonetsa chikondi kwa Mulungu; monga kusamala swala, kuchitila ubwino makolo, kupereka chaulere, kuchitira ubwino anthu, kunena zoon, kuwerenga Quru'an, kumutchulatchula Mulungu, ndi ntchito zina zabwino, yemwe angapange zimenezi Mulungu wapamwamba mwamba amamukonda⁽¹⁴³⁾.



MAFUNSO

OKHUDZA ANGELO



? Kodi Angelo ndi ndani? Nanga amaonekabwanji?

Iwo ndi zina mwa zolengedwa za Mulungu analengedwa kuchokera kudangalira (kuwala), Mulungu adawalenga iwo asadamulenge munthu. Iwo ali ndi chifuniro, nzeru ndi mapiko, ndipo maonekedwe a nkhope zawo ndi okongola, alinso ndikuthekera kodzisintha kuti aoneke ngati munthu, iwo samadya kapena kumwa, iwo ndi akapolo a Mulungu amapanga zomwe alamulidwa, iwo ali ndi maulemelero a pamwamba osiyanasiyana.

Ndipo wolemekezeka kwambiri mwaiwo ndi **Jibir** (as); iye ndi amene anapatsidwa ntchito yokafikitsa chivumbulutso (uthenga wa Mulungu) kwa atumiki.

Wina ndi Mikail; **Israfil** ndi ena otero, ena mwaiwo ndi amene anapatsidwa ntchito yosamalira akapolo a Mulungu nthawi ina iliyonse, ndipo pali chiwerengero chochulukuka cha angelo, mgelo wina aliyense ali ndi ntchito yakeyake yomwe Mulungu anamupatsa kuti azigwira⁽¹⁴⁴⁾.

? Kodi maina A Angelo ndi ati?

Ndithu angelo alipo ochuluka kwambiri, palibe amene amadziwa kuchuluka kwawo kupatula Mulungu (mwini ulemero wapamwamba), ena mwa maina awo ndi awa: Jibiril, Mikail, Israfiil, Ridhwani, Maliki (as), palinso omwe anyamula mpando wa Mulungu, ena otetezera akapolo a Mulungu, ndi ena omwe amasunga ntchito za akapolo a Mulungu, ndi ena otero⁽¹⁴⁵⁾.

? Chifukwa chiyani Mulungu analenga Angelo?

Mulungu analenga angelo kuti azigwira ntchito yabwino, iwo onse ndi abwino nthawi zonse, sapanga choipa ndipo sachidziwa. Angelo kwao kweni kweni ndi kumwamba, koma kutsika kwa munthu kubwera pansi pano kunapangitsa kuti angelo ena azitsikanso pansi pano kudzagwira ntchito zawo zina zomwe Mulungu wawalamula kuti adzagwire, monga kudzasamalira, ndikudzawatetezera ndi kuwayang'anira anthu, ndi kudzafikitsa uthenga kwa aneneri, ndikudzapulumutsa, ndikuwapemphelera chikhululuko anthu, kudzakhala nawo anthu pamalo pomwe akumutchula Mulungu ndi ntchito zina zotero.

Ndipo ndi zotheka kumuza mwana kuti angelo ali ndi ntchito ziwiri zikulu zikulu zofunikira kwambiri izi: kupembedza Mulungu ndikuyika ndondomeko yakayendetsedwe kadziko limeneli⁽¹⁴⁶⁾.



Kodi nchifukwa chiyani sitimawaona Angelo?

Anthu alibe kuthekera kowaona angelo mkaonekedwe kao komwe Mulungu adawalegera. Nchifukwa chake iwo amadzisintha namaoneka ngati munthu ndicholinga choti anthu athe kuwaona iwo kapena kugwira nawo ntchito, ngati m'mene Jibiril anadzisinthila naoneka ngati munthu wachimidzi midzi pa nkhani yophunzitsa malamulo achipembedzo ija⁽¹⁴⁷⁾.



Kodi ziwanda (majini) ndi chiyani?

Izi ndizina mwa zolengedwa za Mulungu, Mulungu adazilenga izi kuchokera kumoto, ndipo iwo analengedwera kuti azimvera malamulo a Mulungu ndikusiya zomwe waletsa, iwo amamwalira ngati m'mene zolengedwa zonse zimamwalilira, ife sitingakwanitse kuziona ndipo tilibe kuthekera kotero, Mulungu adawalengera iwo kuthekera kosiya ndi kuthekera kwa munthu, iwo amatha kuuluka ndi kuyenda mwachangu komanso amakwanitsa kudzisinthira maonekedwe (kusanduka)⁽¹⁴⁸⁾, ndipo kalengedwe kawo ndikosiyana ndi kamunthu, chifukwa munthu adalengedwa kuchokera kudothi pomwe ziwanda zinalengedwa kuchokera kumoto.



Kodi wamphamvu kwambiri ndi ndani pakati pa Angelo ndi Ziwanda?

Ndithu angelo kalengedwe kawo ndikopitilira samwalira kufikira tsiku lomwe lidzaimbidwe lipenga, pomwe ziwanda zimamwalira zisanafike tsiku limeneli. Kotero angelo ndi amene amachotsa mizimu kudzera muchilolezo cha Mulungu akagamula kuti wina wake amwalire **“Mulungu ndiyemwe amatenga mizimu pa nthawi ya ifa yake”**(surat zumar: 42)⁽¹⁴⁹⁾, choncho angelo ndi amphamvu kwam-biri kumbali imeneyi ndi paumoyo wadziko lapansiwu, ndipo satana ndi abale ake amaopa angelo, monga m'mene zinachitikira tsiku la nkondo ya Badri sa-tana ataona angelo omwe Mulungu adawatumiza kuti akawathandizire anthu okhulupilira, iye anawauza makafiri kuti: **“Ine ndikuzipatula mwainu, Ndithu ine ndikuona zomwe inu simukuziona, ndithu ine ndikuopa Mulungu, ndiponso Mulungu ngwaukali polanga”**(surat Al Anifaal:48).



Kodi Angelo amamwalira?

Nzoona kuti angelo ndi zina mwazolengedwa za Mulungu, ndipo chilichonse chidzaonongeka ndipo angelo adzamwalira kupatula Mulungu wapamwamba mwamba, chifukwa iye ndi wamoyo wampakana kalekale⁽¹⁵⁰⁾, Mulungu akune-na kuti: **“chinthu chilichonse chidzaonongeka kupatula nkhope yake (Mulungu-guyo)”**, {surat Al Qasas: 88}, ndiye zonse zili padziko lapansi pano zidzamwalira, chimodzi modzinso zonse zomwe zili kumwamba zidzamwalira kupatula omwe Mulungu adzawafune kuti nthawi imeneyo asamwalire, ndipo palibe yemwe adzatsale osamwalira kupatula Mulungu wapamwamba mwamba, chifukwa iye ndiwamoyo yemwe sadzamwalira mpaka kale kale (wamuyaya).

MAFUNSO

OKHUDZA MABUKU

Kodi mabuku akumwamba ndi ati?

Awa ndi mabuku omwe Mulungu adawavumbulutsa kwa atumiki ake (madalitso ndi mtendere a Mulungu zipite kwaiwo); ndi cholinga choti afalitse uthenga ndi kulamulira malamulo ali mmenemo, mabuku amenewa ndi chiongoko komansochifundo kwa zolengedwa zonse ndi cholinga choti zisangalale pa dziko lino lapansi ndi moyo womwe uli nkudza.

Ndipo zomwe tikudziwa zokhuda mabuku amenewa ndi zoti: Mulungu adavumbulutsa kwa mneneri Ibrahim (Abraham) (a.s.) buku lotchedwa (**Suhufu**), kwa Daud (Davide) **zaburi** (masalimo), kwa Musa (Mose) **Taurat** {chipangano cha kale}}, ndipo kwa Issa mwana wa mariam (Yesu) **Injeel** {chipangano chatsopano}}, ndipo kwa Muhammad (**Quru'an**)⁽¹⁵¹⁾.

KODI NCHIFUKWA CHIYANI TIMAFUNIKIRA QUR'AN? NANGA CHIFUKWA NINJI QUR'AN ILI CHOZIZWITSA CHA MUYAYA?

Ngati chipangizo chophweka chopangidwa ndi munthu chimafunikira ka buku kotidziwitsa mmene chipangizochi tingachigwiritsire nthito moyenera; ndiye kuti munthu – yemwe ndi chopangidwa (cholengedwa) ndi Mulungu- azafunikira kwambiri buku lomuungolera ndikumudziwitsa njira yachiongoko, kupambana ndi kulongosoka padziko la pansi ndi dziko lomwe lili nkudza, Mulungu akunena kuti: **“Kodi asadziwe yemwe adalenga (zinthu zomwe adalenga)? Kumachita kuti iye ngodziwa zinthu zing’onozing’ono kwambiri ndiponso wodziwa nkhani zonse”**. (surat Almulk: 14).

Komanso Quru'an ndi chodabwitsa; chifukwa mtumiki Muhammad (saw) ndi mneneri womaliza wa aneneri onse, choncho pakuyenera kuti chodabwitsa chake chikhale chopitilira mpaka kalekale, chifukwa palibeso mneneri wina pambuyo pake, ndiye pakuyenera kuti umboni ukhalepobe nthawi zonse, pakuyenera kuti tchalenji yake ikhalebe kufikira tsiku lachiweruzo.

Ndipo maumboni osonyeza kuzizwitsa kwa Qur'an ndi ochuluka zedi, ofunikira kwambiri mwaiwo ndi awa:

kuzizwitsa kwake pachilankhulo ndi kulongosoledwa bwino kwa mfundo zake, ndipo ichi ndichimene Mulungu anawatchalenja nacho aluya omwe anali otso-gola pakulongosola ndikumveka bwino mau polankhula, koma anthu ndi ziwana-

da zonse zinalephra kupeka mau angati a mu Qur'an imeneyi yolemekezekayi. Uwu ndi umboni woti Quru'an imeneyi inachokera kwa Mulugu⁽¹⁵²⁾.



Kodi chifukwa chiyani Mulungu sanawatetezenso mabuku akalewa?

Ndithu Mulungu wapamwamba mwamba amapanga zomwe akufuna, ndipo amakhala ndizolinga za nzeru zakuya, zina mwa izo timazidziwa ndipo zina sit-imazidziwa, koma maumboni omveka akuonetsa poyera kuti mabuku akalewo sadali chozizwitsa, choncho sichidali chofunika kuti apitilire, komanso iwo anali malamulo anthawi yochepa ndi kwa anthu ochepa⁽¹⁵³⁾.



Kodi ndi maumboni ati omwe akutsimikizira kuti Qur'an siidasinthidwe kalikonse?

Funso ngati ili nthawi zambiri omwe amakonda kufunsa ndiomwe ali a msinkhu woyambira pakatikati ndikumapita mtsogolo, kotero tidzayenera kumulongo-solera modekha ndi momuunikira mwanzeru zomwe zingatsindike kuti Qur'an ndi yoona, kenako timuuze kuti: ndithu zinthu zikanenedwa mobwerezabwereza ndikuchitika kambirimбири zimakhazikika ndipo zikafala zimatsimikizika, ndipo Qur'an inatipeza kudzera munjira yofala (yowanda), ndipo timulongosolere tanthaunzo lakufalako (التواتر) kuti ndikulandilidwa nkhani ndi gulu lochuluka kuchokeranso ku gulu lochuluka losatheka kumveka ndi bodza, adziwe zimenezo anthu wamba ngakhale anthu odzitsata, ndipo asilamu anatengera zolandila nkhani zimenezi m'bado kuchokera ku m'bado wina, amaphunzitsana Qur'an imeneyi mokhala mwawo, amaiwerenga m'mapemphero awo, ndipo amawaphunzitsanso ana awo, moti titati tiyerekeze kuti munthu wophunzira wamkulu ndi wolemekezeke kwambiri komanso woopsa atati alakwitse chilembo chamu Quru'an mo, ana adzamudzudzula iye akulu akulu asanamudzudzule, choncho kufikira inatipeza ife Quran imeneyi ilibe choonjezera kapena chopunguka, ili yotetezeke yosasindidwa.

Atati atsuste mwanayo umboni umenewu ndiye kuti adzathanso kutsutsa maumboni ena onse omwe ali okhazikika ndi oona, monga kupezeke kwa mtumiki, ophunzira amtumiki (maswahaba) ndi anthu ena odziwika mumbiri yachisilamu, zoterezi ngakhale anthu anzeru onse sangagwirizane nazo (zotsutsa umboni umenewuzi), ndipo mu Qur'an Mulungu adawatchalensa anthu ndi ziwanda kuti abweretse chofanana ndi Qur'an yo ndipo sanakwanitse, ndipo mu Qur'an yonse mulibemo kusemphana kapena kukhulana ngakhale kupelewerwa ndipo kudabwitsika kwa nkhani zake, malamulo ndi mau ake Zikusonyeza kuti ndithudi Qur'an yo sidachokere kwa munthu, chifukwa munthu ntchito zake komanso mau ake amasinthasinthwa komanso kupunguka; Qur'an yo inachokera kwa Mulungu ndipo iye anatenga yekha udindo woyiteteza⁽¹⁵⁴⁾.

MAFUNSO

OKHUDZA ATUMIKI

Kodi aneneri ndi atumiki ndi ndani?

Iwo ndi anthu ochokeranso mwa ana a Adam, Mulungu anavumbulutsa kwa iwo utumiki ndipo anawalamula kufalitsa uthenga wa Mulungu kwa anthu awo, ndikuwaitanira kuti adzimupembedza Mulungu yekha. Mneneri woyamba ndi Adam ndipo womaliza wawo ndi Muhammad (saw). Chiwerengero chawo ndi chochuluka kwambiri chifukwa Mulungu amawatumiza iwo ku mibadwo yonse yomwe idapezeka padziko lapansili, moti nyengo iliyonse mumbiri zakale imakhala ndi mneneri wowaitanira anthu ake ndikuwaongolera kunjira yoongoka.

Kodi chifukwa chiyani Mulungu adatumizaatumiki?

Mulungu adatumiza atumiki chifukwa cha chifundo chake pa anthu ndi kufuna kuwaongola, kuti (atumikiwo) afalitse kwa anthuwo uthenga wa mbuye wawo, ndiye mtumiki amakhala munthu yemwe anthu ake amamudziwitsitsa bwinobwino komanso yemwe iwo amaikira umboni za ubwino wake kuyambira asanalandire chibvumbulutso, ndipo Mulungu adawapanga atumiki kukhala chitsanzo chooneka ndi maso pa anthu, amawaphunzitsa iwo kudzera mmakhalidwe ndi zichitochito ndikumawalongosolera zomwe zingamawathandize ndikuwatalikitsira zomwe zingawazunze, moti kutumiza atumiki kunali kuika umboni pazolengedwa zake ndikuwasonkhanitsa anthu pachipembedzo chimodzi chomupembedza Mulungu yekha⁽¹⁵⁵⁾, chifukwa anthu akufunikira wowaongolera kunjira yoona muchilankhulo chawo, pachifukwa ichi Mulungu amavumbulutsa kwa atumiki amenewa mabuku muchiyankhulo cha anthu awo ndicholinga choti uthengawo uwapeze momveka bwino kwambiri.

Kodi aneneriwa samalakwitsa (anali otetezeka ku machimo)?

Anenerinso ndi anthu mwaiwo mulinso matanthauzo aumunthu, Mulungu anawateteza iwo kumbali ya utumiki yokhayo, anawateteza kuti asagwere mu zomwe zingadetse zochita zawo kapena makhalidwe awo, ndicholinga choti akakhale chitsanzo chabwino, anthunso azikhutitsidwa ndi mau komanso zochita zawo, ndinso kuti chisakhale chifukwa chodetsera ntchito yawo yakufalitsa uthenga wa Mulungu, koma ngakhale zili choncho iwo ndi anthunso amatha kulakwitsa kwa wamba kosapereka vuto kuutumiki wawo, monga: kulakwitsa kuyeza malo oyenera kulima kapena a nkondo, kapena mulingo wachidwi choyitanira anthu kuchipembedzo⁽¹⁵⁶⁾.



Kodi Muhammad ndi ndani?

Iye ndi mneneri womaliza mwa aneneri omwe Mulungu anawatumiza kwa akapolo ake, ndipo dzina lake ndi Muhammad mwana wa Abdullah mwana wa Abdul-muttalib wochokera mwa Hashim wafuko la chiquraish, anabadwira ku makkah, tsiku lolemba mwezi wa Rabiul-awwal, chaka cha Njovu, bambo ake anamwalira iye ali m'mimba mwa mayi ake, mayi ake adamwalira iye ali ndi zaka zisanu ndi chimodzi (6) zakubadwa, kenako analeredwa ndi agogo ake Abdul-muttalib omwe anadzamwalira mtumiki ali ndi zaka zisanu ndi zitatu (8), kenako anamulera iye amalume ake (bambo ake ang'ono) Abu Taalib, mtumikiyu ankatchedwa “wonena zoonawokhulupilika” chifukwa chakhalidwe lake lapa mwamba, analandira utumiki ali ndi zaka makumi anayi, anakhala akuitanira anthu ake kuchisilamu ku Makkah kwa zaka khumi ndi zitatu (13), kenako anthu aja atamuzunza kwambiri iye anasamukira ku Madina nakakhazikika kumeneko kwazaka khumi, analumikiza kumeneko ubale pakati pa asilamu ochokera ku Makkah ndi aku Madinako, Ndipo anakhazikitsa kumeneko malamulo a Mulungu, ndipo adamwalira kumeneko muchaka cha khumi ndi chimodzi chisamukireni kuchokera kuMakkah, komanso pambuyo pofalitsa uthenga wa Mulungu mokwanira ndikubweza kwa anuwake zonse zomwe anasungitsidwa⁽¹⁵⁷⁾.



Kodi nchiyani chomwe chingatsimikizire zoti mtumiki Muhammad amanena zoonawokhazokha?

Maumboni osonyeza kuti Muhammad ndi mtumiki ndi ambirimbiri, ndipo ofunikira kwambiri mwa iwo ndi: Quran yolemekezeka, buku limeneli ndi lozizwitsa zedi ndipo lakhala likudabwitsa mibado pambuyo pa mibado chifukwa cha nfun-do za pamwamba zomwe zimagwedeza nzeru za anthu.

Chinanso chimene chimasonyeza za utumiki wake (SAW) ndi mbiri ya khalidwe lake yomwe adamusimba nayo adani ake asanamusimbe nayo omukonda ake, moti ankamutcha kuti “wonena zoonawokhulupirika”.

Umboni winanso ndi zozizwitsa zomwe aliyense amazidziwa zomwe anthu a nthawi yake adazona, ndipo mibado ya m'mbuyo idamva kuchokera ku mibado ya kale.

Umboninso wina ndi malamulo ogwira mtima, ogwirana bwino, okoma komanso okwanira omwe ali mu chipembedzo cha chisilamu.

Umboni wina ndi nkhani zabwino zoloseza za kubwera kwa iyezochuluka zomwe zikupezeka mmabuku akale.

Enanso mwa maumboniwa ndi kufalikira kosalekeza kwa chipembedzo cha chisilamu kumeneku pa malo aliwonse ndi nthawi zonse.

Ndipo umboni wina ndikufotokoza kwake mtumikiyu zokhudza mibado yakale ndi zinthu za mtsogolo⁽¹⁵⁸⁾.



KODI ZINATHEKA BWANJI MTUMIKI KUYENDETSEDWA KUPITA KU JERUSALEM NAKAKWEZEDWA KUPITA KUMWAMBA MPAKA KUBWERERA USIKU umodzi WOMWEWO?

Ndithu mtumiki (SAW) anayendesedwa kuchokera ku makkah kukafika ku mzikiti wa ku Jerusalem pa Buraq (chinyama chokwera), kenako anakakwezedwa kupita ku mwamba motsogozedwa ndi Jibril (Gabriel), ndipo Mulungu ndi waku-tha chilichonse, palibe chomwe chingamukanike pansi pano ngakhalenso kumwamba, monga mmene tikuonera lero: amakwanitsa bwangi munthu wofooka kugwiritsa ntchito nzeru zake kupanga ndege yoyenda mwachangu kuposa mau, komanso anapanga chipangizo chojambulira zithunzizomwe zimampangitsa munthu kumaoneka wochuluka ndi malo angapo nthawi imodzi, ndiye Mulungu ndi wamkulu kwambiri yemwe ali ndi kuthekera kwakukulu kuposa zolengedwa zake.



Kodi nchifukwa ninji Muhammad anali mneneri womaliza?

Ndithu kutumizidwa kwa aneneri kumalumikizana ndi cholinga- kumene kuli kuongola ndi kuongolera- ndipo kukupezeka kuti mabuku akale anakumana ndi kusintha ndi kupunguka (ma chapter ndi ma verse ena) pambuyo pomwalira atumiki awo. Mulungu anachiona kuti ndi chanzeru zakuya kuti atumize mneneri ndi buku lomwe silingakumane ndi m'pungwepungwe ngati umenewu (kusintha ndi kupunguka), ndipo Mulungu anatenga udindo woliteteza kufikira tsiku lomaliza, ndipo poona kudabwitsa kwa Qur'an koti ilo ndi buku lomveka bwino lokhala ndi maumboni opambana pa zolengedwa zonse- mpaka kale kale, chinali chanzeru kuti mtumiki Muhammad (saw) akhale womaliza mwa aneneri ndi atumiki.



Kodi nchifukwa chiyani kuli koyenera kuti tizimukonda mtumiki (saw)?

Chifukwa chakuti kumukonda iye ndi imodzi mwa nsanamira zachikhulupiliro, ndipo kukhulupilira mwa Mulungu sikungakhale kokwanira pokha pokha chikon-di ichi chitapezeka, ndipo kumukonda Mulungu kumalumikizana ndi kumukonda

mtumiki wake (saw), komanso kuti Mulungu adamusankha iye pakati pa anthu onse kuti agwire ntchito yaikulu kwambiri ya utumiki imeneyi, chifukwa Mulungu anasankha munthu yemwe ali ndi khalidwe, mau ndi ntchito zabwino kwambiri komanso wochokera ku banja labwino kwambiri, chifukwa iye (Allah) ndi amene amamudziwa bwino munthu woyenera kumpatsa utumiki umenewu, ndipo poona kuti Mulungu ndi amene adamusankha iye pakati pa anthu onse pompatsa udindo waukulu umeneu.

Ndithu ndizoyenera kwa ife kumukonda kwambiri iyeyo kuposa munthu wina aliyense; chifukwa iye ndi amene anawadziwitsa za mbuye wawo, ndipo anali mneneri wabwino kwambiri kwa anthu ake, palibe mwazolengedwa ndi m'modzi yemwe amene anatipangira zabwino zapamwamba woposa iye (saw)⁽¹⁵⁹⁾, iye adapilira ndi mazunzo omwe amapezana nawo pa nthawi yoitanira anthu kuchipembedzo ndi ubwino, moti amabanika ndi kudandaula akamapanda kukhulupilira yemwe iye akumuitanirayo; chifukwa chowadandaulira zokulowa kumoto, Mulungu akunena kuti: “Mwina uziononga wekha pakuwadandaulira (anthuwo) chikhalidwe chawo kuti sakukhulupilira nkhani iyi, (Iyayi usakhale woadandaula ndi zimenezo)” (Surat Al kahaf: 6). Pachifukwa chimenechi mtumiki (saw) ndi amene ali woyenera kumukondetsetsa pambuyo pa Mulungu.



MAFUNSO OKHUDZA KUKHULUPILIRA TSIKU LOMALIZA



? Kodi tsiku lomaliza ndi liti?

Ilo ndi tsiku lomwe Mulungu adzaukitse zolengedwa zonse kuti akaziwerengere ntchito zake, ndipo limatchedwa lomaliza chifukwa palibenso tsiku lina pam-buyo pake, ndipo limatchedwanso kuti ndi tsiku lamalipiro chifukwa Mulungu akawalipira anthu patsiku limeneli pa zintchito zomwe adatsogoza ali padziko lapansi lino, kotero yemwe angagwire ntchito yabwino kapena yomvera Mulun-gu ndiye kuti Mulungu akamulowetsa iye ku Jannah, ndipo yemwe angagwire ntchito zoipa nanyozera malamulo a Mulungu; Mulungu akamulowetsa iye ku moto, ndipo ili ndi tsiku lomwe lidzakhale lomaliza paumoyo wa padziko lapansi ndi kwa anthu onse. Tsikuli limatchedwanso kuti louka, kutanthauza kuti: patsiku limeneli anthu adzauka m'manda kulunjika kumwamba kuti akawerengeredwe ntchito zawo⁽¹⁶⁰⁾.

? Kodi tsiku loukali lidzabwera liti? Nanga nchifukwa chiyani Mu-lungu anatibisira tsiku limeneri?

Palibe amene akudziwa kuti tsikuli lidzabwera liti, Mulungu akunena kuti: **“Iwe (ntchito yako) ndikuwachenjeza amene akuopa; (osati kulengeza za nthawi)”** (Surat Annazi’ati: 45), Mulungu anatibisira tsiku limeneli ndi cholinga choti til-imbikire kugwira ntchito ndikukhala okonzekera tsiku lililonse, pogwira ntchito zabwino ndi kusiya ntchito zoipa; ndipo munthu akanadziwa tsiku limeneri lob-welera kwambuye wake sakanalapa kufikira nthawi itasala yochepa, ndipo dziko likanadzadza ndi zoipa kuposa m’mene liliri panopa⁽¹⁶¹⁾.



Kodi kuwerengetseredwa ndiko kutani?

Uku ndi kusunghanitsa komwe Mulungu adzasonkhanitse anthu onse oyambilira mpakana omalizira, Mulungu akunena kuti: **“Nena kwa iwo (poyankha kutsutsa kwawo) kuti ndithu, amibadwo yoyamba ndi yomaliza omwe inu muli m’gulu lawo adzasonkhanitsidwa m’nthawi ya tsiku lomwe lakhazikitsidwa”** (Surat Al Waqi’ah: 49-50), nawaonetsa ntchito zawo ndikuwalipira molingana ndi momwe anagwilira ntchitozo, munthu yemwe angagwire ntchito yabwino akalipidwanso zabwino, ndipo yemwe angagwire ntchito yoipa adzalipidwanso zoipa, Mulungu akunena kuti: “Choncho amene angachite chabwino cholemera ngati kanjere kakang’ono azaona malipiro ake, ndipo amene angachite choipa cholemera ngati kanjere kakang’ono, azaona malipiro ake” (Surat Azilizaal: 7-8).



Kodi infa ndi chiyani?

Ndithu mwana wazaka zisanu ndi chimodzi ndikumatsika – nthawi zambiri- sangathe kumvetsa tanthauzo leni leni lainfa ndi kuuka kwa akufa. Komano zoona zake ndizoti infa ndi mathero eni eni amunthu wina aliyense pa umoyo uno, pomwe mwana wazaka zisanu ndi chimodzi kufikira wazaka zisanu ndi zitatu angathe kumvetsa nthawi zambiri- tanthauzo lainfa komanso zoti idzakhudza anthu onse, ndipo mwana woyambira zaka zisanu ndi zitatu kufikira zaka khumi; angathe kumvetsa mokwanira nkhani ya ifa ndikuuka kwa akufa, amatha kuona kapena kumva nthawi zina amatha kudutsana ndi nyengo ya infa m’banja mwake, nakhala kuti kumemeko ndikukumana kwake koyamba ndi infa, koma sitikudziwa m’mene angadzamvere kapena adzakhuzidwire akadzamva za infa ndi manda, zachidziwikire adzadzadzidwa ndi mantha chifukwa chakutchulidwa zinthu zimemezi; choncho tikuyenra kumulongosolera mwana za infa mosamunamiza komanso mogwira mtima mpaka akhutitsidwe kuti munthu womwalira amakhala kuti, ali paulendo- mwachitsanzo- munjira imeneyi mwana adzadziwa zenizeni kuchokera kwa anthu ena mwachangu. Ndipo ndi bwino- mwana asanakumane ndi banja lomwe lili munyengo ya infa timudziwitse kapena timuonetse mbalame yakufa kapena mtengo wakufa, chifukwa zimenezi zidzamuwalit-sira tanthaunzo la ifa mwa njira yokhudzika, kenako tiyetsetse kumulongosolera mwanayo mwachidule kuti ndithu munthu akamwalira amapita kukakhala mu umoyo wina, ndipo tonse tidzamwalira ndipo tidzakakumana ndi onse omwe adamwalira ndi kukhala nawo ku mtendere Mulungu akadzalora. Ndipo ndizofunika kuti mwana adziwe kuti ndithu infa simathero amunthu ayi, koma kuti ndi kusuntha kuchoka kwa munthu wokhulupilira kunka ku umoyo wabwino ndiwapamwamba kwambiri, komanso kusuntha kwa munthu woipa kukakumana ndi malipiro azoipa, ndipo Mulungu akamatenga moyo wathu (kutipha) sizimatanthauza kuti Mulungu samatikonda ayi, koma amatenga moyo umeneu ndicholinga choti tikakhale naye pafupi m’minda yapamwamba komanso yokongola kwambiri yomwe kukongola kwake sitingathe kukuyerekeza⁽¹⁶²⁾.

Kodi chifukwa ninji ana ena amamwaliranso?

